

CHIVUMBULUTSO

CHA YESU KHRISTU



Zikomo inu, mochuluka kwambiri, M'bale Neville.

Mukhoza kukhala pansi.

² Ine ndikukhulupirira zinanenedwapo kamodzi, kuti, “ine ndinali wokondwa pamene iwo ananena kwa ine, “Tiyeni ife tipite ku nyumba ya Ambuye.””

³ Tsopano, ife tikupepesa kuti ife tiribe chipinda, kapena chipinda chokhalamo, kwa iwo onse amene ali pano, ndipo mwinamwake ife tizichuluka tikamadutsa msabata ikubwerayi, anthu obwera muno, akamamva za msonkhano.

⁴ Koma cholinga cha nthawi ya padera iyi chinali kuti ife tidzakhoze...Pa mtima wanga Mzimu Woyera unali utaika chenjezo la kukhudzika uku, kuti, “Mpingo mu tsiku lino ukuyenera kukhala ndi Uthenga uwu.” Chifukwa, ine ndikukhulupirira kuti iwo ndi Uthenga wopambana kwambiri wa Baibulo, chifukwa iwo ukumuwlula Khristu mu Mpingo Wake pa nthawi ino.

⁵ Ndiye, palibe mmodzi aliyense angakhale ndi chikhulupiriro kapena kudziwa chimene iwo akuchita, kapena kumene iwo akupita, pokhapokhapo iwo atakhala ndi china, chinachake choti akhazikitsepo malingaliro awo ndi chikhulupiriro. Chotero, ngati Lemba lawulula Khristu kwa ife mmasiku otsiriza ano, ndi chikhalidwe cha nthawiyi, izo zikanatichitira ife ubwino kuti—kuti tiwafufuze Iwo ndikukapeza pamene ife tiri.

⁶ Tsopano, ndife—ndife opepesa kuti tchalitchi chathu si chachikulu, tsikulina ife tikuyembekeza kudzakhala nacho icho.

⁷ Ndipo masiku anayi otsiriza awa, makamaka, kuphunzitsa izi pa gawo la mbiriyakale ya—ya Bukhu la Chivumbulutso, Ine ndalowapo mu zinthu zimene ine sindinaganizirepo kuti zinachitikadi. Ndipo izo mpaka zabweretsa kwa ine ku—kumverera kwakuti, ikatha *Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo* iyi, ine ndinadutsapo mu zimenezo, Ine ndikufuna ndidzakhale ndi mndandanda wina wotero wobweretsa “a—Mpingo woona ndi mpingo wabodza,” pamodzi, ndipo kudzangodutsa mu mbiriyakale ndi Lemba. Monga nthawi imodzi ine ndinayesetsa, pa ulaliki, kuti nditenge “Mpesa woona ndi mpesa wabodza,” zopezeka mu Baibulo. Ndipo ife tiri . . .

⁸ Ife tidzayesa kuti tidzatenge mipando ina, pamene ine ndikuganiza za anthu kuyesetsa kuti adzakhale pansi. Ndipo

ife tidzatenga, tidzayesetsa kuti tidzatenge, mipando ina yowonjezera, kuti tidzayesere kudzazitsa zipinda kumbuyo kuno, ndi panja, ndi ina yowonjezera mozungulira, kuchitira kuti tidzathe kukhazika anthu ena ochulukirapo nthawi ya misonkhano.

⁹ Tsopano, pa izi, ine ndikanafunsa mmodzi aliyense wa inu amene mukukhudzika kwambiri ndi zinthu izi, mu—muzibwera nthawi iliyonse imene ife tizikhala ti—tikufotokoza Zimenezo. Ndipo ine sindingachite, kapena kuti ndinachita kuganzira ndekha...[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. ... kuchita...[Malo opanda kanthu pa tepi.]...Bukhu lalikulu ili la Chivumbulutso cha...[Malo opanda kanthu pa tepi.]... Mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo. Koma ine ndikudalira mwaulemu pa Mulungu, kuti—kuti awulule izo kwa ine basi pamene ine ndizibwera kwa izo.

¹⁰ Mbiriyakale ya chirengedwe, imene ili ya...yotengedwa kuchokera ku mbiriyakale yodziwika imene ine ndikuidziwa. Ine ndiri nazo mu chipinda changa chowerengera, pakali pano, pafupifupi olemba ndemanga faivi kapena sikisi, La Hislop *Two Babylons*, *Foxe's Book Of The Martyrs*, ndi mabuku ena opambana; monga la Pre-Nicene Council, pafupifupi mabuku foro pa zimenezo, pafupifupi masamba foro handiredi mu bukhu lililonse. Ndipo pamenepo a Nicene Council, ndi mbiriyakale yonse imene ife tingathe. Chifukwa, kuseri kwa izi, kuchokera pa tepi ya maginito, ife tilemba ndemanga pa Mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mpingo, kuti tidzazitumize ku dziko lonse, kumene ife tingathe, chifukwa ife tiri mmasiku otsiriza. Ife tiri kumathero a nthawi.

¹¹ Izo sizinafike pa mtima wanga mochuluka mpaka chi—chisankho chotsirizachi, ndiyeno ine ndikuwona pamene ife tiri. Kenako Mzimu Woyera unayamba kuwulula kwa ine, kuti—kuti ndiwachenjeze anthu, ndikuziika izi. Ndipo ine sindingathe kuchita izo mu—mtchalitchi ngati ichi, mokwanira. Ndiyeno ngati ine nditakhala pansu ndipo nkungolemba bukhu... Ine ndikumverera kuti ngati ine nditafika pa guwa, ndipo kudzodza kwa Mzimu Woyera pakati pa Akhristu kutabwera pa ine, kudzandithandiza ine, ndiye ine ndikhoza kudzakhala wokwanira mochuluka kulemba bukhu pamene, ine nditatha kudzazichotsa izo pa tepi, chifukwa pamenepo ife tikhoza kudzakhala ndi kudzoza kwa izo. Mabukhu, ndithudi, akhala ngati awongoledwapo pang'ono, chifukwa, pano, ife timaikamo zinthu zimene ife sitingathe kuziika mu bukhu. Ndiyeno ife...Ndipo ife timatenga nthawi yochuluka pa kudzibwereza tokha, kapena ine ndimatero. Ndiyeno, mu bukhu, izo zonse zidzawongoledwamo. Koma ife tidzayesera kuzitunga zonsezo, mochuluka mmene ife tingathere, pa matepi.

¹² Tsopano, matepi, usiku uliwonse, mabukhu ndi zina zotero, anyamata akhala nazo izo kunja kwa nyumbayi uko.

13 Tsopano, ine mwinamwake sinditha usiku uliwonse, monga mmene tadzitengera pa ifeeni kuti tiyesere kwa ulemelero wa Mulungu, kuti—kuti tibweretse Mauthenga asanu ndi awiri a mpingo awa, kapena Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo, mu mausiku asanu ndi awiri; kutenga usiku uliwonse, m'badwo. Monga, Lolemba usiku, Efeso; Lachiwiri usiku, Smurna; Lachitatu usiku, Pergamo; Lachinai usiku, Tiyatira; Lachisanu usiku, Sarde; ndi Loweluka usiku, Filadefia; ndipo Lamlungu mmawa ndi Lamlungu usiku, Laodikaya, m'badwo wa mpingo umene ife tikukhalamo. Kupereka mbiriyakale ya mpingo wapachiyambi, ndi a—ndi olemba ndi azambiriyakale, ndi angelo a m'badwo umenewo, ndi—ndi mauthenga, ndi mmene mpingo umayendetsedwera, pamene iwo ukuyenda kutsikira kudutsa kufika nthawi ino.

14 Ndipo ndi zodabwitsa kuwona momwe choneneratu chirichonse cha Lemba limenelo chimafika mokhazikika ndi mbiriyakale, ndendende basi, ku lingaliro la izo. Izo mpakana zinandidabwitsa ine kwambiri, kufikira, dzulo, ine ndinali nditawerenga kufikira kuti ndinamverera ngati maso anga atupa. Ndipo ine ndinadzatuluka ndipo ndinati kwa mkazanga, “Ine sindinayambe ndalotapo za izo kukhala mwanjira imeneyo.” Mukuona? Momwe izo zinali zopambana!

15 Ndipo tsopano, nthawi ina, ine mwinamwake sindingakhoze kumalizitsa izo mu usiku umodzi, mpingo, uthenga kwa mpingo. Ndipo ngati ine sindingakhoze kumalizitsa izo, usiku, ndiye mmawa wotsatira pa teni koloko. Zizilengezedwa usiku uliwonse, kwa iwo amene akufuna kuti abwere ndi kudzamvetsera pa zonse za izo, chifukwa ife tikufuna, tiyesetse, kuziika izo pa tepi. Ine ndizikhala ndi misonkhano ndiye kuyambira teni koloko, mmawa, kupitirira mpaka masana, mu nthawi yamasana, kuyesetsa kuti tizitulutse izo, uthenga wonsewo, chifuwa iwo akhoza kudzazigwira izo pa tepi. Osati . . .

16 Ife talengeza kuti sipakhala misonkhano iliyonse ya machiritso, chifukwa ife tikuyesetsa kuti tizisunge pansu pa kuyankhula kwa uneneri wa Baibulo. Ndiye, ife tinali ndi msonkhano wamachiritso posachedwapa muno. Ndiye ikangotha misonkhano imeneyi, ndiye ife tidzakhala ndi msonkhano wa machiritso kenanso kubwerera pa malo ano.

17 Koma tsopano ine—ine ndikufuna kuti ndizipange izi momveka kwenikweni, kuti aliyense azikhoza kukumbukira, kuti tsopano, muno, izo zikhoza kudula ndi kukoka, ndi kutipatsa ife tonse kugwedeza konse kwakukulu. Koma ine ndiri ndi udindo, osati wa—wa chirichonse koma kulalikirira Mawu. Izo, ndizo zonse. Basi—basi kumangogwiritsitsa ku Mawu. Ndipo nthawi zambiri izo zikhoza, mu mibadwo ya mpingo imeneyi, zikhoza kuwonsetsera pa chipambedzo cha winawake. Ndipo ngati izo zingachite zimenezo, izo sizinakonzedwe kuti

zikhale mwa nkhanza. Izo—izo zikungonena chimene Lemba lanena, ndi vumbulutso limene ine ndiri nalo la Ilo. Ndipo ngati inu mutaganiza kuti ine ndikulakwitsa mu zimenezo, ndiye musandiyimbe ine mlandu, mudzangondipempherera ine kuti Mulungu andiwonetsere ine chimene chiri cholondola, pakuti ine ndithudi ndikufuna kukhala wolondola.

¹⁸ Ndiyeno chinthu china, pozindikira kuti udindo umene ine ndiri nawo, mu—mu msonkhano wonga ngati uno, kuti kuwaphunzitsa anthu, kuti Mzimu Woyera udzandipanga ine kuti ndidzayankhire chifukwa cha mawu amene ine ndingayankhule pa guwa pano. Chotero inu mukuwona momwe tikufikira pa izo mwaulemu. Tsopano, wathu . . .

¹⁹ Ine ndikanakhala ndi izi kunja kwinkwike. Koma, pokhala kuti ndi kuphunzitsa, ndiye mwathu . . . Kunja mu misonkhano ya uvangeli, aliyense wa ife amakhala nalo lingaliro kapena—kapena kuzindikira za mumtima, kapena monga mmene zakhala zikukhalira kudutsa m’badwo, ndipo ife tiri nawo matchalitchi athu athu, ndi zimene matchalitchi athu amatiphunzitsa ife, ndi zimene ife timakhulupirira. Ife . . . Ine sindimakonda kupita mu tchalitchi cha munthu wina, kapena pakati pa anthu monga chomwecho, ndi kukanena chinachake chosiyana ndi chimene anthu aphunzitsidwa. Pakuti, kuwonjezera apo, ine ndayetsetsa momveka bwino kupanga maneno anga kuti . . .

²⁰ Ngati munthu ali Mkatolika, ndipo iye akudalira pa Mpingo wa Katolika kuti ndicho chipulumutso, iye wataika. Ngati iye ali wa Baptisti, akamadallira pa Mpingo wa Baptisti, iye wataika. Kapena wa Pentekoste, akamadallira pa Mpingo wa Pentekoste kuti udzamupulumutsa iye, iye wataika. Koma . . . mpingo uliwonse! Koma ngati munthu ameneyo akudalira mwaulemu pa chikhulupiroro mu ntchito yomalizika ya Khristu pa Kalvare, iye wapulumutsidwa, ine sindikusamala kuti iye ndi wa mpingo wuti. Chifukwa, “Mwa chikhulupiroro inu munapululumutsidwa, ndipo ndizo mwa chisomo.”

²¹ Tsopano, nthawizina, pochita izi, ndiye ine ndikuganiza, mu chipinda changa chomwe chaching’ono ichi chimene ife tinachiyamba zaka zambiri zapitazo, chongokhala ndi kamulu kakale ka mabuloko a konkire ndi zinthu, ndipo ali ngati malo opatulika kwa ife. Ife timadana nazo izo, basi timadana nazo kuziwona izo zikusinthidwa, mwanjira ina, chifukwa pano ndi pamene Mulungu koyamba anayamba kukumana ndi ife, pamene ife tinalibe ngakhale simenti pansu mmenemo. Koma icho—icho chafika pamalo tsopano kuti icho chikukulamba, ndipo ife tiri mkumanga—dongosolo la kumanga pano, kuti tiwadzadzitse malo ano ndi tchalitchi.

²² Tsopano, kufikira nthawi imeneyo, ine ndikumverera kuti pamene ine ndidzabwerera kuchokera ku munda, kumene ine sindikawavulazako abale ndi, kapena, mauthenga ndi zina

zotero, ndiye izo zimandipatsa ine ufulu wofotokoza maganizo anga omwe, kuchokera—kuchokera panga . . . kuchokera pa guwa pano. Ndipo chotero inu mukamati, “Ine ndaphunzitsidwa mosiyanapo pang’ono,” Ine ndingati. . . Ndiyeno, mu izi, ife timangoitana aliyense yemwe akufuna kuti abwere. Mukuona? Palibe aliyense amene akuthandizira izi, kapena chirichonse. Ndi kachisi pano. Ndipo aliyense amene akufuna kuti abwere, ndi wolandiridwa basi kuti abwere. Azingobwera basi. Chotero ine ndikukuitanirani inu kuti muzibweretsa Baibulo lanu, msonkhano uliwonse, ndipo muzibweretsa pensulo ndi pepala.

²³ Ndipo tsopano, ndi zolembedwa zonse ndi zina zotero, ine sindikanakhoza kubweretsa mabukhu onse. Chotero ine ndangolemba, ndimalemba, nthawi iliyonse, pa pepala apa, zolemba zapang’ono kuchokera mu mbiriyakale ndi ndemanga, ndi zina zotero, kuti ndidzakhoze kungowerenga izo kuchokera ku—ku zolemba pano, mmalo mokhala ndi bukhu ndikumatembenusa kudutsa masamba. Komabe, pamene izo zibwera ku Lembu, ife tizigwiritsa ntchito Baibulo. Ndipo kenako mu ndemanga, ine ndizizifotokoza; kapena mbiriyakale, yemwe wazambiriyakaleyo anali amene ananena izo, ndi zina zotero. Ndiye mu. . . Ndithudi, mu nkhani ya bukhu likubwerali, bwanji, ndiye ife tikhoza kudzazilemba izo bwino bwino pamenepo, ndipo tikhoza kudzakhala ndi chirichonse chitachitika bwino bwino.

²⁴ Tsopano, ife tichita chirichonse chimene ife tingathe kuti tiziyamba mofulumirirapo ndi kumatuluka mofulumira mmene tingathere. Iyo ikhala misonkhano ya, masiku eyiti, Lamlungu mpaka Lamlungu.

²⁵ Mmawa uno ine ndikuyamba ndi mutu wa 1 wa Chivumbulutso, wa Bukhu la Chivumbulutso. Ndipo Chivumbulutso chinaikidwa mu magawo atatu. Ndipo mitu yoyamba itatu ndi yomwe ife tikhale tikuchita nayo masiku eyiti amenewa. Pamene, m’badwo wa mpingo umodzi ukhoza kutitengera ife mwezi. Koma ife tikungoyenera kuti tizigunda malo ofunikirawo, monga mmene ife timanenera izo. Ndiye pamene inu mudzapeza bukhu, ilo lidzalembedwa, mwatsatane tsatane.

²⁶ Tsopano, Chivumbulutso, mitu itatu yoyamba, ikuchita ndi Mpingo, kenako Mpingo ukudzasowapo. Ife sitikuwuwonanso Iwo mpaka pamapeto a nthawi. Kuyambira Chivumbulutso 1 mpaka 3, ndi Mpingo; Chivumbulutso 4 mpaka 19, ndi Israeli, fuko; ndipo 19 mpaka 22, ndi zonse ziwiri, pamodzi. Ndipo miliri ndi mächenjezo, ndi zina zotero, kumapeto! Zaikidwa mzigawo zitatu. Mukuona? Ndipo ife tikutenga mitu itatu yoyambirira, yokhudzana ndi Mpingo, ndi m’badwo wa mpingo umene ife tikukhalamo.

²⁷ Tsopano, poyamba, izo zikhoza kuwoneka ngati zowuma chifukwa ife tikuyenera kuti tibwerere mmbuyo ndi kukapanga maziko. Ine ndinapemphera ndi kuwerenga, ndipo ndinachita chirichonse chimene ine ndikanatha, kuti ndiyesere ku—kuti ndipeze kumverera kwa Mzimu Woyera, momwe ndingaziyikire izi, kuti anthu athe kuziwona izo, ndipo kuti inu mudzakhoze, powona izi, mudzawunikiridwe ndipo zidzakupangitseni inu kubwera pafupi ndi Khristu, pakuti ife tiri kumapeto a nthawi.

²⁸ Ndipo ndicho chinthu chopambana chotero, monga ine ndakhala ndikuwerenga za mbiriyakale, kuti ndipeze momwe mpingo umenewo unayambira, ndipo mmene iwo unadzachokera, ndi zimene zinadzachitika, ndipo kuiwona Mbewu yaing’ono ya Mulungu ija ikuyenda kudutsa umodzi uliwonse wa mibadwo imeneyo; kuchokapo kwathunthu, pafupifupi, mu malo amodzi.

²⁹ Tsopano, mawa usiku, ife tidzayambira, ndipo tidzakhala ndi—tidzakhala ndi—chojambula apa; osati chojambula, koma bulakibodi, limene ine ndikufuna kuti ndizidzaphunzitsa izo kuchokera pa bulakibodi. Ine ndikukhulupirira mphunzitsi wa Sande sukulu, mmodzi wa iwo, ali ndi bulakibodi. Ine ndikuliwona ilo kumbuyo. Ine ndiwauza oyang’anira pano kuti alibweretse ilo kuno, adzaliike ilo kutsogolo kuno, kuti ine ndiphunzitsire kuchokera pa bulakibodi limenelo, ndi kudzazilemba izo kuchitira kuti mudzakhale otsimikiza. Ndipo inu mukhoza kudzajambula izo pa pepala lanu, ndi zina zotero, ndi kudzazitenga izo moyandikira momwe ife tingakhoze kudzazibweretsa izo.

³⁰ Koma ine ndikufuna ndingonena izi ndisanayambe: Kuwona chiyambi cha m’badwo wa mpingo, ndi kuwona mmene atumwi, ziphunzitsa, ndi zinthu zimene iwo ankaphunzitsa, ndi mfundo za Baibulo; ndipo kenako nkudzawuwona mpingo umenewo, pafupifupi gulu lachiwiri la atumwi, mmene iwo unayambira kuzilalira, kuphunzitsa kowona, kwenikweni; gulu lachitatu, kumapita kutali kwambiri; podzafika gulu lachinai, iwo unali utazimirira kukakhala—wofunda, mpingo unabweretsa mpingo wofunda.

³¹ Ndipo kenako Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu! Umene, ine ndikunena izi ndi kulemekeza kwa umulungu uku kwa chipembedzo cha munthu aliyense. Kuyambira pachiyambi, kufikira nthawi ino, weniweni, Mpingo woona wakhala uli Mpingo wa pentekoste. Izo ndi zoon. Mulungu wawusunga Mpingo uwu.

³² Ndipo ine kawirikawiri ndimadabwa, pamene Yesu anapanga ndemanga, anati, “Musawope ayi, nkhosha zapang’ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu ufumu.” Ine kawirikawiri ndakhala ndikudabwa chimene izo zimatanthauza, koma ine ndikumvetsa tsopano.

33 Sabata lapitali tinali ndi msonkhano ku Shreveport, Louisiana, msonkhano wopambana wauzimu umene ine ndinayamba ndapitako, mmoyo wanga. Shreveport!

34 Ine ndinali...Ine ndinali ndi masiku angapo a tchuthi, ndipo ine ndinapita kumusi mu Kentucky ndi M'bale Wood apa, mmodzi wa madikoni a pa mpingo, kapena matrastii, kani, kupita kukasaka. Ife tinapita mu nkhalango.

35 Ine ndinali nditawombera gologolo woyamba. Ndipo ine ndinati, "Ine ndingodikirira," chifukwa winawake anadutsa ndi agalu ena. Ndipo ine ndinati, "Ine ndingodikirira mpaka agologolo atabwerera kutuluka mmaunawo. Iwo amathamanga kukwera mmitengo, mmauna, ndipo anakabisala tsopano." Ine ndinati, "Iwo akamatuluka...Ine ndikhala pano ndipo ndizidikirira." Chifukwa, kukuzizira kwenikweni ndipo kwachita nkhungu, ndipo makutu akutentha. Ndipo, inu mukudziwa, mphe—mphepo yamphamvu ikubwera kudzera mmagwembe. Ine ndinati, "Ine ndingodikirira mpaka agologolo atulukirensa."

36 Ndisanati ndikhale pansi, Mzimu Woyera unati, "Dzuka, ndipo upite chokwezeka mtunda ku malo amene iwe umawatcha 'sportsman's hollow.' Kumeneko Ine ndikayankhula ndi iwe."

37 Ndipo ine ndinapita uko ku malo amenewo amene ine ndinawatcha "sportsman's hollow." Chifukwa, chifukwa chimene ine ndinawatchula mabowo amenewo, inemwini, chinali kuti ndizidziwa kumene ine ndiri. "Sportsman's hollow," chinali chifukwa iwo anali...Ine ndinapita kumeneko ndipo ndinawona agologolo sikistini atakhala pa mtengo umodzi; ndinawombera malire a mulingo, ndinawasiya ena onsewo pamenepo, ndipo ndinachokapo. Ndipo masewero ake ndi amenewo, chinthu choyenera kuchita. Chotero ndiye ine ndimawatchula iwo, "sportsman's hollow."

38 Ndipo Iye anandilozera ine, "Malo amene iwe umawatcha 'sportsman's hollow.'" Osati kuti Iye anawatchula iwo, koma ine ndinawatchula iwo chomwecho.

39 Kenako ine ndinapita pamwamba pa nsonga ya bowo limenero ndipo ndinakakhala pansi pa mtengo woyera wa thundu, ndipo ndinadikirira pafupifupi theka la ora, ndipo palibe chimene chinachitika. Ine ndinazigoneka ndekha pansi, ndinadzilambatitsa ndekha pansi, ndinatambasula manja anga. Kenako Iye anayankhula ndi ine.

40 Ndipo pamene Iye anatero, Mawu amene Iye anawawulula kwa ine, pa Lemba lomweli ili limene ife tikubwerapo mmawa uno, Ine ndinali ndisanaliwonepo ilo kale, mmoyo wanga wonse.

41 Ndiyeno pamene ine ndinafika ku Shreveport, Louisiana, mkazi amene ali mkazi wa mphatso, dzina lake ndi Akazi a Schrader...

⁴² Zaka zambiri zapitazo, pamene Mngelo wa Ambuye anakumana nane ine kumusi kuno ku mtsinje, nthawi yoyamba, ndipo anawonekera mu Kuwala kumeneko, ndi Mawu amene Iye anawayankhula pamenepo; zaka leveni kenako, pamene ine ndinadzalowa mu msonkhano, mkazi wamng'ono uyu anadzuka ndipo anadzayankhula ndi malirime ndipo anawatanthauzira. Iwo anali mawu pa mawu chinthu chomwecho chimene Mngelo ananena.

⁴³ Ndipo mkazi wamng'ono yemweyu, pamene ine ndinadzalowa mu kachisi pa...kapena pa malo ku Shreveport kumene ife tinali, Life Tabernacle, Mzimu Woyera unadzasanthira pa mkazi ameneyo ndipo ananena mawu pa mawu chimene Iye ananena kwa ine kumtunda uko pa phiri. Zitatero Mzimu unayamba kusuntha ndi kupereka kutanthauzira, kuneneratu zinthu mwa vumbulutso, mwa ulosi, zinthu zimene zikanadzachitika mu msonkhano usiku wotsatira, ndipo palibe nthawi imodzi izo zinalepherapo.

⁴⁴ Zisanachitike zimenezo, mkazi wamng'ono anaimirira mu msonkhano, mkazi wa Chibaptisti anabwera kumeneko asakudziwa chimene iye akanati adzachite. Ndipo iye anali ataima pakati pa msonkhano ndipo Mzimu Woyera unagwera pa iye, ndipo iye anayamba kuyankhula ndi malirime, mkazi wa Chibaptisti wochokera ku First Baptist Church cha ku Shreveport. Ndipo kenako iye samadziwa chimene iye anali atachita. Ndiyeno, iye asanayankhule kalikonse, Mzimu Woyera unapereka kutanthauzira, unati, "PAKUTI ATERO AMBUYE, 'Mkati mwa miyezi itatu, pakhala pali Mzimu wa Mose, Eliya, ndi Khristu, ukutumikira mu kachisi muno.'" Pamenepo izo zinachitika, mwangwiwo.

⁴⁵ Bambo wa Chibaptisti wochokera ku Meridian, Mississippi, anayamba kuika dzanja lake pa firiji yake, kuti atenge chinachake kuchokera mu firijiyo, ndipo Mzimu wa Mulungu unabwera pa iye. Ndipo iye anayankhula ndi malirime, asakudziwa chimene iye anali kuchita. Ndipo iye asanati... asanamvetse zimene iye amachita, Mzimu Woyera unayankhula mobwezera ndipo unati, "Upite ku Shreveport, Louisiana. Watchito Wanga akakuuza iwe choti uchite."

⁴⁶ Ndipo iye anabwera kumeneko, anati, "Ine sindikumvetsa izi; sizinachitikepo ndi kale lomwe." Oh, mai!

Ife tikukhala moyo mu masiku otsiriza basi Kubwera kwa Ambuye kusanachitike.

⁴⁷ Mpingo wawung'ono umenewo nthawizonse wakhala uli mwa ochepa, wa Pentekoste. Ine sindikutanthauza chipembedzo cha Pentekoste. Ine sindikutanthauza zimenezo. Koma, anthu okhala ndi chowachitikira cha chipentekoste! Pentekoste si bungwe. Pentekoste ndi chokuchitikira chimene chimapita kwa aliyense amene angafune. Mkatolika, Myuda, Proselyte,

Methodist, Baptisti, “Aliyense amene akufuna, muloleni iye abwere.” Ndi chokuchitikira chimene aliyense payekha... Mulungu samachita ndi chipembedzo, komanso Iye samachita ndi Amitundu ngati mtu—mtundu kapena anthu. Iye amachita ndi aliyense payekha, “Aliyense amene angafune.” Kaya iye ndi woyera, wakuda, wachikasu, waburawuni; Methodist, Baptisti, Protestanti, Mkatolika, chirichonse chimene iye ali, “Muloleni iye abwere,” aliyense. Ndine wokondwa kwambiri kuti Iye anazipanga izo mwanjira imeneyo. Ine...

⁴⁸ Monga munthu ananena nthawi ina, “Ine kulibwino ndimurve Iye akunena zimenezo kusiyana ndikuti atchule dzina langa, ‘Msiyeni William Branham abwere,’ chifukwa pakhoza kukhala woposa William Branham mmodzi. Koma pamene Iye anati, ‘Aliyense,’ ine *ndikudziwa* inenso ndatengedwamo.”

Chotero umo ndi mmene ife tonse tikhoza kumverera, “Aliyense amene akufuna, muloleni iye abwere.”

⁴⁹ Tsopano, ine ndikudziwa pali anthu ambiri akudikirira kunja kuno mu ma hotelo ndi motelo, amene abwera kuchokera kuzungulira dziko. Mukuona? Pali anthu pano ochokera ku Ireland ndi malo osiyanasiyana, akudikirira kuti awonedwe. Koma ine sinditha kuzikwanitsa izo pakali pano. Ine ndikufuna kuti ndipereke nthawi yanga kwa izi, inu mukumvetsa.

⁵⁰ Pamene ine ndidzabwerera kuchokera ku maulendo awa, ine kawirikawiri ndimabwerera kuti ndidzakhale—kuti ndidzakhale ndi winawake woti ndimutumikire, chifukwa iwo amasamalitsa zofuna kuwonedwazo. Koma pakali pano ife tikuyenera tilole izo zipite chifukwa cha Izi.

⁵¹ Tsopano, chinthu chimodzi chokha ife tisanayambe pa Bukhu ili. Pachiyambi panali Mpingo wa Pentekoste. Mpingo wa Pentekoste umenewo unakayenda mu mphamvu ya Mzimu ndipo unalemba Bukhu la Machitidwe. Gulu lachiwiri, ilo linayamba kunyentchera, mpingo unayamba kufunda. M’badwo wa mpingo wachiwiri, iwo unali utafunda kwenikweni, koma Mbewu yaing’ono imeneyo ya Pentekoste inakhala ikupitirirabe ikumabwerabe, yauzimu. Kenako iyo inadzalowa mmalo a mibadwo ya mdima, ya pafupifupi zaka fortini handire ndi chinachake, za kuzuzidwa kwa mdima. M’badwo wa Pentekoste waung’ono uja umapitirira kumakhalabe moyo kudutsa mmenemo. Mmene iwo unapulumukira izo, musandifunse ine. Ilo linali dzanja la Mulungu, chinthu chokhacho chimene chikanatha kuchita izo.

⁵² Chifukwa, iwo ankawakhomera iwo pansu, ku nsanamira. Ndipo ankawatenga amunawo ndi kuwasandutsa kukhala—chitsa, ndipo ankatenga zikhomo ndi kuzikhomera mmiyendo yawo, ndipo amasiya nyama, agalu, ziwadye iwo kuyambira ku nsana, kumakoka matumbo awo kuchoka mwa iwo, iwo asanafe nkomwe. Ankawatenga akazi, nkukawadula mabere awo, ndi

chodulira monga *chomwecho*, bere lawo lakumanja, ndipo amaimea nkuwasiya magazi amenewo azingotuluka, kufikira miyoyo itachoka mwa iwo. Ankawatenga makanda kuchokera kwa amayi oyembekezera ndi kukawadyetsa iwo kwa agalu ndi nkhumba, iwo akuyang'ana pa iwo. Pomaganiza kuti chinali Chikhristu; koma Baibulo linati, ndipo Yesu anati, "Izo zidzafika pochitika kuti iwo adzakuphani inu, kumaganiza kuti iwo akumuchitira Mulungu ntchito." Mukuona?

⁵³ Ndipo tsopano chinthu chimenecho chinakwawira pansu mpaka m'badwo winawo. Kenako potsiriza icho chinadzatulukira poyera. Ndiye ife tikuzindikira pamene mpingo unadzatulukira mu kukonzanso, iwo unayamba kuchokapo ndi kuchokapo, kuchokera nthawi imeneyo, ndipo unachoka kwa Mzimu, unachoka kwa Mzimu, kupita mpaka pansu kufikira m'badwo wotsiriza uno pamene iwo wakonzeka kudzipanga wokha chitaganya ndi kupanga chifano kwa chirombo.

⁵⁴ Koma Mzimu waung'ono uja udzakhalapobe mmitima ya anthu mpaka Yesu adzabwera. Izo zikuyenera kutero. Musunge zimenezo mu mtima mwanu.

⁵⁵ Ife tizijambula izo pa mapu, tidzatenga mbiriyakale ndi chirichonse, ndi kudzakuwonetsani inu kuti izo ndi ndendende mwanjira imeneyo. Tidzakulolani mudzatenge mbiriyakale, inueni, ndi kukawerenga iyo. Kukawona chimene Baibulo linanena, ndipo kenako chimene mbiriyakale inanena. Kuwona mmene izo zikukumanirana ndendende basi monga *chomwecho*. Oh!

⁵⁶ Ife tonse tisangozitenga izi ngati phunziro, koma ife mwaulemu, mwaulemu titenge machenjezo a Mzimu Woyera ndi kupemphera, usana ndi usiku. Musalole chirichonse chikulepheretseni inu kuti musamapemphere.

⁵⁷ Ife tilowa mkati, izo zikumbira pamwamba miyoyo ya amuna opambana amenewo kumbuyo uko, momwe iwo ankaperekera nsembe. Inu mudzawona momwe mwachitira zapang'ono. Zimandipangitsa ine kudzichitira ndekha manyazi nthawizina, mmene ife timachitira kukhala ndi chirichonse mophweka, ndipo iwo ankakhala ndi chirichonse mochita kuvutikira. "Ankayendayenda," Paulo ananena mu Ahebri 11, "mu zikopa zankhosa ndi zikopa zambuzi, ankazunzidwa ndi kusautsika, osowa pokhala." Umboni wathu udzaima bwanji pambali pa wawo? Iwo udzakhala motani pambali pa umenewo? Ndipo ife timafuna chirichonse chizikhala mwabwino kwambiri.

⁵⁸ Tsopano, basi molemekeza, ife tisanatsegule Bukhu, ine ndikufuna kuti ife tonse, amene tingathe, tingoima kwa mphindi la pemphero. Tsopano ndi kudzipereka kwa mtima wanu, mupume liwu la pemphero kwa . . . kwa Mulungu.

⁵⁹ Ambuye Mulungu, Mlenzi wa miyamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo Wosatha, ndi Wopereka wa mphatso zonse zabwino ndi zangwiwo. Ife tikukupemphani Inu, Ambuye, poyamba, kuti mutikhululukire ife kusayanjanitsika kwathu konse, ndi machimo athu ndi zolakwitsa zathu pa Inu, ndi zoyambana wina ndi mzake ndi azimzathu.

⁶⁰ Mulole nthawi yapang'ono iyi yobwera pamodzi isangokhala yomangiriza miyoyo yathu yokha, koma mulole ikhale yotiwunikira ife mwanjira imeneyo, ndi kutidzoza ife, kufikira kuti ife tikapite ndi kukawauza ena. Mulole ikhale nthawi yodziperekanso, kulumikizana ndi Thupi lathunthu la Khristu ndi kukhala wokonzekera Mkwatulo.

⁶¹ Atate Mulungu, osati mwakumverera kwanga komwe, podziwa kuti wantchito Wanu, ndi antchito ena onse, ndi osakwanira ku ntchito yaikulu iyi. Pozindikira mmene amuna amphamvu, amene anapita, anazitengera pa mitima yawo kuti ayesere kuwulula Izi, kapena kuchitira ndemanga pa Vumbulutso lalikulu; ndiye ife tikuzindikira kuti ndife, ochuluka kuposa iwowo, osakwanira. Koma Inu muli wokwanira wathu.

⁶² Ndipo ine ndikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu muchite chinachake chapadera mu nthawi ino, kuti Mzimu Woyera ukhale ndi uyambiriro mu mtima uliwonse. Muvinire milomo imene iyankhule ndi makutu amene ati amvetsera. Ndipo pamene izi zonse zidzatha, ndipo ife nkupereka izo kwa Inu, mulole ife tidzayende kuchoka pansu pakhomo la nyumba iyi, tikuti, “Izo zinali zabwino kwa ife kukhala kumeneko. Mzimu Woyera unayankhula ndi ife pamene ife tinakhala pamenepo. Ndipo tsopano ife tiri otsimikiza kuti tichita zonse zimene ife tingathe pamene Nyali zamadzulo zikuwala.” Perekani izi, Ambuye.

⁶³ Mulole, pa msonkhano uno, zipangitse amuna ndi akazi kuti agwiritsitse, mwatsopano. Inu muwukitse oyankhula ndi malirime, otanthauzira malirime. Inu muwukitse mphatso za kunenera. Muwukitse alaliki, azibusa, avangeli, ena otero, kuti Mpingo ukakhoze kumangirizidwa. Muwukitse mamishonare kuti apite mminda kutali ndipo akabweretseko Uthenga wa ulemelero uwu. Kulikonse kumene Mawu ati adzapite, mulole Iwo akagwere pa nthaka yabwino, azikabweretsako mazana mazana, pakuti ife tikukhulupirira kuti ife tiri kumapeto a m'badwo. Chimaliziro chayandikira.

⁶⁴ Perekani zinthu izi, Atate. Ndipo pamwamba pa zinthu zonse, Ambuye, pa nthawi ino, ndithandizeni Inu ine, iye wosowayo. Pakuti ine ndikupempha izi, pamene ine ndikudzipereka inemwini kwa Inu chifukwa cha misonkhano iyi, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

[Mlongo akuyankhula mu lirime lina, m'bale akutanthauzira—Mkonzi].

⁶⁵ Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe munamuukitsa Yesu kwa akufa, ife tiri okondwa kwambiri kudziwa kuti Mzimu Wanu ukukhala pakati pathu. Nthawizonse Iye ndi woona ndipo wopanda mawu abodza. Ndipo tsopano, Atate, tsimikizirani mopitirira Mawu Anu pamene ife tikuwawerenga, kwa ulemelero Wanu. Ndipo mulole mtima uliwonse, monga Inu mwanenera, “Ukhale wokonzeka ndi wokonzekera, pakuti pakubwera chinachake.” Icho mwinamwake chikhoza kukhala kuti anthu alandira chenjezo lawo lotsiriza kuti achoke ku zinthu zimene iwo akuchita tsopano, kupita ku njira yolondola. Ife tikukuthokozani Inu, Mulungu Woyera, mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu. Ameni.

⁶⁶ Kutembenukira tsopano ku Bukhu la Chivumbulutso, mutu wa 1. Tsopano, poyamba, ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime zitatu zoyambirira za Chivumbulutso.

Chivumbulutso cha Yesu Khristu, chimene Mulungu anachipereka kwa iye, kuti akamuwonetse wantchito wake zinthu zimene zikuyenera kufika pochitika posachedwapa; ndipo iye anatumiza ndipo anazizindikiritsa izo ndi mngelo wake kwa wantchito wake Yohane:

Yemwe anachitira umboni wa mawu a Mulungu, ndi umboni wa Yesu Khristu, ndi kwa onse...za zinthu zonse zimene iye anaziwona.

Wodala ndi iye amene awerenga, ndi iwo amene amvetsera mawu a chinenero ichi, ndi kusunga zinthu zimenezo zimene zinalembedwa mmenemu: pakuti nthawi yayandikira.

⁶⁷ Monga ine ndinanenera kale, tsopano, mu zimenezi ife tiyesera kuti tipereke kugawaniza pang'ono tsopano kwa Bukhuli, molingana ndi mbirizakale ndi zina zotero. Ndipo nthawi iliyonse pamene inu muzindiwona ine ndikulozera ku masamba amene ine ndawalemba apa, ndi zinthu zimene ine ndazitenga kuchokera mu ndemanga ndi zina zotero.

⁶⁸ Tsopano, mlembi wa Bukhu ili ndi Yohane, Yohane Woyera wauzimu, analemba ku m'badwo wamtsoyolo (A). (B) Kupita kwa angelo asanu ndi awiri a nthawi zisanu ndi ziwiri zosiyanasiyana za m'badwo wa Chikhristu, m'badwo wochokera ku masiku a atumwi mpaka ku Kubwera kwa Ambuye. Ndipo...tsopano, mibadwo ikuwonekera molandizana, umodzi uliwonse, kuchokera ku kukwera mmwamba kwa Ambuye wathu mpaka ku Kubwera Kwake kwachiwiri. M'badwo wa mpingo uliwonse umafotokozedwa ndi chikhalidwe chake chazimu. (E) M'badwo wa mpingo uliwonse ukhoza kudziwona wokha mwa kuyankhula kwake kwa Malemba ndi uzimu kwa

iwo. Pamene Mzimu ukuyankhula, m'badwo uliwonse ukhoza kudziwona wokha. M'badwo uliwonse umabereka Mpesa woona wa Khristu, namwali Wochenjera. Ndipo m'badwo uliwonse umabala mpesa womedzanitsidwa, namwali wopusa.

⁶⁹ Azambiriyakale amavomereza, uwu ndi moyo wa Yohane. Yohane anakhala moyo zaka zake zotsiriza mu mzinda wa Efeso ndipo anafera kumeneko. Iye anali pa chisumbu cha Patmo, pa nthawi imene iye ankalemba Bukhuli, Chivumbulutso. Iyo siinali nkhani ya moyo wake, koma nkhani ya Khristu mu mibadwo ya mtsogolo. Mukuona? Iwo unali ulosi. Osati moyo wa Yohane, osati moyo wa Khristu, koma amalosera za m'badwo umene unkadza. Iwo sanali maneno ake a ulosi; koma, kumukweza Ambuye, mwaulemu. Ilo si Vumbulutso la Yohane Woyera wauzimu, koma Vumbulutso la Khristu Ambuye.

⁷⁰ Ilo ndi Bukhu lotsiriza la Chipangano Chatsopano, komabe ilo limanena chiyambi ndi mathero a nyengo ya Uthenga. Tiri ndi oluphuzira za Baibulo amene amavomereza.

⁷¹ Makalata opita kwa mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo analembedwa, mwauneneri, kupita ku mibadwo ya mtsogolo. Paulo analemba za moyo ndi ulemelero wa mipingo isanu ndi iwiri imene inalipo mu tsiku lake. Yohane analemba za moyo ndi ulemelero wa mipingo isanu ndi iwiri ya mtsogolo, kuti Yohane amalemba azibusa asanu ndi awiri kapena amthenga monga molunjika kwa Akhristu onse a pansu pa angelo osiyanasiyana asanu ndi awiri amenewa.

⁷² Tsopano, Bukhu la Chivumbulutso, tsopano ife titenga, pamene ife tikunyemanyema izi mmawa uno ndi madzulo ano. Ndipo ife tiyesetsa kuti tituluke pafupifupi leveni koloko ndi hafu-leveni, chinachake monga chomwecho, ndipo kenako tidzayambiranso usikuuno pa seveni.

⁷³ Tsopano zamkati za mutu wa 1 uwu. Ndime ya 1, iyo—iyo kwenikweni imadziyankhulira Yokha, chifukwa iyo ndi Chivumbulutso cha Yesu Khristu. Ndime ya 2, Yohane Woyera wauzimu ndi mlembi ndi wantchito. Ndime ya 3, madalitso akulengezedwa. Ya 4 kudutsa ndime ya 6, malonje kwa mpingo. Ndime ya 7, kulengeza. Ndime ya 8, Umulungu wapamwamba wa Yesu Khristu. Ya 9 mpaka ku ndime ya 20, masompheya apa Patmo.

⁷⁴ Ndipo, aponso, ndime ya 14 ndi ya 15 imafotokoza za ulemelero Wake wofutukuka pasanu ndi pawiri wa Umunthu Wake. Oh, ndi zokongola pamene ife tizimuwona Khristu mu ubusa Wake wofutukuka pasanu ndi pawiri wa-... umunthu wofutukuka pasanu ndi pawiri wa ubusa Wake, mu chiukitsiro Chake cha ulemelero.

⁷⁵ Tsopano, udindowo ukufotokoza za khalidwe.

Chivumbulutso cha Yesu Khristu, . . .

⁷⁶ Osati vumbulutso la Yohane Woyera wauzimu, koma Chivumbulutso cha Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.

⁷⁷ Tsopano, mawu a Chigriki a *vumbulutso* ndi *apocalypse*, amene amatanthauza “kufutukuka.” Ndipo ine ndimatenga mawu amenewo ndi kuwafufuza iwo. Iwo amatanthauza, *apocalypse*, ndi ku...Monga wosema, wapanga chosema chachikulu, ndipo iye wachivindikira icho ndi chophimbira. Ndipo kenako akupita ndi kukaching’amba chophimba chimenechi ndi kuwulula chimene ali nacho kuseri kwa chophimbacho. Kumeneko ndiko kuvundukula.

⁷⁸ Ndipo Bukhu ili si kuvundukula kwa, mochuluka chomwecho, Munthu wa Yesu Khristu. Komabe, izo ndithudi zikuyankhula za Umulungu Wake ndi kufutukuka pasanu ndi pawiri kwa ubusa Wake, ndiponso kwa zinthu zimene Iye ali, monga Wansembe, Mfumu, ndi zina zotero. Koma iko ndi kuwulula kwa tsogolo la ntchito Zake mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo Yake imene ikubwera. Iyo . . .

⁷⁹ Pamene Ambuye wathu anali pa dziko lapansi, ophunzira anamufunsa Iye, ndipo anati, “Ambuye, kodi inu pa nthawi ino mubwezeretsa ufumu kubwerera kwa Israeli?”

⁸⁰ Ndipo Yesu anati, “Si kwa inu kuti mudziwe ora lino kapena nthawi.” Ndipo palibe mmodzi amene angadziwe. Anati, “Ngakhale Mwana,” mpaka pano, “samadziwa.”

⁸¹ Koma itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro, ndi kukwera mmwamba mu Ulemelero, Iye analandira kuchokera kwa Mulungu tsogolo la Mpingo. Kenako Iye anabwereranso, kuti adzabweretse Uthenga uwu ku Mpingo, ndi Uthenga uwu wa kubwera Kwake ndi chikhalidwe cha mipingo Yake kutsika kudutsa M’badwo.

⁸² Iye sakanatha kuchita zimenezo imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro zisanachitike, chifukwa Iye anali asanazidziwe izo apabe. Koma kodi inu munazindikira mmene Lemba likuwerengekera apa?

Chivumbulutso cha Yesu Khristu, chimene Mulungu anapereka kwa iye (Khristu), . . .

⁸³ Mmene kuti Mulungu Atate anaperekera Chivumbulutso kwa Mwana Wake Yesu Khristu. Ndipo Iye anamtuma mngelo Wake kupita kwa Yohane, kuti akazizindikiritse zinthu izi zimene zinali; zimene zinali, zimene ziri, ndi zimene zidzakhala. Oh, izo zaikidwa mokongola!

⁸⁴ Tsopano, mu m’badwo waukulu uwu umene ukubwera umene Yohane amawuwona! Tsopano, izi, Chivumbulutso ichi chinaperekedwa kwa iye, mosamalitsa, kuti chikawulule cholinga chinachake cha Khristu, chimene Iye akanati adzakhale ndi kudzakhala, mu m’badwo uliwonse. Ndi chifukwa chake ine ndinanena, mmawa uja, muike malingaliro anu

pa Mpingo woona. Mpingo woona unayamba pa Tsiku la Pentekoste.

⁸⁵ Palibe wazaumulungu, wophunzira Baibulo, kapena wazambiriyakale, amene angakhoze kunena kuti iwo unayamba mmasiku a Martin Luther, Wesley, m'badwo wa Katolika, kapena m'badwo wina uliwonse. Iwo unayambira pa Pentekoste. Kumeneko kunali kutsegulira kwa Mpingo. Chimenecho chinali chiyambi. Koteru, choteru, mu kukambirana ndi wina aliyense, muziima pa chipata cha Pentekoste, ndipo iwo sangathe kupita kwina kulikonse.

⁸⁶ Ziri ngati kumuika kalulu mmunda. Iwe umadziwa pamene bowo lirilonse liri, ndiye iwe umakatseka pamenepo. Iye akuyenera kuti adzabwerere pa malo omwe awa amene iye analowerapo.

⁸⁷ Chabwino, ndiyo njira yake, aliyense akamayankhula zokhudza mipingo ndi mibadwo ya mpingo, ndi ntchito za Mzimu Woyera, iwe ukuyenera kubwereranso ku chiyambi, koyambirira. Izo zikuyenera kubwerera kumeneko chifukwa Mulungu ndi wopandamalire, ndipo Iye ndi wamphamvuzonse. Choteru, Iye pokhala wopandamalire, Iye sangakhoze kuchita chinachake *apa*, ndi kudzachita chinachake chosiyana ndi icho, cha *apa*. Iye akuyenera kuchita nthawi iliyonse monga Iye anachitira icho nthawi yoyambirira.

⁸⁸ Monga Petro ananena, pa tsiku la... pamene Amitundu analandira Mzimu Woyera, iye anati, “Kodi ife tingaletse madzi, powona kuti iwo alandira Mzimu Woyera monga ife tinachitira pachiyambi?”

Yesu, pamene Iye anali pa dziko lapansi, anayankhula ndipo anati, “Iwo...”

⁸⁹ Winawake anabwera ndipo anati, “Kodi ndi koyenera kwa ife, kusiya akazi athu pa chifukwa china chirichonse?”

⁹⁰ Yesu anati, “Iye amene anampanga mwamuna, anampanga mkazi. Pa chifukwa ichi mwamuna adza...”

Iye anati, “Koma Mose anatiloleza ife kalata ya chilekaniro.”

Yesu anati, “Sizinali chomwecho kuyambira pachiyambi.”

⁹¹ Bwererani ku chiyambi. Choteru, ngati ife tingayankhule za m'badwo wa mpingo, ife tikuyenera kubwerera ku chiyambi, kuyika pambali neno lirilonse limene munthu aliyense anapanga kutsika kudutsa m'badwo.

⁹² Ili ndi Bukhu lovomerezeka kwambiri la Bukhu lirilonse la mu Baibulo. Ili ndi Bukhu lokhalo limene Khristu anaikapo chisindikizo Chake pa ilo. Ilo likuyamba ndi mdalitso ndipo likuthera ndi themberero. “Wodala ndi iye amene awerenga.” Ndipo, “Wotembereredwa ndi iye amene adzachotsa chirichonse kuchokera mwa Ilo.”

⁹³ Ilo ndi Bukhu lokhalo limene Khristu analilemba, Iyemwini, la Baibulo lonse. Malamulo Khumi, Iye analembe ndi chala Chake. Uko nkulondola. Ayuda anagwiritsitsa kwa zimenezo. Ndipo, lero, ndi a—a Chivumbulutso.

⁹⁴ Ndipo ngati Satana amadana ndi Bukhu lirilonse mu Baibulo, ndi Chivumbulutso. Alipo awiri. . .Iye amadana ndi Lemba lonse, ndipo ndiyo nsonga yonse ya Lemba. Koma, ngati chirichonse, chimene iye amachinyoza kwambiri, ndi Chivumbulutso ndi Genesis. Chifukwa, Genesis imanena za chiyambi. Chivumbulutso chimawulula chimene chidzachitike kwa iye mu tsiku lotsiriza. Adzamangidwa kwa zaka sauzande; kenako iye, ndi mneneri wabodza, ndi chirombo, adzaponyedwa, wamoyo, mu Nyanja ya Moto.

⁹⁵ Ndipo iye amalimbana ndi Bukhu la Genesis chifukwa cha—chifukwa cha kulondola kwake. Iye amanena, kuti, “Ilo si lolondola.” Ndipo iye amakondoweza malingaliro a anthu. Penyani kumene mdierekezi amakhala, Bukhu limenelo la Genesis kapena Bukhu la Chivumbulutso, loyamba ndi lotsiriza.

⁹⁶ Ndipo Bukhu la Chivumbulutso liri ndi ziphiphiritso zochuluka mwa ilo kuposa Mabuku ena onse mu Baibulo. Ilo liri ndi ziphiphiritso zochuluka chifukwa ilo ndi Bukhu la uneneri. Ilo ndi Bukhu la uneneri. Chotero ilo likuyenera kumvetsedwa ndi kalasi la uneneri. Bukhu limeneri silinapangidwe kuti likhale la aliyense. Palibe wina aliyense amene angathe kulimvetsa ilo, nkomwe. Bukhu ili linapangidwira kagulu kenakake ka anthu. Cha mu Deuteronome, Ilo limati, “Zinthu zobisika ndi za—za—za Ambuye.” Uko nkulondola. Ndipo Iye amawulula kwa ife, ana Ake, zinthu zobisikazo. Chotero izo sizimapita. . .

⁹⁷ Malingaliro achithupithupi sangakhoze kuzimvetsa zinthu zopambana zimenezo za Lemba, chifukwa izo ndi zopusa kwa iwo. Koma kwa iwo amene ali okonda Mawu a Mulungu, ndiwo amene Bukhulo linalembedwera, kwa Mpingo. Chivumbulutso cha Yesu Khristu, “Kwa mpingo wa ku Efeso, kwa mpingo wa ku Smurna, kwa mpingo, kwa mipingo,” mpaka mmusi. Chivumbulutso cha Yesu Khristu kwa Mpingo. Ine ndikuzikonda zimenezo.

⁹⁸ Ndipo zindikirani, ilo lirinso chimaliziro cha Malemba, chimaliziro chathunthu. Ndipo mwa jogalafe linaikidwa pa malo oyenera, kumapeto kwa Baibulo. Chivumbulutso cha chinthu chonsecho chinaikidwa kumbuyo kuno ndi mdalitso kwa yemwe atawerenge Ilo ndi kumvetsera Ilo, ndi themberero kwa iwo amene adzawonjezere kapena kuchotserapo. Ilo ndi nsonga yathunthu, oh, mtheradi. Palibe chimene chingakhoze kuwonjezeredwa kwa Ilo. Ndipo pamene munthu ayesera kuchotsa chirichonse kuchoka kwa Ilo, kapena kuwonjezera chirichonse kwa Ilo, Mulungu anati Iye adzatenga gawo lomwelo

kulichotsa kuchokera mu Bukhu la Moyo. Mukuona? Iye akanadzachotsa gawo lake kuchokera mu Bukhu, ngati iye awonjezera kwa Ilo.

⁹⁹ Chotero, pamene ife tiwona zambiri za Vumbulutso la Ambuye wathu, yemwe Iye ali, chimene Iye ali, ngati munthu aliyense adzawonjezera chinachake kwa Ilo kapena kudzachotsamo chirichonse kuchoka mwa Ilo, zimenezo ndi uneneri wabodza. Ambiri ayeserapo kunena kuti iwo anali ndi chinachake chatsopano chosiyana ndi Ilo. Koma Ilo ndi Vumbulutso lathunthu la Ambuye Yesu mu m’badwo Wake wa mpingo ndi mu Tsiku Lake, Vumbulutso la Ambuye wathu.

¹⁰⁰ Tsopano—tsopano, *kuvundukula*, mawu a Chigriki, chinachake chimene chabisika, chosa- . . . “kuwulula” Khristu.

Tsopano, ndime yotsatira, ife tikupeza, mu ndime ya 2.

¹⁰¹ Ndime ya 1 ikumuvundukula Khristu, Chivumbulutso, kapena kumuvula. Oh! Mmene m’badwo wotsiriza ndi Kubwera kwa Ambuye kunali ko- . . . kunaphimbidwa, kwa atomwi! Iwo anafunsa funso, koma mmodzi yekha anakhala moyo kuti akhale ndi Vumbulutso. Ndipo komabe, iye sanazimvetse izo, chifukwa mbiriyakale inali isanapangidwe apabe.

¹⁰² Tsopano, mbiriyakale ya Bukhu ili, kapena n—nkhani za Bukhu ili, zinalunjikidwa ku mipingo seveni mu Asia Minor, imene inalipo panthawi imeneyo. Izo zinalunjikidwa kwa mipingo isanu ndi iwiri imeneyo. Kunali mipingo yochulukira kuposa isanu ndi iwiri imeneyo, pa tsiku limenero. Koma umodzi uliwonse wa mipingo imeneyo umadziwika ndi khalidwe mu mpingo umenewo, limene likanadzatsatira iwo kutsika kudutsa m’badwo, khalidwe la mpingo umenewo. Monga wa Efeso, iwo unali ndi khalidwe. Smurna, Pergamo, ndipo mpaka mmusi, Filadelfia, uliwonse wa mipingo imeneyo unali ndi khalidwe mwa iwo, limene likanadzawonekera kenanso mu mibadwo yakudza. Oh! Ngati inu mukanangoti basi . . .

¹⁰³ Munthu aliyense akhoza kuwona ku—kugwira ntchito kwauzimu kwa Malemba ndipo akhoza kunena kuti iwo sanali odzodzedwa? Zochita zanu zomwe, cholinga kumene, zolinga kumene za anthu, bwanji, izo zimatsimikizira kuti Lemba ndi lodzodzedwa, kuwona momwe Mulungu amaziikira zinthu zimenezo. Basi zimene inu mumachita, *apa*, pali choimira cha chinachake.

¹⁰⁴ Monga Abrahamu akumupereka Isaki, mwana wake yekhayo; choimira cha Mulungu kumupereka Mwana Wake, zaka mazana mtsogolo. Mmene Yosefe anagulitsidwira ndipo ali mndende, wodedwa ndi abale ake ndipo wokonedwa ndi bambo ake; Yesu, mu choimira. Mmene Mzimu unkagwirira ntchito kudzera mwa Yosefe, munthu, ndipo mophweka zimaimirira moyo wa Khristu, mwangwirowo. Mmene, Davide, Mwana wa Davide anadzakhala pa phiri lomwelo. Pamene

Davide anakanidwa ngati mfumu ndipo anapita pamwamba pa phiri, Phiri la Azitona, akuyang'ana mmbuyo, akulira, ngati mfumu yokanidwa; zaka mazana pang'ono zitatha zimenezo, Mwana wa Davide anadzakwera phiri lomwelo, ngati Mfumu yokanidwa, ndipo analirira Yerusalemu. Mzimu mu choimira ndi mawonekedwe. Oh!

105 Ndiye kodi inu mukukhoza kuwuwona Mpingo wa pentekoste waukulu mu tsiku lotsiriza lino? Kodi inu mukukhoza kuwona mmene Mulungu anatsegulira izo pa Tsiku la Pentekoste? Mzimu umenewo uyenera kukhalabe mu Mpingo kudutsa mibadwo yonse.

106 Iwo anakhala ofunda ndi osayanjanitsika. Iwo amayenera kukhala ndi chipembedzo. Iwo anachita kulumikizitsa mpingo ndi boma pamodzi, ndipo potsiriza iwo anachita zimenezo ndipo zinapangitsa zaka mazana za chisautso. Kenako, Kukonzanso, iwo anatulukamo. Ndipo chaka chirichonse, iwo akhala akudzidula kuchoka kwa Mzimu ndi kumawonjezera ku chathupi, kuchoka ku Mzimu ndi kumawonjezera ku zathupi, mpakana tsopano iwo akonzeka basi kuti achite izo kenanso. Ife tikukhala moyo mu maora otsiriza ano, otsekera, chimalizitso cha mpingo. Ife tiri mu Filadelfiya...kapena M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya.

107 Tsopano, mutu wa 1, ndime ya 1, ikufotokozedwa kwa—kwa Yohane. Tsopano, wolembayo ndi ndani? Yohane. Yohane. Ilo silinali vumbulutso la Yohane, ndipo ife tikudziwa kuti ilo silinali, chifukwa ilo linali Vumbulutso la Ambuye Yesu Khristu. Iye anali ichi, iye anasankhidwa kukhala wophunzira. Ndipo Bukhulo Palokha likuwulula chimene chinthucho chinali, Yesu Khristu, kwa amene Iye amadziwulula.

108 Ndipo izo zinatimizidwa kwa...“Ndipo anazindikiritsa izi mwa mngelo wake kwa Yohane.” Ife sitikudziwa yemwe mngeloyo anali. Baibulo silimanena yemwe mngeloyo anali. Koma ife tikudziwa kuti iye anali mneneri, chifukwa Baibulo mtsogolo linanena, kuti, “Ine Yesu ndatumiza mngelo wanga kuti adzachitire umboni zinthu izi zimene zikuyenera kuchitika posachedwapa.”

109 Kenako ife tikupeza kuti pamene Yohane anayamba kumupembedza mngeloyu, mngeloyo anati, “Tapenya usachite zimenezo.” Chivumbulutso 22, ine ndikukhulupirira ndi pamene. Ndipo iye anati, “Pakuti ndine wantchito mzako ndipo wa aneneri.” Iye akhoza kukhala kuti anali Eliya. Iye akhoza kukhala kuti anali mmodzi wa aneneri. Yohane anali mtumwi. Koma mneneri uyu anatomizidwa.

110 Ndipo Yohane, pokhala mtumwi, taonani chikhalidwe cha makalata ake onse, zikutsimikizira kuti sanali Yohane amene analemba iwo, chifukwa iwo alibe chikhalidwe ngati cha Yohane. Mutenge Yohane Woyamba, Yohane Wachiwiri, ena

otero, ndipo muwerenge izo. Ndipo muwone chikhalidwe cha zimenezo, kenako muwone chikhalidwe cha izi. Yohane anali mlembi ndipo anali mtumwi, koma uwu ndi mzimu wa mneneri. Uyu ndi munthu wosiyana, palimodzi. Mukuona? Sizinali zolembe za Yohane. Silinali vumbulutso la Yohane. Ilo linali Vumbulutso la Mulungu la Yesu Khristu kwa mipingo. Ndipo ilo linali. . . Yohane anangokhala wolembe, mlembi, ndipo—ndipo Bukhulo likulengeza chomwecho.

¹¹¹ Tsopano, izo sizinalembedwere kwa Yohane. Izo zinalembedwera kwa Mpingo. Chabwino. Yohane, pa nthawi imeneyo, anali m’busa wa mpingo wa Efeso. Ndipo tsopano Bukhulo linalembdwe kwa Yohane. . . kapena kwa mpingo, osati kwa Yohane.

¹¹² Tsopano ndime ya 3, Iye akulengeza madalitso. Tamvetserani pa izi.

Wodala ndi iye amene awerenga, ndi iwo amene amvetsera mawu a chinenero ichi, ndi kusunga zinthu zimenezo zimene zalembedwa mmenemo: pakuti nthawi yayandikirira.

¹¹³ Nthawi yake iti imene yayandikirayo? Nthawi imene zinthu izi zikuchitika, pamene Vumbulutso ili la Yesu Khristu likutsirizika mu m’badwo wa mpingo uliwonse.

¹¹⁴ Tsopano chifukwa chimene Iye analembera izi monga chonchi. Ngati iye akanati, “Chabwino, tsopano, Iye. . .” Iwo amamuyembekezera Iye kuti atero; ngati izo zikanawululidwa, ngati Iye. . . izo zikanawululidwa kwa Yohane, kuti Iye akubwera mwamsanga mipingo imeneyo kumeneko ikamalizika. Umo ndi mmene Yohane ankaganizira zimenezo. Koma ngati izo zikanatero, mipingo imeneyo, mwamsanga iyo ikamalizika, iyo ikafika. . . Ngati iye akanadziwa, ngati izo zikanawululidwa kwa iye kuti pakhala mibadwo ya mpingo isanu ndi iwiri yaitali, zaka zikwi zingapo, kapena zaka mazana angapo, ndiye sipakanakhala chifukwa chodikirira. Iwo basi akanangokhala mu m’badwo wawo wa mpingo.

¹¹⁵ Chotero, Mulungu anayankhula izo, ndipo izo sizinawululidwe kwa iwo. Izo sizinawululidwe kwa Martin Luther, zinthu zimene John Wesley ankazidziwa za Lemba. Izo sizinawululidwe kwa a Baptist, chimene a Pentekoste amadziwa zokhudza Lemba, chifukwa izo ziri mu m’badwo wosiyana. Iyo ndi nthawi yosiyana. Ndipo Mulungu amawulula zinthu Zake basi mu nyengo yake. Oh!

¹¹⁶ Inu simungabzale chimanga mu nthawi yamasika ndi kukolola pa nthawi yomweyo. Inu mumabzala mbewu ndipo iyo imakula nkudzafika pokhwima. Mulungu amabzala Mawu Ake ndipo kenako Iwo amakula. Ndipo kenako ife timayang’ana mmbuyo ndi kudzati, “Kumeneko Iwo anali.” Bwanji, ndithudi, ife tikuwawona Iwo atatha kuwululidwa.

117 Tsopano, “Wodala,” Mawu, kulengeza kwa mdalitso, pa ndime ya 3, “kwa iwo amene awerenga kapena kumva zinsinsi zake.”

118 Kupanga... malingaliro achithupithupi amazikana zimenezo, chifukwa malingaliro achithupithupi samadziwa kanthu kalikonse kokhudza izo. Nzosadabwitsa malingaliro achithupithupi samazidziwa izo, chifukwa ndi Satana mmalingaliro achithupithupi amenewo. Ndipo Satana akuyalutsidwa, ndipo Satana samafuna iyeyo kuti aziyalutsidwa.

119 Inu mumawona momwe izi zimakhalira zowopsya kwa Satana pamene iye aganiza kuti akukayalutsidwa? Mudzawone mu umodzi wa misonkhano. Mudzawone mmene anthu amachitira. Inu mudzawonetsetse, pa msonkhano. Basi Satana asanafike poyalutsidwa, pa munthu winawake, inu mukhoza kudzawona nkhope zawo zikusinthatantha. Inu mwaona, iwo samadziwa choti aganize. Zonse pakamodzi, Mzimu Woyera umabwera pansu ndipo umadzamuyalutsa mdierekezi ameneyo. Oh! Iye amadana nawo msonkhano wa mtundu umenewo. Ndi chifukwa chimene ife takhala ndi nkondo yoteroyo, chifukwa Mawu a Mulungu amamuyalutsa mdierekezi. Mukuona? Iwo amanena chimene iye ali.

120 Monga iwe kunena kuti, “Mkazi uyu wakhala apayu,” pansu pa kudzodza kwa Mzimu Woyera, kuti, “dzina lake ndi Abiti Jones. Iye amachokera Kwakuti-ndi-kwakuti.” Kodi chimenecho chikuchita chiyani? Icho chimakatenga mzimu wake, ndikuwubweretsa iwo pamenepo.

121 “Inu mwandidziwa bwanji ine? Bambo ameneyo samandidziwa ine, chotero iwo ukuyenera kukhala mzimu winawake. Ndi mzimu wa mtundu wanji umenewo?”

“Ndi Mzimu wa Mulungu.”

“Motani? Vuto ndi chiyani ndi ine?”

122 “Inu muli ndi chifuwa chachikulu, khansa,” chirichonse chimene icho chiri, “koma PAKUTI ATERO AMBUYE. . .”

“Oh!” Oh, mmene Satana amadana nazo izo, chifukwa Izo zimamuyalutsa iye.

123 Tsopano, malingaliro achithupithupi amayang’anitsitsa pamenepo, ndikuti, “Kuwerega-maganizo, zam’bwebwe.” Iwo sakuzidziwa izo. Izo ndi zopusa kwa iwo.

124 Koma kwa iwo amene akudziwa chimene Iwo uli, oh, ndi mdalitso bwanji! Ndi chiyani chimenecho? Vumbulutso. Vumbulutso la ndani? La munthu ali pa guwa? La Yesu Khristu mu m’badwo wa mpingo wotsiriza uno, akudziwulula Iyemwini monga Iye analonjezera kuti Iye akanadzachita. Mukuona?

125 Ndi vumbulutso, mwaona, ndipo Satana amadana nazo izo. Mai, mmene iye amadanirana nazo izo! Iye amayalutsidwa,

zimayalutsa mapulani ake. Satana amadana ndi Chivumbulutso ndi Genesis, ine ndinalemba apa. Izo ndi ndendende zoon.

¹²⁶ Tsopano, nchifukwa chiyani iye amadana ndi vumbulutso? Nchifukwa chiyani iye amatsutsana kwambiri ndi vumbulutso? Ndi chifukwa chakuti nsonga yonse ya Mawu a Mulungu ndi Mpingo wa Mulungu zinamangidwa mwaulemu pa vumbulutso.

¹²⁷ Izo sizidzakhala konse kudzera mu—mu sukulu, ziribe kanthu ndi ma seminare abwino angati amene ife tiri nawo. Iwo ali mmbuyo kutali mu m’badwo wa mdima. Baibulo ndi Mpingo ndizo mwamtheradi vumbulutso.

¹²⁸ Tiyeni titembenuzire, ine ndiri ndi Malemba ena alembedwa apa, Mateyu, wa—mutu wa 16 ndipo ndime ya 18. Tiyeni tingotenga pang’ono—tiyang’ane pang’ono pa Mateyu 16:18, tiwone pamene Malemba ali, pamene pali vumbulutso. Akutsika kuchokera pa phiri, ndime ya 17.

Ndipo Yesu anayankha ndipo anati kwa iye, Wodala ndiwe, Simon Bar-yona: pakuti thupi ndi mwazi sizinawulule izi kwa iwe, koma Atate anga amene ali kumwamba.

Ndipo Ine ndikuti . . . kwa iwe, . . . iwe ndi Petro, ndipo pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo mpingo wanga; ndipo zipata za gehena sizidzawuluka iwo.

¹²⁹ Tsopano, mpingo wa Katolika umati, “Iye anawumanga iwo pa Petro.” Chabwino, uko, uko ndi kuganiza kwachithupithupi kwenikweni. Inu simungakhoze kulingalira kuti malingaliro auzimu angavomereze chinthu ngati chimenecho; monga Mulungu, ndi Mwana Wake Yemwe ataima pamenepo, ndipo komaba akanatha kumanga Mpingo Wake pa munthu wamba, wopanda pake, wobadwa mu tchimo. Munthuyo anatsimikizira izo. Iye, ndi mzimu womwewo pa iye, iye anamutukwana Yesu ndipo anamukana Iye pankhope Yake. Izo sanali Petro.

¹³⁰ Kapena, komanso ilo silinali tha—thanthwe limene linakhala pamenepo, monga mipingo ina imati iwo unali. Silinali thanthwe. Chifukwa, Petro . . .

¹³¹ Thanthwe limene Iye anali kulikamba pamenepo, silinali Petro, komanso sanali Iyemwini.

¹³² Tsopano, ambiri a anthu a Chiprotestanti amayesera kunena kuti, “Izo anali Yesu. Izo zinali Iye pamene Iye anamangapo Mpingo. Iye!” Ayi, izo ndi zolakwikabe. Ngati inu mungazindikire, sanali Yesu, komanso sanali Petro. Ilo linali vumbulutso.

. . . thupi ndi mwazi sizinawulule izi kwa iwe, koma Atate anga amene ali kumwamba achita vumbulutso limeneli.

¹³³ Taonani. Ine ndikufuna kuti ndikufunensi inu. Mmunda wa Edeni, munalibe Malemba analembedwa. Ndiyeno anyamata

awiriwo, Kaini ndi Abele, ndipo iwo awiri onsewo ankafuna kupanga nsembe ndi kuti azikonedwa ndi Mulungu. Pamene iwo anachita zimenezo, Kaini anadzabwera ndipo anadzamanga guwa; Abele anamanga guwa. Chabwino, ngati izo ziri zonse zimene Mulungu amafuna, Mulungu angakhale wosalungama kuti anamutsutsa Kaini. Chabwino. Kenako Kaini anapanga nsembe; chomwechonso anatero Abele. Awiri onsewo anapanga nsembe. Kaini ankapembedza, ndipo chomwechonso Abele ankatero. Kaini anachita chirichonse chimene Abele ankachita.

¹³⁴ Chotero ngati kupita ku tchalitchi, kukhala wa tchalitchi, kupanga nsembe, ndi kupemphera, ndi kamupembedza Mulungu, ndizo zonse zimene Mulungu amuzifuna, ndiye Mulungu angakhale wosalungama kuti anamutsutsa Kaini chifukwa chochita ndendende zimene Iye ananena kuti azichita.

¹³⁵ Koma, inu mwaona, Abele, mwa vumbulutso, iye anadziwa kuti izo sizinali zipatso zimene zinawatulutsa iwo mmunda wa Edeni, monga malingaliro ambiri a chithupithupi amaganizira lero. Abele anabwera ndipo anadzapereka chipatso cha mnthakayo, ndipo Mulungu anazikana izo, koma izo zinawululidwa...ine ndikutanthauza, Kaini anatero, mundikhululukire ine. Kaini anapereka chipatso cha mnthakayo chifukwa iye ankaganiza ndicho chimene chinawatulutsitsa iwo mmunda wa Edeni. Penyani vumbulutso limenero. Penyani kusagwirizana ndi izo. Penyani mmene izo zimapwetekera lero. Koma icho sichinali chipatso chimene chinawatulutsitsa iwo. Eva sanadye ma apulo. Ndithudi. Iye anazindikira bwanji kuti iye anali wamaliseche, ngati kunali kudya apulo? Izo zimakhudzana ndi moyo wogonana. Zimayenera kutero!

¹³⁶ Tsopano, ife timatenga zimenezo ngati phunziro, ndipo ife tatero, timabwerera mmenemo. Iwo alibe Lemba limodzi.

¹³⁷ Ena a iwo amati, “Chabwino, iye anati, ‘Ine ndiri ndi mwana kuchokera kwa Ambuye.’” Inde, bwana. Chomwechonso hule. Mulungu amayenera kupanga moyo wonse.

¹³⁸ Koma iwo ndi moyo wopotozedwa. Tayang’anani chikhalidwe cha mnyamata ameneyo. Iye anali wa atate ake, mdierekezi; udani, umbombo, wakupha. Mukuona?

¹³⁹ Ndiyeno mmene, Abele, pamene iwo...makolo ake mwinamwake anamuza iye kuti—kuti mitengo inali ndi chipatso pa iyo, ndi zina zotero. Koma, izo zinawululidwa kwa Abele. Abele anapita ndipo anakatenga mwanawankhosa, pofuna magazi, kuchotsa moyo. Osati mtengo wazipatso, kubweretsa ma apulo ndi nthochi ndi mapeyala. “Koma Abele, mwa vumbulutso lauzimu,” Ahebri 11, “anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana kwambiri. Mulungu akuchitira umboni za izo, pakuti izo zinaululidwa kwa iye mwa chikhulupiriro.”

140 Pamenepo ndi pamene Mulungu anamangapo Mpingo Wake. “Pakuti thupi ndi mwazi sizinawulule izi kwa iwe.” Sunaphunzire konse Izi ku seminare. Winawake sanaziphunzitse Izi kwa iwe kwinakwake. “Koma Atate Anga amene ali Kumwamba awulula Izi kwa iwe.” Pamenepo, chinthu chonsecho chiri pa vumbulutso, Mpingo wonse, “Pa thanthwe ili la Vumbulutso la Yesu Khristu, Ine ndidzamangapo mpingo wanga.”

141 Iwe ukhoza kutenga chimene abusa akunena. Iwe ukhoza kutenga chimene seminare ikuphunzitsa. Iwe ukhoza kutenga chimene mpingo ukunena. Ndipo izo si zoon, apobe. Iwe ukhoza kukhala ndikuthekerera kofotokozwa ndi kuyankhula bwino. Koma kufikira Mulungu atawulula kwa iwe kuti Yesu Khristu ndi Mwana Wake, ndipo iwe unapulumsidwa kudzera Magazi Ake; pa vumbulutso limenero, kuti, “Iye ndi Mpulumutsi wanga.”

142 “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka.”

143 Chotero ndiye inu mwaona chifukwa chimene Satana amadana kwambiri ndi Bukhu la Chivumbulutso. Chirichonse chimene chawululidwa, vumbulutso lauzimu, Satana amadana nazo izo. Ndi chifukwa chake iye amadana kwambiri ndi utumiki lero. Chifukwa, ndi chiyani icho? Kuwulula kwa Khristu.

144 Mpingo ukamapitirira ndi zipembedzo zake ndi mabungwe aakulu, ndi mauthenga ake amaluwamaluwa pang’ono ndi zina zotero. Iwo akamapitirira nazo, Satana sasunthika ndi zimenezo. Iwo sakhala ndi mavuto. Aliyense amawasisita iwo pa nsana.

145 Pamene ifika nthawi imene Mulungu, kudzera Mzimu Woyera, awululanso Khristu mu Mpingo, ndi mphamvu ndi kuwonetsera kwa machiritso a odwala, ndi kupanga zizindikiro zimene Iye anati zidzawatsatira okhulupirira, ndikufika pochitika, zikatero Satana amadzitembenuza pa bedi lake. Iye amachita chinachake chokhudza izo. Kufikira nthawi imeneyo, Satana samasamala kuti mwajowina kangati tchalitchi. Iye samasamala kuti ndi kangati. Koma pamene Khristu awulula kwa inu kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, ndipo ntchito zimene Iye anachita inu mukumazichitanso; osati ntchito zina, koma ntchito zomwezo.

146 “Iye amene akhulupirira mwa ine. . .” Yohane Woyera 14:7. “Iye amene akhulupirira mwa ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iyenso adzazichita. Kudzachita ntchito zomwezo, ndipo zazikulu kuposa izi.” Chifukwa, Khristu sanalalikire ubatizo wa Mzimu Woyera, izo zikanakhala zazikulu. Iye sanathe kubweretsa izo kwa iwo, chifukwa Mzimu Woyera unali usanaperekedwe. Koma pamene Yesu anadzabwera ndipo anadzapereka nsembe Moyo Wake, ndipo Mzimu Woyera nkubwerera, zitatero iwo akanatha kupereka Moyo Wamuyaya kwa anthu. Ndizo “zazikulu.”

147 Koma zizindikiro ndi zodabwitsa, Yesu ananena momveka, mu Marko 16, “Pitani inu ku dziko lonse lapansi, ndipo mukalalikire uthenga kwa cholengedwa chirichonse.” Mpaka kuti? Ku dziko lonse. Angati? Cholengedwa chirichonse. Bola ngati Uthenga ukulalikidwa, zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ndipo pamene izo zikhala vumbulutso, m’bale, ndiye kuti iwe wayandikira Ufumu. “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzaulaka iwo.”

148 Chifukwa, mwamuna kapena mkazi amene anakhalapo kuseri kwa chipululu icho yekha, monga Mose anachitira, ndipo vumbulutso la Mulungu nkuwonetseredwa kwa iye kudzera mwa Mzimu Woyera, palibe chirichonse chingamugwedeze iye. Iye amangokhala wokhazikika basi ndi wolimba mmene iye angathere.

Satana amadana ndi Vumbulutso. Iye samalikonda ilo konse, nkomwe; zimasokoneza mapulani ake.

149 Khalidwe la Bukhulo limawonetsera kuti Yohane sanalembe ilo. Uko nkulondola. Pakuti izo ndi—izo ndi za ena. . . Izo ndi zolembe zake, koma osati kudzodza kwake. Ndiko kudzodza kwa Mulungu kumene kunalembe Bukhulo. Chabwino.

150 Tiyeni tiwone chimene ilo likunena tsopano.

Wodala ndi iye amene awerenga, ndi iwo amene amvetsera. . . chinenero ichi, ndi kusunga zinthu zimenezo zimene zinalembedwa mmenemo: pakuti nthawi yayandikira.

151 Tsopano, “Nthawi yayandikira.” Chiyani? Pamene Vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu lapangidwa kudziwika kwa mipingo Yake. Ndipo pamene mibadwo ikupitirira, izo zimangowululidwa kwa iwo.

152 Tsopano ife tiri mmusi kumene kumapeto a nthawi yotsiriza, chotero tsopano ife ndithudi tiri kumapeto a dziko. Ife tiri ku chimaliziro cha mbiriyakale ya dziko lapansi. Ndipo sabata ino isanathe, ndipo Mulungu akakhala ndi ife, kutithandizira ife, ife tidzatsimikizira kuti ife tiri ku chimaliziro cha mibadwo ya mpingo. Ife tiri mu Filadel- . . . kapena M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, kumalizitsa kwa mibadwo yonse. Ife tiri ku chimaliziro cha dziko la ndale. Ife tiri ku chimaliziro cha—cha dziko la chirengedwe. Ife tiri ku chimaliziro cha zinthu zonse. Ife tiri ku mapeto a chinthu chachirengedwe chirichonse, kukonzekera kulowa mkati.

153 Ndikubwera tsiku lina, ine ndikukhulupirira ine ndimapita ku Shreveport, kapena ndimabwera kwinakwake. Ine ndinayang’ana. Ine ndinati, “Mitengo ikufa. Udzu ukufa. Maluwa akufa. Ine ndikufa. Dziko likufa. Chirichonse chikufa. Chirichonse mu dziko lino chikufa.” Ife takhala pano mmawa uno, tikufa.

154 Ndithudi kuli dziko kwinakwake, kumene chirichonse sichimafa. Ngati pali kumodzi kumene chirichonse chikufa, pakuyenera kukhala kumodzi kumene chirichonse chikukhala chamoyo. Zimenezo ndi zimene ife tikudikirira, kuti tikafike ku malo kumene kuli...mitengo imaima osafa. Oh, kumene chirichonse ndi chosafa ndipo icho chimaima mu—mu ulemelero wa Mulungu.

155 Tsopano, tsopano, ndime zitatatu zoyambirira zimene ife tinali nazo tsopano, kuyika maziko. Ya 1, “Vumbulutso la Yesu Khristu.” Ya 2, “Linaperekedwa kwa Yohane ndi mngelo.” Ndipo ya 3, ndi, “Wodala, mdalitso kwa iwo amene awerenga, ndipo,” ngati iwe sungathe kuwerenga, “wodala ndi iye amene amvetsera.” Iwe sumatha kuwerenga? Iwe uzingomvetsera Iwo. Ndi zokhazo. “Wodala ndi iye amene awerenga, ndipo,” ngati iwe sumatha kuwerenga, “wodala ndi iye amene amvetsera, pakuti nthawi yayandikira.”

156 Tsopano, taganizani chimene nsonga ya ichi ikutanthauza, ndi kuti, Yohane, wolemba pamenepo, polemba izo, anali... *Uyu* ndi Yohane apa, akungonena “madalitso” ndi zina zotero. Tsopano, chimene ine ndikuganiza kuti icho chinali, mu Chipangano Chakale, wansembe ankaima mmawa ndipo amawerenga Malemba. Osonkhana amamvetsera. Ambiri sankatha kuwerenga. Chotero iye anati, “Wodala ndi iye amene awerenga, ndi iye amene amvetsera.” Mukuona? Wowerengayo ndi womvetsera; mmodzi amene awerenga, ndi kumvetsera, ndi wodala. Chotero ngati iwe utangokhala ndi kumamvetsera izo, iwe ndi wodala. “Wodala ndi iye amene awerenga, ndi iye amene amvetsera, pakuti nthawi yayandikira.”

157 Tsopano, kuyambira 4 mpaka 6 ndi malonje kwa Mpingo. Tsopano ife tikufuna kuti titenge ya 4 ndi ya 6 iyi.

158 Tsopano, ife tisanakhudze izo, ine ndikufuna kuti aliyense ayesere kuganiza mwamphamvu tsopano. Ndi chiyani Chimenecho tsopano? Ndi vumbulutso la Yesu Khristu, pamene Mulungu anachotsa chophimba cha nthawi. *Apa* pali nthawi, kuti Yesu samatha kuwona pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, mibadwo ya mpingo, zimene zikanadzachitika. Chotero, Mulungu anachotsapo chophimbacho, anachikokera icho mmbuyo, ndipo anamulola Yohane kuti ayang’ane mkati ndikuwona chimene m’badwo wa mpingo uliwonse ukanadzachita, ndipo anzilemba izo mu bukhu ndipo anazitumiza izo kwa mipingo isanu ndi iwiri.

159 Ndi chiyani chimenecho? Khristu kuwululidwa mu masiku a Ake—akugwira ntchito Kwake. Ilo ndi lodzaza ndi zochitika, Bukhulo liri. Ndipo ilo ndi—ndi Bukhu la uneneri limene Khristu walipereka, Mulungu anapereka kwa ife kudzera mwa mngelo Wake, linalembedwa ndi Yohane. Ndipo mdalitso kwa aliyense amene ati adzawerenge Ilo kapena kumvetsera Ilo

likuwerengedwa, pakuti—pakuti nthawi yayandikira imene izi zonse ziti zidzakwaniritsidwe.

¹⁶⁰ Ndiri ndi maziko abwino tsopano. Ndipo kumbukirani, ife tikusunga Mpingo mmalingaliro. Uko kumbali ina, Mpingo unayambika; kumbali inayo, mpingo ukukathera. Zochuluka za izo, Lolemba usiku, pamene ife tidzakhudze mibadwo ya mpingo.

Yohane kwa mipingo isanu ndi iwiri imene ili mu Asia: Chisomo chikhale kwa inu, ndi mtendere, kuchokera kwa iye amene ali, . . . amene anali, ndi amene ali nkudza; ndi kuchokera ku Mizimu isanu ndi iwiri imene ili pamaso pa mpando wachifumu.

¹⁶¹ Tsopano ife tikulowa mu zachinsinsi ndi magawo akuya a zophiphiritsa. Ilo likulembedwera kwa mipingo isanu ndi iwiri imene ili mu Asia Minor. Iwo anali—iwo anali . . . Mi—mibadwo, pa nthawi imeneyo, inali yoti idzabwera mtsogolo. Ndipo iye ankaikweza iyo ndi—ndi kumaitamandira iyo chifukwa cha ntchito zake ndi zimene iyo inkachita. Koma, tsopano, izi zikulembedwera kwa mipingo imeneyo, mipingo isanu ndi iwiri imene ili mu Asia Minor.

¹⁶² Tsopano, Asia Minor sanali Asia yense, kontinenti ya Asia. Iyo inangokhala gawo laling’ono. Iwo amati, malo a pafupifupi kukula kwa boma la Pennsylvania, mwaona, kapena chinachake chonga chimenecho, kapena Indiana; basi kamalo kakang’ono kumene mipingo isanu ndi iwiri iyi imakhala. Kumeneko kunali yochuluka kuposa mipingo imeneyo pa nthawiyo. Ndipo, koma, izo zimawulula khalidwe lake. Tsopano ine ndikuwerenga apa chimene ine ndinachipeza kuchokera mu kuwerenga kwanga kwa mbiriyakale ya izo.

¹⁶³ “Ndipo iye ali . . . Wotembereredwa ndi iye amene amva ndipo, kapena, ndipo osamvetsera kwa Iwo.”

¹⁶⁴ Ndipo—ndipo tsopano, izo zikutsikira mmusi mu nthawi ya ndime ya 4 iyi imene ife tikufuna kufotokoza chinachake apa. “Kuchokera kwa Iye amene anali, ndi amene ali, ndi amene ali nkudza, ndipo ali ndi Mizimu isanu ndi iwiri; kuchokera ku Mizimu isanu ndi iwiri imene ili pamaso pa mpando Wake wachifumu.” Tsopano, “Mizimu,” ife tifika kwa iyo mtsogolo.

¹⁶⁵ Tsopano, apa izo zikufotokoza, ngati inu mungazindikire m—mmenemo. Komanso mu ndime ya 7, kapena ndime ya 8, Iye akubweranso ndipo anati, akufotokoza apanso. Tsopano penyani. Mpingo isanu ndi iwiri ikuyankhulidwa. “Kuchokera kwa Iye amene ali, amene anali, ndi amene ali nkudza. Amene anali, nthawi ina; ali tsopano; ndi amene ali nkudza.” Tsopano, Iye akufotokoza apa kufutukuka patatu Kwake, mawonetseredwe ofutukuka patatu Ake a ntchito Yake.

¹⁶⁶ Tsopano ngati inu mungatenge ndime ya 8. Ife tibwera kwa izo, basi mu miniti. Ife titenge ndime ya 8.

Ine ndi Alfa ndi Omega, chiyambi ndi mathero, atero Ambuye, amene ali, . . . amene anali, ndi amene ali nkudza, wa Mphamvuzonse.

167 Tsopano ife tagwira ndime ya 4 ndi ya 6 powonekera, ziwiri zonsezo ndi zofanana. Imodzi, Iye akuti, “Kwa Iye amene anali, amene ali, amene ali nkudza.” Kodi Iye akuyesera kuika chiyani pamaso pa Mpingo? Umulungu Wake. Lero, anthu amayesera kumupanga Iye m—mneneri. Iye ndi woposa mneneri. Ndipo anthu ena amayesera kumupanga Iye Amulungu atatu. Iye sali Amulungu atatu. Iye ndi Mulungu mmodzi amene amakhala mu maudindo atatu, mawonetseredwe atatu a Mulungu yemwe yemweyo.

168 Tsopano, kumbukirani, ili ndi Vumbulutso, “Ndipo aliyense amene amvetsera izo ndipo osasunga maneno a mu bukhu ili, gawo lake lidzachotsedwa kuchokera mu bukhu la moyo.” Yesu sakudziwulula Iyemwini ngati Amulungu atatu, koma Mulungu mmodzi ndi maudindo atatu. Oh! Izo zifika pokoma kwambiri pakapita kanthawi, tikadzafika mu mibadwo ya mpingo imeneyo ndi kuwona pamene iwo anatayira izo. Izo zinapangitsa kugawikana kwakukulu ku Nicene Council. Awiri onsewo anapita mu mathero akuya.

169 Ndipo iwo achita chinthu chomwe chomwecho mu masiku otsiriza ano kenanso, chimodzimodzi monga a pre-Nicene Council panonso, chifukwa padzakhala inanso. Motsimikiza basi monga ine ndaima pano, mipingo ya Katolika ndi Chiprotestanti idzalumikiza chinachake pamodzi, kapena idzagwirizana wina ndi mzake. Tamuwonani alikibishopu waku Canterbury uko tsopano. Zonse izo zikuwunjikana pamodzi. Ndipo palibepo kuphunzitsa kwa Mulungu wapatatu mu Baibulo. Alipo Mulungu mmodzi.

170 Ndipo izo zikuwululidwa apa mu Bukhu la Chivumbulutso, kuti nsonga zonse za Malemba zikathe kutsimikiziridwa apa, ndipo Khristu anaika chisindikizo Chake pa izo. Ichi ndi Chimenecho. Ngati aliyense adzachotsera kapena adzawonjezera, zomwezo zidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo, kwa iye. Chotero muzifikire izi osati mwaumbombo, muzifikire izi ndi mtima wotseguka ndi malingaliro otseguka.

171 Tsopano, ku Nicene Council, iwo anafika ku maganizo aakulu awiri. Pa . . . Oh, ambiri a iwo mu tsiku limenelo a atate a mpingo woyambirira, iwo anali ndi kuwona kuwiri kopitirira muyezo. Mmodzi wa iwo anali wa Mulungu wapatatu, wautatu. Ndipo mmodzi winayo anali wa—wa Mulungu mmodzi. Ndipo iwo awiri onsewo anafika pokhalapo ndipo anatuluka kupita pa nthambi ziwiri zolunjika, kunja monga *choncho*. Utatuwo unadzakhala malo a munthu wa milungu itatu. Aumodzi anadzakhala okhulupirira mmodzi, basi kumangopitiriza kulakwitsa monga chimodzi chinacho chinali. Chotero awiri

onsewo anapita pa nthambi, koma *Umu* kumene mukuwulula Choonadi.

172 Yesu sakanakhala Atate wa Iye mwini. Zosatheka, ngati Iye akanakhala ndi atate kunja kwa Mzimu Woyera, ndiye Iye akanakhala mwana wapathengo. Ndipo osati. . . Mzimu Woyera unamupangitsa Iye kukhala ndi pakati, ndipo Iye anati Mulungu anali Atate Ake. Chotero Mzimu Woyera ndi Mulungu. . . Ameneyo ndi Mateyu 1:18. Ngati. . . Mzimu Woyera ndi Mulungu akuyenera kukhala Munthu yemweyo, kapena Iye anali ndi atate awiri. Ndipo Iye anatchedwa *Emmanuele*, chimene chiri, “Mulungu nafe.” Iye ankadzinenera, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kuti Iye ndi Atate anali Mmodzi.

173 Ine ndiri nawo Malemba onse atalembedwa apa kuchitira kuti inu mukhoze kupeza, ngati ife tikanakhala ndi ili—funso ili, kapena chinachake.

174 Tsopano, pamene Iye anawonetseredwa kuno, ngati udindo wofutukuka patatu wa umunthu Wake, “Iye amene anali, Iye amene ali, Iye amene adzaza, Wamphamvuzonse,” tsopano, kulibeko Amulungu atatu pamenepo; alipo Mulungu mmodzi.

175 Ndipo mu Nicene Council, kuchita izi, kuti achite izi, iwo ankayenera kuti atenge utatu, chifukwa mu dziko la Chiroma iwo amakhala ndi milungu yambiri. Iwo ankapemphera kwa makolo awo akufa. Ine ndiri nayo mbiriyakale pomwe pano pamene ife tikhoza kuwerenga izo mobwereza. Mukuona? Iwo ankapemphera kwa makolo awo akufa. Ndi chifukwa chake ali ndi Cecelia Woyera, ndi Marcus Woyera, ndi woyera, woyera, woyera, woyera.

176 Pamene, Mtumwi Petro anati, “Palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi anthu, koma Munthu ameneyo Khristu Yesu.” Mmodzi.

177 Iwo ankayenera kukhala ndi mulungu wa utatu. Chotero, iwo—iwo anali ndi Jupiter, Mars, Venus. “Ndipo izo sizinali zolondola, kuziika zonsezo pa Mulungu mmodzi,” chotero iwo anangozigawaniza izo, ndipo anapanga maudindo ofutukuka patatu a Mulungu kuti akhale Amulungu atatu osiyanasiyana.

178 Koma Iye akunena momveka bwino apa, mu Chivumbulutso, Yemwe Iye ali. “Ine ndine Iye amene anali, Iye amene ali, ndi Iye amene ali nkudza, Wamphamvuzonse.” Ife tizipeza Izo patsogolo pang’ono apa, Iye anati, “Ine ndi Alfa ndi Omega,” A mpaka Z, zonsezo, zilembo za Chigriki zimenezo. “Kakombo wa Mchigwa, Rozi la Sharon; Atate, Mwana, Mzimu Woyera; Iye amene anali, amene ali, ndipo adzaza; Muzu ndi Mphukira ya Davide.” Iye ndi Mulungu, Mulungu. “Popa-. . .” Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana, chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi, anawonedwa ndi Angelo, anakhululupiridwa mdziko, analandiridwa mu Ulemelero.” Mulungu! Osati munthu wachitatu kapena mneneri,

koma Mulungu Mwiniwake, kuwonetseredwa mu mawonekedwe a thupi. Tsopano, ili ndi vumbulutso, kumbukirani.

179 Tsopano, Mulungu, pachiyambi, anali Yehova wamkulu amene ankakhala mu Lawi la Moto, ankapachikika pamwamba pa Israeli, ndipo ankawatsogolera iwo. Ameneyo anali Mulungu, Mngelo wa Pangano. Anadzatsika pansi pa phiri; phiri lonse linagwidwa ndi Moto. Moto kumawuluka kuchokera pa phiri, ndipo unalemba Malamulo Khumi. Iye ankatchedwa “Utate wa Mulungu,” kwa ana Ake, mtundu Wake wosankhidwa wa anthu, Ayuda.

180 Kenako Mulungu yemwe yemweyo anadzawonetseredwa mu thupi lobadwa mwa namwali limene Iye analilenga mu chiberekero cha Maria, ndipo anadzakhala moyo ndi kudzakhala mkachisi ndipo anadzamufunzulira hema Wake, monga izo zinachitikira, pakati pa anthu. Ndipo Mulungu yemwe yemweyo anadzapangidwa thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Baibulo linanena chomwecho. “Mulungu anali mwa Khristu.” Thupilo linali Yesu. Yesu, “Mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mthupi.” Simungathe kumupanga Iye anthu atatu, tsopano. Osamabatiza kwa Amulungu atatu. Alipo Mulungu mmodzi. Mukuona? Mulungu Mmodzi. Tsopano, Mulungu yemweyo uyu anadzasandulika thupi.

Iye anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo Ine ndikupita kwa Mulungu.”

181 Iye atachoka pa dziko lapansi, itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiukitsiro, ndi kukwera mmwamba, Paulo anakumana naye Iye panjira akupita ku Damasiko, pamene iye ankatchedwabe “Saulo.” Ndipo Liwu linabwera, ndipo linati, “Saulo, Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Iye anati, “Inu ndinu Ndani?”

Iye anati, “Ine ndi Yesu.”

182 Ndipo Iye anali Lawi la Moto, Kuwala kumene kunapangitsa khungu maso a mtumwi. Iye anali atabwereranso. Yesu yemweyo anali atabwereranso kwa Mulungu, Atate, kachiwiri. Ndi chifukwa chake Iye ananena apa, “Ndine Wamphamvuzonse,” mu mawonekedwe omwewo amene Iye analimo Iye asanasandulike thupi; ndi thupi Lake limene Iye ankakhalamo, linkatchedwa Yesu, Munthu amene ife timamudziwa, Yesu.

183 Tsopano, chimodzimodzi monga ambiri a anthu aumodzi inu mumabatiza mu, “Dzina la Yesu,” inu mukulakwitsa. Alipo mazana a Yesu mu dziko lero, koma alipo Ambuye Yesu Khristu mmodzi yekha. Iye anabadwa ali Khristu. A Yesu ambiri. Ine ndakumanapo ndi ambiri a iwo. Koma alipo Ambuye Yesu Khristu mmodzi, Iye ndi Mulungu.

184 Ndipo Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera si *maina*. Iwo ndi maudindo amene amapita kwa Dzina limodzi. Iwo amabatiza, “Dzina la ‘Atate, Mwana, Mzimu Woyera.’” *Atate* si dzina, ndipo *Mwana* si dzina, ndipo *Mzimu Woyera* si dzina. Ndi udindo, monga “munthu.” Ndizo zimene izo ziri, Mzimu Woyera. Munthu. . . Kapena, mzimu, Mzimu Woyera. Ndiye mukati, “Mu dzina la ‘Atate.’” Tayang’anani pa atate, ndi ana a ana anu. Tayang’anani pa anthu muno. Mukuona? “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” si dzinalo. Iwo ndi udindo umene umapita kwa Dzina la “Ambuye Yesu Khristu.”

185 Umo ndi mmene Mpingo wa atumwi unkabatizira, pachiyambi. Ndipo ine ndimufunsa aliyense kuti andipatse mutu umodzi wa Lemba, kapena nthawi imodzi mu mbiriyakale, pamene aliyense anabatizidwapo mu Mpingo wa Chikhristu mwanjira ina iliyonse kusiyana ndi mu. . .koma mu Dzina la “Yesu Khristu” kufikira pamene mpingo wa Katolika unadzapangidwa. Ndipo iwo anadzatenga “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” kukhala kachikhulupiriro. Tsopano ibweretseni mbiriyakale yanu, ena, azambiriyakale. Eya. Kulibeka chinthu choterocho. Pambuyo pa 304 A.D., 304, panadzabwera ubatizo wa patatu wa Mulungu wa patatu, “Mulungu Atate, Mulungu Mwana, Mulungu Mzimu Woyera.” Ichu ndi chikunja.

186 Sabata ino isanathe, ine ndiwerenga izo kuchokera mu mabukhu ndi kukuwonetsani inu mwa Baibulo. Ife tikuyankhula mmawa uno pa Chivumbulutso, ndi kutsimikizira kumene izo zinadzabweramo, ndi mmene zinayambira kukhalapo. Kubwerera ku Choonadi, m’bale! Ife tiri mu tsiku lotsiriza.

187 Dikirani mpaka ife tidzatenge mpingo wa Efeso uwo ndi kuwufanizitsa ndi wa Laodikaya, ndi kuyang’ana chimene chinachitika pakati pawo. Inu mudzawona mmene chinthu chimenecho chinadzakwawira mmenemo. Kubwera mu m’badwo wa Lutera, anati, “Uli nalo dzina lakuti iwe ‘uli moyo,’ koma ndiwe wakufa.” Mawu kumene akuti *Sarde* amatanthauza “wakufa.” Iwo anazitaya izo mu zaka ffitini handiredi za M’badwo wa Mdima. Umodzi uliwonse wa mipingo imeneyo unkasunga zimenezo kufikira nthawi imeneyo. Ndiye pamene iwo anadzakhala ndi Nicene Council mu 606, ndiyeno nkudzafafaniza Dzina limenero nadzapanga Milungu itatu kuchokera mwa Ilo.

188 Iye ananena apa, “Ine ndine Iye amene anali, Iye amene ali, ndipo adzabwera, Wamphamvuzonse.” Ndithudi.

189 Iye anali Umunthu wofutukuka patatu pa dziko lapansi. Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali Munthu wofutukuka patatu. Pa dziko lapansi, Iye anali Mneneri. Iye alinso Kumwamba, Wansembe. Ndipo pamene Iye azidzabwereranso ku dziko lapansi, Iye adzakhala Mfumu. Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu. Iye amene anali, amene ali, ndipo adzabwera. “Iye

amene anali,” anali Yesu, mneneri. “Iye amene anali tsopano,” ndi Wansembe, akupanga nsembe zauzimu, Wansembe Wamkulu yemwe akhoza kukhudzidwa ndi zomverera za zofooka zathu, ndipo akudziwonetsera Iyemwini ndi kudzitsimikizira kuti Iye ali pakati pathu. Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu, koma Mulungu Mmodzi.

¹⁹⁰ Pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali Mneneri, Mawu. “Mboni yokhulupirika,” Baibulo limadzamutichula Iye, mtsogolo pang’ono. Mboni yokhulupirika, ndi mneneri. Iye anali Wansembe, ndipo pamene. . . Iye ali Wansembe tsopano, ndipo pamene Iye adzabwera, Iye adzakhala Mfumu.

¹⁹¹ Ngati mukathana nazo, mukawerenge Chivumbulutso 15:3, inu mukhoza kukawona mu Chivumbulutso 15:3. Tiyeni titembenuzire apa ndipo tiwone chimene Iye. . . ngati Iye ati adzakhale Mfumu, ngati Iye adzakhale Mfumu pamene Iye akubwera. Tsopano ife tikupita ku Chivumbulutso, mutu wa 15 ndipo ndi—ndime ya 3.

Ndipo iwo anaimba nyimbo ya Mose wantchito wa Mulungu, ndi nyimbo ya Mwanawankhosa, kumati, Zazikulu ndi zodabwitsa ndi ntchito zanu, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse; zolungama ndi zooni ndi njira zanu, inu Mfumu ya oyera.

¹⁹² Kodi Iye anali chiyani pa dziko lapansi? Mneneri. Anthu anadziwa bwanji kuti Iye anali Mneneri? Iye anachita chizindikiro cha Mesiya, amene anali Mneneri. Oh, lodala likhale Dzina la Ambuye! Kodi iwo anamuphonya bwanji Iye? Chifukwa iwo anali kuyembekezera chinthu chinachake. Ndipo Iye anadzachita chizindikiro cha Mesiya, ndipo iwo sanathe kumva izo. Iye anali Mneneri.

¹⁹³ Mose anati, “Ambuye Mulungu wanu adzadzutsa Mneneri wonga ine. Izo zidzachitika ngati iwo sadzamumvera Mneneri uyu, iwo adzadulidwa kuchoka pakati pa anthu.”

¹⁹⁴ Iye anali Mneneri pa dziko lapansi, tsopano, chifukwa Iye anali chiyani? “Mboni yokhulupirika ya Mawu a Mulungu.” Ameni. Iye anali Mawu a Mulungu akuwonetseredwa.

¹⁹⁵ Yohane Woyera, mutu wa 1.

Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.

Ndipo Mawu anasandulika thupi, ndipo anadzakhala pakati pathu, . . .

¹⁹⁶ Iye anali mboni yooni ndi yokhulupirika ya Mawu a Mulungu a Muyaya. Iye anali Mawu, anali Mawu a Mulungu. Ndipo, pokhala Mawu, Iye anali Mneneri. Pakuti Mawu a Mulungu amayenderera kudutsa mwa Iye. Iye anali woti adzanene Chinthu chokhacho. “Ine sindingachite kalikonse mwa Inemwini, koma chimene Atate andiwonetsera Ine kuti ndichite.

Si Ine amene ndikuchita ntchitozo. Koma Atate amene akukhala mwa Ine, Iye akuchita ntchitozo. Ine ndi Atate Anga tiri Mmodzi. Atate Anga ali mwa Ine,” anatero Yesu, Munthuyo, Kachisiyo.

¹⁹⁷ Mulungu ali nawo maudindo ambiri: Yehova, Yehova-Yire, -Rapha, -Manase. Oh, ambiri! Iye ali ndi maina apasanu ndi pawiri a chiwombolo. Iye ali ndi maudindo ambiri: Rozi la Sharon, Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi ya Mmawa; Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Zonse zimenezo. Koma Iye ali ndi Dzina limodzi la umunthu. Mulungu anali ndi Dzina limodzi lokha, ndipo limenelo linali “Ambuye Yesu Khristu.”

¹⁹⁸ Pamene Iye anabadwa, Khristu, Ambuye. Masiku eyiti mtsogolo, Mzimu Woyera unamutcha Dzina Lake “Yesu.” Amayi Ake anamupititsa Iye ku mdulidwe, ndipo anakamutcha Iye “Yesu.” Iye anabadwa ali Khristu.

¹⁹⁹ Monga, ine ndinabadwa ndiri Branham. Ine ndinali Branham pamene ine ndinkabadwa, ndipo ndinapatsidwa dzina la “William.”

²⁰⁰ Ameni. Ndipo Iye anabadwa Khristu, Mpulumutsi. Ndipo pamene Iye anali masiku eyiti akubadwa, Iye anapatsidwa Dzina lakuti “Yesu.” Ndipo Iye anali Ambuye wa Ulemelero, akuwonetseredwa. Chotero, Iye ndi Ambuye Yesu Khristu, Mulungu wa Ulemelero akuwonetseredwa pakati pathu. Oh, ndi Uyo pamenepo!

²⁰¹ Pa dziko lapansi, Iye anali Mneneri. Mu Ulemelero, Iye ndi Wansembe. Akamadzabwera, Iye adzakhala Mfumu. Oh! Ine ndikuzikonda zimenezo.

Mneneri, “Mboni yokhulupirika ya Mawu.”

Wansembe, “Ndi Magazi Ake Omwe pamaso pa Mulungu.”

Mfumu, “Mfumu ya oyera.” Osati mfumu ya dziko lapansi, tsopano. Iye ndi Mfumu ya oyera. Ife tiri nawo mafumu a dziko lapansi pamwamba pa anthu amenewo. Koma ife tiri nayo Mfumu, nafeso, ndi Ufumu. Ndi chifukwa chake ife timachita mosiyana.

²⁰² Monga ine ndinanenera osati kale kwambiri, zokhudza mkazi wanga, ife timapita ku sitolo kumtunda kuno ndipo ife tinawona chozizwitsa, pafupifupi. Iyo inali nthawi yachirimwe, mzimayi anali atavala diresi. Ndipo ine ndinati, “Icho ndi chinthu chachirendo.” Ine ndinati, “Ngati ine ndikanakhala ndi kamera, ine ndikanamujambula chithunzi donayo.” Mukuona? Chifukwa ife. . . Uyo anali mkazi woyamba amene ife tinamuwonapo atavala siketi, inu mukudziwa, atavala mmene dona amayenera kukhalira, akazi onse.

²⁰³ Iye anati, “Chabwino, nchifukwa chiyani ziri chomwecho, Bill, kuti anthu athu amavala, kodi ndiye kuti ife tiri—ife titalamulidwa?”

204 Ine ndinati, “Si anthu athu. Ndi anthu a Mulungu. Anthu a Mulungu, amafunikira chiyero.”

Anati, “Chabwino, kodi iwo sapita ku tchalitchi?”

205 Ine ndinati, “Pali dona pomwe *apo*, amene amaimba mu kwaya pa mpingo winawake kuno.”

“Chabwino, ndiye, chifukwa chiyani zimenezo?”

206 Ine ndinati, “Chifukwa sanaphunzitsidwe mosiyana mulimonse.” Ndizo kulondola ndendende.

207 Ndiwo mpingo wachithupithupi uwo, ife tilowa mu zimenezo sabata ino; Mpingo wauzimu, mpingo wachithupithupi. Iwo onse akubwerera mmbuyo kubwerera kwa manthu wa mpingo, monga Baibulo linanenera, mu Chivumbulutso 17, iwo akanadzachita izo. Iwo akubwereranso kumeneko pakali pano, onse a iwo, akuchita monga chomwecho, akupanga bungwe. “Chabwino, ndife *wakuti*. . .Ife timachita bungwe. Ndife *ichi* ndipo ndife *icho*.” Izo sizinali chomwecho pachiyambi. Kutenga mphamvu yonse kuichotsa mu mpingo ndi kukaiyika iyo pa bishopu kapena papa. Mulungu amakhala mu Mpingo Wake, pakati pa anthu Ake, kumadziwonetsera Iyemwini kudzera mwa anthu wamba ndi paliponse, tsopano. Koma mu tsiku lino. . .

Iye anati, “Chabwino, kodi sindife Achimerika?”

208 Ine ndinati, “Ayi. Ife timakhala kuno, koma ife sindife Achimerika. Ife ndi Akhristu. Ufumu wathu ndi wa Kumwamba.”

209 Ndipo ngati miyoyo yathu imachokera kumwamba Uko, ndiye ife tizichita monga chomwecho. Chifukwa, ife tinachokera. . .Moyo Wathu ndi wochokera ku Malo oyera. Iwo umawoneka mosiyana. Iwo umavala mosiyana. Akazi kumwamba Uko amakhala ndi tsitsi lalitali. Ndipo iwo samazipakapaka utoto pa nkhope zawo. Ndipo—ndipo iwo samavala makabudula. Iwo—iwo amavala masiketi, ndi miinjira yaitali ndi madiresi. Ndipo iwo amakhala ndi tsitsi lalitali, ndi zinthu. Chotero—chikhalidwe cha izo, chochokera kumwamba Uko, chimanyezimiritsidwa pa ife.

210 Amuna samasuta, kutukwana, kunama, kuba. Iwo amabwera, mizimu yawo, imachokera ku Malo oyera, zimawapangitsa iwo kuti azichita mwachiyero, amazindikirana wina ndi mzake ngati abale. Uh-huh. Ndi zimenezotu.

211 Ndife a Ufumu, ndipo ife tiri naye Mfumu. Ndipo Iye ndi Mfumu ya oyera. Ndipo mawu akuti *woyera* amachokera ku mawu a “oyeretsedwa awo.” Ndiye pamene munthu wayeretsedwa, Khristu, Mzimu Woyera umasunthira mu mtima ndipo amadzakhala Mfumu pa iwo. Oh, mai! Zimenezo zikuyenera kufika mkati. Oh! Pamene chida choyeretsedwa cha Mulungu. . .Khristu, Mfumu, Mzimu Woyera, asunthira

mkati. Ndipo Iye...Mfumu amakhala ndi ulamuliro Wake. Amen. Ndipo umunthu wanu wonse umalamuliridwa ndi Mfumu ya oyera. Ufumu! Ufumu uliwonse pa dziko lapansi udzagwedzedwa, udzang'ambidwira pansu ndi mphamvu ya atomu. Koma Baibulo limati, "Ife tidzalandira Ufumu umene sungathe kusunthidwa." Amen. Ndi Ameneyo apo, Mfumu ya oyera.

212 Ine ndikufuna kuti inu muzindikire ziphiphiritso za Khristu, aponso, mu Baibulo ndi apa pa dziko lapansi. Pa dziko lapansi, Iye anali Mneneri. Inu mukukhulupirira zimenezo? Mneneri ndi Mawu. Ife tikudziwa zimenezo. Mawu akuti *mneneri* amatanthauza "wotanthauzira Wauzimu wa Mawu." Mawu Auzimu analembedwa, ndipo mneneri amakhala ndi Mzimu Wauzimu wa Mulungu mkati mwa iye. Ndipo, inu mukudziwa, mneneri mu Chipangano Chakale ankatchedwa "mulungu." Ndi angati amadziwa zimenezo?

213 Yesu anati, "Ngati iwo ankawatcha iwo milungu... Kodi izi sizinalembedwe mu lamulo lanu, iwo ali... 'Inu ndi milungu?' Ndipo ngati iwo ankawatcha iwo 'milungu,' omwe Mawu a Mulungu ankabwerako, mneneriyo, kodi inu munditsutsa Ine bwanji pamene Ine ndikuti ndine Mwana wa Mulungu?"

214 Chifukwa, iye ankatchedwa "mulungu," chifukwa iye ankanyamula mkati mwa iye Mawu a Mulungu, PAKUTI ATERO AMBUYE. Chotero, mawu akuti *mneneri* amatanthauza, "kwake—kutanthauzira kwake sikoyenera kusakanizidwa." Mukuona? Ngati Mulungu...Iye akuti, "Ngati patakhalammodzi pakati panu, yemwe ali wauzimu, kapena mneneri, Ine Ambuye ndiziyankhula ndi iyeyo. Chimene iye anena chikadzachitika, ndiye mudzamumvere iyeyo, chifukwa Ine ndiri ndi iye. Koma ngati izo sizichitika, ndiye musamumvere iye; Ine sindinamutume iye." Ndiyo njira imene mungadziwire zimenezo. Ndiyeno, inu mukuona, Kutanthauzira Kwauzimu kwa Mawu kukuyenera kugwirizana ndi vumbulutso lotsiriza ili kwa mpingo.

215 Iye ndi Mulungu, Wamphamvuzonse. Pa dziko lapansi, Iye anali Mneneri, imene ili mphungu. Ndi angati amene amadziwa kuti mneneri amatengedwa ngati mphungu?

216 Mphungu ndi mbalame yamphamvu kwambiri imene ife tiri nayo, yamphamvu kwambiri. Ena a mapiko ake amatambasuka mafiti fortini, kuchokera pa nsonga mpaka nsonga. Iyo ikhoza kuwuluka mmwamba kwambiri mwakuti ngati mbalame ina iliyonse itayesera kumutsatira iye, iyo ikhoza kunyenyeke, nthenga zikhoza kuthothokapo kuchoka pa iyo ndipo iyo ikhoza kukhadzuka. Chifukwa chiyani? Iyo inamangidwa mwapadera. Ndipo zimaichitira ubwino wanji iyo kukwera mmwamba chomwecho ngati iyo siingathe kuwona chimene iyo

ikuchita pamene iyo ili pamwamba apo? Kukamba za diso la khwangwala? Inu mukuyenera mudzawone diso la mphungu.

²¹⁷ Khwangwala akhoza, akhoza kuiwona nkhuku. Uko nkulondola. Ndiro limene liri vuto ndi a khwangwala enawa lero. Uh-huh. Koma, ine ndikukuuzani inu, mphungu imapita chomwecho, ngati khwangwala ayesera kumutsatira iye, iye akhoza kukafa. Iye akhoza kukabanikako. Iye sangakhoze kufika mu madera amenewo amene mphungu imakafikako.

²¹⁸ Ndiyeno iye ali ndi diso, limene iye akhoza kuwona patali, pamene iye wafika pamwamba pamenepo. Chotero ndicho chifukwa chake Mulungu amawatcha *aneneri* Ake, “mphungu.” Iye amafika pamwamba pamenepo, ndipo iye ndi mphungu. Iye akhoza kuwona, patali kwambiri.

²¹⁹ Ndipo Khristu, pa dziko lapansi, anali Mphungu. Pamene Iye anafa, Iye anali Wansembe, chotero izo zinamupanga Iye kukhala Mwanawankhosa. Nkulondola uko? Ndipo pamene Iye azidzabwereranso, Iye ndi Mfumu, chotero Iye adzakhala Mkango, ameni, Mkango wa fuko la Yuda. Ameni. Iye ndi Mphungu, Mwanawankhosa, ndi Mkango; ameni; Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera; Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu; Iye amene anali, amene ali, ndipo adzaza; Wamphamvuzonse; Alfa ndi Omega, kuyambira pachiyambi mpaka kumapeto, Mulungu Wamuyaya.

²²⁰ Ndikufuna ndikufunsi inu, ena a inu anthu ofunikira Akatolika, amene mumamutcha iye, “Umwana Wamuyaya wa Mulungu; Mulungu, umwana Wamuyaya wa Yesu Khristu ndi Mulungu.” Inu munganene bwanji mawu oterowo? Ndine mbuli, ya maphunziro a sitandade-seveni, koma ine ndimadziwa bwino kuposa zimenezo. Mawu akuti mwana amayenera kukhala ndi chiyambi. Chotero Iye angakhale bwanji Wamuyaya ndipo nkukhala mwana? Umuyaya sumakhala ndi chiyambi kapena mapeto. Chotero, Iye sangathe kukhala mwana, mwana Wamuyaya, ndiyeno nkukhala ndi chiyambi, chifukwa kulibeko chinthu chotero ngati mwana Wamuyaya. Mwana anali ndi chiyambi, chotero iye sangakhale Wamuyaya.

²²¹ Inu mwaona, Iye ndi Mulungu Wamuyaya, osati mwana Wamuyaya. Ulemelero! Wamphamvuzonse, Yehova-yire, Yehova-rapha, anawonetseredwa mu thupi, “Mwa Iye munkakhala chidzalo cha Umulungu mthupi.”

²²² Ndipo pa Tsiku la Pentekoste, pamene Lawi la Moto limenero linadzatsika pa anthu, kodi inu munazindikira, Ilo linadzigawaniza Lokha? Ndipo malirime a Moto anadzakhala pa aliyense wa iwo. Moto, monga malirime, anadzakhala pa mmodzi aliyense. Mulungu amachita chiyani? Amadzigawaniza Iyemwini mu Mpingo, pakati pa mmodzi aliyense, kuwapatsa akazi, amuna, ndi onse a iwo; zinali zidutswa za Mzimu Wake, kuzigawaniza Iyemwini pakati pa Mpingo Wake.

223 Munthu angabwere bwanji ndikumati, “Munthu woyera ndi papa. Munthu woyera ndi bishopu”? Munthu Woyera ndi Khristu, Mzimu Woyera mwa ife. Inu munganene bwanji kuti anthu wamba alibe mawu oti anene? Mmodzi aliyense wa inu ali ndi kanthu koti anene. Mmodzi aliyense wa inu ali ndi ntchito yoti achite. Mmodzi aliyense wa inu akuyenera kunyamula Uthenga. Ulemelero!

224 Mzimu Woyera unadzigawaniza Wokha pa Tsiku la Pentekoste. Mulungu, kudzigawaniza Iyemwini. “Tsiku limenero inu muzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, Atate mwa Ine; Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.”

225 “Tsiku limenelo,” Mzimu Woyera, “pa onse, mwa onse, kudutsa mwa onse.” Ameni. Ndi zimenezotu pamenepo. Mzimu Woyera uli ndi udindo woyenda kupita kulikonse kumene Iye akufuna kupita, pa aliyense amene Iye akumufuna. Iwe sumayenera kutenga chimene bishopu wina kapena wansembe wina akunena. Iyeyo ndi Wansembe wathu yekhayo, kulondola, Wansembe Wamkulu. Tsopano: Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu.

226 Tsopano:

Ndipo... Yesu Khristu, yemwe ali mboni yokhulupirika, . . . woyamba kubadwa wa akufa, . . . (Ife tilowa mu zimenezo.) . . . ndi kalonga wa mafumu apa dziko lapansi. Kwa iye amene anatikonda ife, ndipo anatitsuka ife kuchoka ku machimo athu mu magazi ake omwe,

227 Mawu akuti *kutsukidwa* pamenepo, kwenikweni, mu Chigriki, amatanthauza “kumasula.” Iye anatimasula ife kuchoka ku athu. . . Ife tinamangidwa ku dziko lapansi, ndi tchimo lathu. Ife sitimatha kuwona, sitimatha kumva, tinalibe chidziwitso cha Kumwamba kapena kalikonse. Koma pamene Magazi anadzabwera pansu, Iwo anadzadula chingwecho ndipo ife tinamasulidwa. Oh!

228 Ine ndinawerenga nkhani nthawi ina, ndi. . . ikhoza kukwanirana bwino apa. Mlimi anagwira khwangwala ndipo iye anamumangirira iye. Ndipo iye anati, “Ine ndiwaphunzitsa akhwangwala enawo phunziro.” Chotero iye anamumangirira khwangwala wokalambayo, ndipo pa mwendo, ndi chingwe, ndipo kanthu kokalamba kosauka kanatsala pang’ono kufa ndi njala. Iye anali atafooka kwambiri, iye amalephera kuti aziyendayenda.

229 Ndi zimene, ena a mabungwe awa ndi matchalitchi, awamangirira anthu pansu. “Basi osakwanitsa! Chabwino, iwo ukhoza kungopita kufika *apa* basi. Masiku a zozizwitsa anapita.” Eya. Iwe unamangidwa basi. Ndizo zonse. “Palibepo chinthu chotero ngati Mzimu Woyera. Iye samayankhula ndi malirime monga Iye ankachitira.”

²³⁰ Iye ndi Mulungu. “Iye ali basi yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” Ahebr 13:8, kumakhala moyo mmipingo yonse. Ife tifika kwa izo tikatha kukhazikitsa izi mmawa uno. Mukuona? Iye ndi Mulungu, amene amakhala moyo mu m’badwo wa mpingo uliwonse. Iye adzakhala moyo mu m’badwo wa mpingo uliwonse, ndipo adzakhala moyo mwa anthu Ake monga. . .kwa Muyaya. Pakuti ife tiri nawo tsopano, mkati mwathu, Moyo Wamuyaya.

²³¹ Chotero, chipembedzo ichi chinali chitamumangirira iye pansu, mwaona, “Chabwino, masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu chotero ngati machiritso Auzimu.” Munthu wokalamba wosaukayo anayenda motsimpina mpaka kuti iye anali wosauka kwambiri iye amayenda movutikira.

²³² Ndipo tsiku lina panali munthu wabwino amene anadzabwera, ndipo iye anati, “Inu mukudziwa, khwangwala wosauka wokalamba uyo, ine ndikumumvera iye chisoni kwambiri. Kuwonjezera apo, mwinamwake akhoza kukhala kuti akudya chimanga chake, koma ndiyo njira yokhayo imene iye angakhalire moyo. Iye akuyenera kukhala ndi chinachake choti azidya. Chotero iye sakudziwa kusiyana kulikonse, iye basi ali kunja kumeneko akudya chimanga. Chotero ngati. . .” Kenako iye anatenga wake. . .ndipo anatenga mpeni wake ndi kumudula khwangwala wokalambayo.

²³³ Ndipo inu mukudziwa, apa pakubwera akhwangwala enawo, akubwera pamenepo, anati, “Bwera kuno, Johnny Crow. Tiye tizipita Kummwera. Nyengo yozizira ikubwera.”

²³⁴ Inu mukudziwa chiyani? Khwangwala ameneyo azingopita utali wa momwe iye ankapitira kunja uko. Iye anati, “Ine sindingathe kuchita zimenezo. Sizimenezo ayi, izo si za ife basi mu tsiku lino. Ife—ife basi sitingakhoze kuchita zimenezo.” Mukuona? Iye anali atamangiriridwa nthawi yaitali, kufikira kuti amaganiza kuti iye anali womangidwabe. Mukuona?

²³⁵ Ndipo ndi mmene zakhallira ndi anthu ambiri, inu mwamangidwira pansu ndi tizikhulupiriro ndi zipembedzo, kuchokera kwa mayi wakale hule kumbuyo uko, kumakuuzani inu, kuti, “Yesu Khristu sali yemweyo. Ndipo kulibeko chinthu chonga ngati machiritso. Kulibeko ubatizo wa Mzimu Woyera. Kulibeko chirichonse cha zinthu ngati izi.” Kumayesera kuti awawuze iwo. Inu mwamangidwa kwa nthawi yaitali mpaka inu mumaganizabe kuti ndinu womangidwa.

²³⁶ Munthu wabwinoyo, Khristu, anapereka Magazi Ake kuti Iye akathe kutitsuka ife ndi kutimasula ife ku tchimo lathu. Kodi tchimo ndi chiyani? Ine ndimufunsa aliyense kuti andiuzene. Tchimo ndi chiyani? *Tchimo* ndi “kusakhulupirira.” Uko nkulondola. “Iye amene sakhulupirira waweruzidwa kale.”

²³⁷ Ndipo tchimo lanu ndi chinthu chanu chokhacho chimene chimakulepheretsani inu kukhala womasuka. Ndi chifukwa

chakuti Mulungu anakudulani inu kukusakhulupirira kwanu, koma ndinu womangidwa kwambiri ndi tizikhulupiriro kufikira kuti inu mumaganizabe kuti ndinu womangidwa. Basi kumangofa ndi njala, mwaona, kumangozungulira pamenepo, “Ndine wa Presbateria. Ndine wa Methodisti. Ndine wa Baptisti. Iwo amandiuza ine (Ndine wa Mpingo wa Khristu), ‘Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu choterocho.’”

²³⁸ Iwe khwangwala wosauka wanjala! Bwanji sukungobwera nafe mmawa uno? Bwanji sukungowulukira kutali? Aleluya! “Dzuka ndi mapiko a mmawa, ndipo uwulukire kutali ku Dzuwa la Chirungamo, ndi machiritso mu mapiko Ake.” Ameni. Ndi zimenezotu. Ndi zimenezo, m’bale, mlongo. Oh! “Iye amene Mwana wamudula kukhala mfulu, ndi mfulu ndithudi.” Inde, bwana!

²³⁹ “Chabwino, abusa anga...” Palibe zokhudza zimenezo. Baibulo linati, “Ndinu mfulu.” Uko nkulondola. Inu ndi mfulu.

“Mpingo wanga...”

²⁴⁰ Chabwino, dulani mumasuke. “Watitsuka ife ndi kutimasula ife ku zipembedzo zathu, mu Magazi Ake Omwe,” ndipo watipanga ife kukhala afulu kuti tizikhoza kuziganizira tokha, ndi kudzychitira tokha, ndi kudziyankhulira tokha, ndi kudzychitira tokha.

²⁴¹ “Chabwino, ngati ine nditabwerera ndi kukawauza abusa ine ndikufuna kuti ndibatizidwenso, iwo angati...”

²⁴² Nanga bwanji, “Iwe uli mfulu”? Ili ndi vumbulutso, inu mukudziwa. Chabwino. Ndiwe mfulu.

²⁴³ Ngati iwe unakonkhedwa ndi ka mchere pang’ono monga *chonchi*, dzina la “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” apa pali dziwe liri apa, ndilokonzeka mmawa uno, ndi madzi mmenemo. Mukuona? Inde, bwana. Izo si zolondola.

²⁴⁴ Chotero, inu simuli omangidwanso. Inu ndi amfulu, koma mwinamwake inu simukudziwa izo. Koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu mmawa uno, Baibulo linati, “Iye anatimasula ife ku machimo athu, kusakhulupirira kwathu, kuti ife tikakhoze kulandira Vumbulutso la Yesu Khristu.” Kazipitani, mwamasulidwa!...simukuyenera kutenga chimene mpingo uliwonse umanena zokhudza Izo. Muzitenga zimene Mulungu ananena zokhudza Izo. Apa pali Vumbulutso Lake akuwulula Yemwe Iye ali.

²⁴⁵ “Ine nthawizonse ndinkakhulupirira kuti Mulungu Atate anali ndi ndevu, zazitali zoyera, tsitsi loyera; ndipo Mwanayo anali bambo wa usinkhu wapakati; ndipo Mzimu Woyera unali mnyamata womutuma.” M’bale, chimenecho ndi chikunja. Chimenecho ndi chikunja ngati inu mumakhulupirira mwa Amulungu atatu.

246 Lamulo loyamba kumene, kodi Lamulo loyamba ndi chiyani? “Imvani inu, O Israeli: Ndine AMBUYE Mulungu wanu, Mulungu mmodzi.” Ndi zimenezotu.

247 Iye ndi Mulungu mmodzi, osati amulungu atatu. Iye amakhala mu maudindo atatu, amatumikira malo atatu. Iye ndi Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu. Iye ndi Mphungu, Mwanawankhosa, ndi—ndi Mkango. Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Rozi la Sharon, Kakombo wa Mchigwa, ndi Nyenyezi ya Mmawa, Muzu ndi Mphukira ya Davide. Iye ndi kuyambira A mpaka Z. Iye ndi Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Iye ali zonse zimenezo, koma Iye ndi Mmodzi. Iye ndi Mulungu mmodzi. Amenewo ndiwo maudindo Ake amene amapita kwa Iye, koma pali Mulungu mmodzi.

248 Sipanakhalepo aliyense, tsamba lililonse la Baibulo ngakhale mu mbiriyakale, kufikira mpingo wa Katolika, anayamba wabatizidwapo pomizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.”

249 Ngati inu mungandiwonetse ine tsamba kapena chirichonse, inu mulembe izo, muziike izo apa kwa ine, usikuuno, ndipo ine ndituluka mu tchalitchi chino, ndikuti, “Ndine wachinyengo; ine ndawaphunzitsa anthu zolakwika.” Ngati inu mungandiwonetse ine mutu umodzi wa Lemba, kapena mundibweretsere ine mbiriyakale imodzi, mbiriyakale yovomerezeka, zimenezo zindiwonetsa ine pamene anthu anayamba abatizidwapo, mu Baibulo, mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Kapena, mundibweretsere ine Lem- . . . kapena, bukhu limodzi la mbiriyakale, tsamba limodzi, chobwera chimodzi mu mbiriyakale, pamene aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kufikira Nicene Council ya mpingo wa Katolika. Mubwere, mubweretse izo kwa ine; ndipo ine ndidzaika chikwangwani ku nsana wanga ndi kuyenda kudutsa mu Jeffersonville, ndipo inu nkukhala kumbuyo ndi lipenga, mukuliwomba. Ine ndidzalemba pamenepo, “Mneneri wabodza, akuwapotoza anthu.”

250 Ndipo, abusa, ngati inu muli pano mmawa uno, inu muchite zimenezo, inu mukuyenera mundilole ine kuti ndichite zimenezo kwa inu. Mukuona? Mubwere, mudzandiwonetse ine. Koma inu mukuchita mantha.

251 Tsopano, ndi chiyani chimenecho? *Ili* ndi Vumbulutso. *Ili* ndi Vumbulutso. Ndipo uwu ndi Mzimu Woyera, Khristu, akutumiza Uthenga Wake ku mipingo. Mverani Izo. Mverani Izo. Ndizo zimene Baibulo limaphunzitsa.

252 Kodi izo zinadzabwera pati? Ngati inu simukwiya, ndikuchokapo, kudutsa msabatayi, inu—inu mudzatenge ma Nicene Council. Mudzatenge la Hislop *Two Babylons*. Mudzatenge . . .

²⁵³ Tsopano, mbiriyakale ya Josephus ndi yabwino, koma iye anangolembe ndime imodzi yokha ya Khristu, anati, “Panali munthu wotchedwa Yesu yemwe an kayendayenda, akuchiritisa anthu. Ndipo—ndipo iye anafa, kapena, ayi, Pilato anamupha iye, ndipo—ndipo, kapena Herodi, kapena anamupha iye. Ndipo kenako ophunzira anapita ndipo anakabako thupi lake, ndipo anakalibisa ilo. Ndipo kenako usiku uliwonse iwo ankapita ndi kukadula chidutswa cha ilo ndi kumadya ilo.” Anati, “Iwo anali odyamzawo.” Akamatero, iwo amadya mgonero, inu mwaona. Malingaliro achithupithupi! Josephus si woti nkumumvera.

²⁵⁴ Koma mukatenge la *Foxes Book Of The Martyrs*. Liripo labwino lovemerezeka. La *Foxes Book Of Martyrs*, ndi angati anayamba awerengapo ilo? Ndithudi. La Pember *Early Ages*, kapena—kapena la Hislop *Two Babylons*, kapena—kapena kuvomereza kwina kwakukulu. Kapena, la—lalikulu kwambiri limene ife tiri nalo ndi la Nicene Council, la pre-Nicene Council ndi la Nicene Council. Ndipo inu mukapeza kunjika uko, zimenezo sizinatchulidwe nkomwe, palibe anthu.

²⁵⁵ Mutenge Malemba Oyera ndipo muwone ngati anayamba wakhalapo aliyense mu Baibulo anayamba wabatizidwapo, pogwiritsa ntchito maudindo amenewo, dzina “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Izo zimaimira milungu itatu. Izo ndi za mwambo wachikunja. Ndipo Chikatolika si kanthu kalikonse mu dziko koma ka—kachitidwe kachikunja ka Chikhristu. Ndipo kuchokera ku mpingo wa Katolika kunadzabwera Martin Luther, John Wesley, Baptist, Presbateria, ndi ena otero.

²⁵⁶ Koma mmasiku otsiriza panali khomo linaikidwa pakati pamenepo, limene linadzatsegula Choonadi kenanso, kuti, “Baibulo linanena chomwecho,” ndi mneneri wamkulu amene an kayenera kubwera pa dziko lapansi mu masiku otsiriza. Ndipo ife tikukhulupirira kuti iye akubwera. Penyani. Ndipo iye adzakhala ndi Mpingo. Tsopano, ife tiziwona izi.

²⁵⁷ Tsopano—tsopano, kumbukirani, ili ndi Vumbulutso. Inu simungakhoze kuchotsera kwa Ilo. Tsopano, ndi kubhetcheredwa bwanji! Mpezeni munthu mmodzi mu Baibulo, malo amodzi amene iwo anamubatizapo aliyense mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” kapena anayamba amukonkhapo aliyense, mupeze zimenezo mu Baibulo, kwa chikhululukiro cha machimo awo. Iwo sanateropo. Ndipo munthu aliyense, ziribe kanthu kuti anabatizidwa chotani, amayenera kubwera ndi kudzabatizidwa, kachiwirinso, mu Dzina la “Yesu Khristu,” kuti alandire Mzimu Woyera.

²⁵⁸ Machitidwe 19, “Paulo akudutsa ku gombe lakumtunda ku Efeso, anawapeza ophunzira enaake.” Iye anati. . . Ophunzira, akukhala ndi msonkhano wopambana. Iwo ankamutsatira munthu dzina lake Apollos, yemwe anali woimira mlandu wotembenuka; wa Baptisti yemwe ankakhulupirira pa Yohane

M'batizi, ndipo amatsimikizira mwa Malemba kuti Yesu anali Khristu.

259 Paulo akudutsa ndipo anamuwona Aquila ndi Priscilla, pa mutu wa 18 wa Machitidwe. Ndipo kenako anapita kuti akadye chakudya chamadzulo, kapena chinachake chimzake, ndi Aquila ndi Priscilla. Iwo anamuuzza iye za munthu uyu wamkulu. Iwo anapita kukamumvera iye. Iye anamumvetsera iye usiku umenewo. Iye anati, “Iye ali bwino kwambiri. Izo ndi zabwino kwambiri. Izo nzabwino. Koma,” anati, “kodi inu munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?”

260 Nanga bwanji inu Abaptisti osauka kumbuyo uko, mukukhulupirira munalandira Mzimu Woyera *pamene* inu munakhulupirira?

Iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira?”

Winawake anati, “Zimenezo sizinalembedwe mmenemo.”

261 Ine ndikutsutsa zimenezo. Ine ndiri nalo la Chigriki lovemerezeka pomwe apa, la Chihebri, nalonso. Baibulo limanena mu Chigriki, ndi ziwiri zonse, Chihebri, ndiponso mu Chiaramaiki. Mu zitatu zonse za izo, ine ndiri nazo izo pomwe pano, zimene zinati, “Kodi munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira?” Uko nkulondola. “Kodi munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira?”

262 Tsopano, iye anati, “Ife sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.”

Kenako iye anati, “Munabatizidwa kwa chiyani?”

263 Iwo anati, “Ife tinabatizidwa kale ndi munthu amene anamubatiza Ambuye Yesu Khristu. Ife tinabatizidwira ku ubatizo wa Yohane,” dziwe lomwelo la madzi, mwinamwake, “munthu yemweyo.”

264 Paulo anati, “Zimenezo sizigwira ntchito. Iye ankangobatiza ku kulapa, osati ku chikhululukiro cha machimo.”

265 Tsopano, ena a inu anthu a Oneness munabwera pamenepo ndipo—ndipo munadzabatizidwa chomwecho, molakwika. Inu mumabatiza chomwecho kwa, kwa chipulumutso. Madzi samamupulumutsa munthu; ndi Magazi, ukalapa. Osati kudzera mu ubatizo kuti usinthidwe. Ayi, bwana. Kusinthidwa kumabwera ndi Mzimu. Ubatizo ndi—ndi mawonetseredwe a panja a ntchito ya mkati ya kusinthidwa kumene kwachitika. Mukuona? Chabwino. Zindikirani.

266 Iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira?” Iwo anati . . .

Iye anati, “Ife sitikudziwa ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse.”

Iye anati, “Nanga inu munabatizidwa chotani?”

Anati, “Ife tinabatizidwira kwa Yohane.”

²⁶⁷ Iye anati, “Yohane indetu ankabatiza ku kulapa, kwa kulapa, kunena kuti ‘inu mukhulupirire pa Iye,’ Mwanawankhosa, Nsembe inkayenera kubwera, pa Ambuye Yesu Khristu.” Ndipo pamene iwo anamva ichi, iwo anabatizidwanso mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anasanjika manja ake pa iwo ndipo iwo analandira Mzimu Woyera, ndipo anayankhula mu malirime ndipo analosera.

²⁶⁸ Ndiuzeni ine kuti zimenezo si Lemba, ndipo mudiwonetse ine paliponse, pamene aliyense anayamba wabatizidwapo njira ina iliyonse mu Chipangano Chatsopano koma Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ndiwonetseni ine.

²⁶⁹ Agabasi Woyera ndi ambiri, amene analipo, amene anabatizidwa kutsika pansu nithawi ya—ya—ya—Nicene Council, ndipo mmodzi aliyense wa iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Mamishonare ankalima mminda ndi Dzina la Yesu Khristu.

²⁷⁰ Koma pamene a Nicene Council anadzabwera, iwo ankayenera kukhala ndi milungu itatu. Iwo anamutsitsira pansu Paulo . . . kapena anamutsitsira pansu Jupiter, ndipo anamuikapo Paulo. Iwo anamutsitsira pansu Venus, ndipo anamuikapo Maria. Iwo anali ndi mitundu yonse ya milungu, mitundu yonse ya oyera ndi china chirichonse, ndipo anadzapanga ubatizo wautatu ndipo anakawadyetsa izo Achiprotestanti. Ndipo iwo amamezerabe izo.

²⁷¹ Koma Kuwala kwa madzulo kwafika tsopano. Mneneri anati, “Kudzakhala kuwala mu nthawi ya kumadzulo.”

Ku—kudzakhala Kuwala mu nthawi ya
kumadzulo,
Njira ya Ulemelero inu mudzaipezadi;
Kudzera mmadzi, ndiko Kuwala lero,
Kumizidwa mu Dzina lofunika la Yesu.
Ana ndi aakulu, lapani machimo anu,
Mzimu Woyera udzalowamo ndithu;
Kuwala kwa madzulo kwabwera,
Ndi zooni kuti Mulungu ndi Khristu ali
Mmodzi.

²⁷² Inu mukhulupirira zimenezo? Petro ananena, pa Tsiku la Pentekoste, “Mulole ichi chidziwike, kwa inu, nyumba ya Israeli, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, Yemwe inu munamupachika, zonse Ambuye ndi Khristu;” ndime ya 16 ya mutu wa 2. Inde. “Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, Yemwe inu munamupachika, ziwiri zonse Ambuye ndi Khristu. Nyumba yonse ya Israeli idziwe, motsimikizika.”

273 Ndimayankhula ndi Myuda osati kale kwambiri, kumtunda kuno ku Nyumba ya Davide, iye anati, “Inu Amitundu simungathe kumudula Mulungu mzidutswa zitatu ndi kumpereka Iye kwa Myuda. Ife timadziwa bwinoko kuposa zimenezo.”

274 Ine ndinati, “Ndi zimenezotu basi, Rabbi. Ife sitimamudula Mulungu mzidutswa zitatu.” Ine ndinati, “Inu mumakhulupirira aneneri?”

Iye anati, “Ndithudi.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumakhulupirira Yesaya 9:6?”

Iye anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Kodi mneneri ankayankhula za ndani?”

“Mesiya.”

Ine ndinati, “Kodi Mesiya adzakhala pa ubale wanji ndi Mulungu?”

Iye anati, “Iye adzakhala Mulungu.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola.” Ameni.

Mwaona, ndi zimenezotu. Mwaona, inu simungakhoze kumudula Iye mzidutswa zitatu.

275 Ngati inu mamishonare kuno...Mmodzi wa iwo akupita kumene kwa Ayuda, ine ndikukhulupirira, bambo wakhala *apayu*. Musakayerekeze konse kukamupatsa Myuda “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Iye akakuuzani inu mwamsanga, iye amadziwa kumene izo zimachokera, “Nicene Council.” Iye sakamvetsera kwa izo. Koma inu mukamuwonetse iye kumene Mulungu ameneyo anadzasandulika thupi, ndipo Iye ndi Mulungu yekhayo amene alipo. Mulungu, anadzasandulika thupi mu mawonekedwe a munthu ndipo anadzakhala pakati pathu, kuti adzatiyeretse ife; anachokapo, kuti Iye Mwiniwake adzakhoze kubwera mu mawonekedwe a Mzimu Woyera. Mulungu, Atate, Mzimu Woyera, ndi Munthu yemwe yemweyo.

276 Baibulo linati mu—mu mibadwo ya Yesu Khristu, mu mutu wa 1 wa Mateyu, Ilo linati, “Abrahamu anabala Isaki. Isaki anabala Yakobo.” Ndipo mpaka mmusi, anati, ndipo kenako mu... Ndiroleni ine ndiwerenge zimenezo, ndipo kenako tsopano inu mudzadziwa basi zimene ine ndikuziyankhula. Mateyu, mutu wa 1. Ndipo ife ti... Tsopano tiyeni tiyambire ndi ndime ya 18.

Tsopano kubadwa kwa Yesu Khristu kunali motere: Pamene... amayi ake Maria anali atatomeredwa ndi Yosefe, iwo asanakhale pamodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa... .

277 “‘Mulungu Atate’”? Kodi izo zikuwerengeka chomwecho? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Anapezeka ali ndi Mwana wa Ndani? [“Mzimu Woyera.”] Wa... [Malo opanda kanthu

pa tepi.] Ine ndimaganza Mulungu Atate anali Abambo Ake? Ndiye, Mulungu, Atate ndi Mzimu Woyera, ndiwo Mzimu womwe womwewo, kapena Iye anali ndi Atate awiri.

Kenako Yosefe mwamuna wake, pokhala munthu wolungama, . . . osafuna kumupanga iye chitsanzo cha pa gulu, anasinkhasinkha . . . zomusiya iye mwamseri.

Koma pamene iye amalingalira pa zinthu izi, taonani, mngelo wa Ambuye anawonekera kwa iye mu loto, kuti, Yosefe, iwe mwana wa Davide, usawope . . . kumutenga Maria mkazi wako: pakuti icho chimene chalandidwa mwa iye ndi cha . . .

278 “‘Mulungu Atate’”? Huh? [Osonkhana akuti, “Ayi. ‘Mzimu Woyera.’”—Mkonzi]. “Mzimu Woyera.” Ndiye Ndani amene anali Atate a Yesu Khristu? [“Mzimu Woyera.”] Mzimu Woyera. Ndi chiyani Icho chiri mwa inu? [“Mzimu Woyera.”] Chabwino, ameneyo ndi Mulungu, Atate, aponso. Si choncho Izo? Ndithudi.

Ndipo iye adzabala mwana wamwamuna, ndipo iwe udzamutcha dzina lake YESU: . . .

279 *Apa* pali Mulungu Atate, *apa* pali Mulungu Mzimu Woyera, ndipo *apa* pali Mulungu Mwana, mwaona, ameneyo ndi Amulungu atatu. Baibulo silimanena izo. Awiri awa akuyenera kukhala chimodzimidzi, kapena Iye anali ndi atate awiri. Mukuona? Iye sangakhale ndi atate awiri. Inu mukudziwa zimenezo.

Tsopano, iye adzabala mwana wamwamuna, ndipo iwo adzamutcha dzina lake YESU: pakuti iye adzapulumutsa anthu ake ku machimo awo.

Tsopano zonse izi zinachitidwa, kuti zikakhoze kukwaniritsidwa zimene zinayankhulidwa ndi Ambuye mwa mneneri, kunena,

. . . namwali adzakhala ndi mwana, ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo iwo adzamutcha dzina lake Emmanuele limene liri kutanthauzira kwake, Mulungu nafe.

280 Umenewo ndi mutu wa 1 wa Mateyu.

281 Mateyu 28:19, pamene Yesu anati, “Pitani, mukabatize mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera ndi ndani? Yesu Khristu, ndithudi.

282 Inu mukawerenga nkhani ya chikondi, yakuti, “Yohane ndi Maria anakhala moyo wosangalala nthawizonse.” Yohane ndi Maria ndi ndani? Mubwerere koyambirira kwa nkhanayo, ndipo mukafufuze.

283 Ngati palibepo chinthu choterocho, palibepo dzina, “Atate, Mwana, kapena Mzimu Woyera,” ndiye Ndani, ndi Dzina la

Ndani limenelo? Mubwerere, koyambirira kwa nkhaniyo, ndipo mukawone Yemwe Iye anali kuyankhula za iye.

284 Petro, pa Tsiku la Pentekoste, anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la ‘Yesu Khristu’ kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu.” Iye anali ndi vumbulutso.

Yohane anali ndi vumbulutso.

285 Yesu *anali* Vumbulutso, Iye anadzipanga Iyemwini pomwe apa mu Lemba, “Ine ndine Iye amene anali, amene ali, ndi amene azadza, Wamphamvuzonse.” Psyii! Chabwino.

286 Tsopano, tiyeni titenge ndime ya 7, mofulumira kwambiri tsopano, ife tisanatuluke, basi mofulumira mmene ife tingathere. Wamphamvuzonse.

. . . ulamu- . . . ulemelero ndi ulamuliro kwa nthawi za nthawi. Amenii.

Ndipo . . . watipanga ife mafumu ndi ansembe kwa Mulungu. . . Atate ake; ndipo kwa iye kukhale ulemelero ndi ulamuliro kwa nthawi za nthawi. Amenii.

287 Mukuwona vumbulutso limenero apo, mmene Ilo likuwululidwira? Momwe Mulungu. . . Amuna amakanda mitu yawo ndi kukoka tsitsi lawo, ndi zinthu, kuyesetsa kuti apeze chimene “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” ali, kupanga atatu, mwa mmodzi.

Musati mukoke tsitsi lanu ndi kukanda mmutu mwanu. Mungoyang’ana mmwamba. Vumbulutso limabwera kuchokera Mmwamba. Ndipo izo nzoona. Iye adzawulula, si “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Ndi maudingo atatu amene Mulungu mmodziyo amakhalamo.

288 Iye anali mu udindo, “Mzimu,” mwa Iyemwini, chifukwa munthu akudzitsitsa, kenako Iye anadzadzipangira Iyemwini thupi, anadzakhala mwa ilo, kuti adzapange Magazi Ake Omwe; osati kudzera mukugonana, monga mmene izo zinkakhalira mmunda wa Edeni, koma anapanga thupi lolengedwa. Ndipo kudzera mwa thupi lobadwa mwa namwali limenelo, Iye anapereka Magazi amene anadzatyeretsa ife ndipo anatisamula ife ku kusakhulupirira kwathu, kuti tikakhulupirire pa Iye. Ndiye, ife timachita zimenezo, ife timamulandira Iye mu mtima wathu, ameneyo ndi Mulungu mwa ife; Mulungu: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Mukuona? Basi monga Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu, ndicho chinthu chomwe chomwecho. Chabwino.

289 Tsopano, ndime ya 7, uku ndi kulengeza. Kulengeza ndi:

Taonani, iye akubwera ndi mitambo; ndipo diso lililonse lidzamuwona iye, . . . iwo nawonso amene anamupyozza iye: ndi onse a chibale a dziko lapansi adzalira chifukwa cha iye.

290 Oh! Ife tatsala ndi nthawi yochuluka bwani? Zimenezo ndi zokongola pamenepo. Kodi inu mungapereke ena sart-... maminiti twente? [Osonkhana akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Inu mungatero? [“Ameni.”] Chabwino. Tsopano, kenako, mawa... Usikuuno, ife tidzayesera kutenga zonse za *Masomphenya Apa Patmo*, usikuuno. Lero, ife tilekezera pa kulengeza.

291 Oh! Inu mukumverera bwino? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Inu mumalikonda Baibulo lakale ili? [“Ameni.”] Ilo ndi Vumbulutso. Chiyani, ndi chiyani chimenecho? Mulungu akufikira, mu Bukhu ili, ndipo akuchotsa chophimba, nkuti, “Ndi Uyo pamenepo: Mneneri, Wansembe, Mfumu; Atate, Mwana, Mzimu Woyera; Iye amene anali, amene ali, ndipo adzadzaz. Zinthu zonse izi, Iye ndi Mulungu.”

292 Tsopano, tiyeni tichotse chophimbacho, basi kwa maminiti pang’ono tsopano, Ambuye akutithandiza ife, tichotse chophimba mmaso athu. Ndipo titenge...

Taonani, iye akudza mmitambo;...

293 Tsopano, Iye akubwera chotani? “Ndi mitambo.” Mtambo wa mtundu wanji? Mitambo ya ulemelero. Osati imodzi ya mabingu awa, mtambo wa mvula, koma mitambo ya ulemelero.

294 Inu muwone ndi mtundu wanji wa mtambo umene Iye anali atakutiridwamo pamene Petro ndi iwo anawona masomphenya Ake pa Phiri la Chiwalitsiro, mtambo unamuphimba Iye. Chovala Chake chinanyezimira. Iye anakutiridwa ndi mtambo, mphamvu ya Mulungu.

295 Oh, ife tifika kwa zimenezo, pano mu mibadwo ya mpingo imeneyi. Ine ndikukuuzani inu, izo basi—basi zikungogirigisha munthu wanga wamkati, ndikaganizira za zimenezo. Chimene kubwera Kwake...ine ndikuwona tsiku lino limene ife tikukhalamo, pamene palibe chirichonse, palibe chiyembekezo chimene chatsala koma Kubwera Kwake.

296 Tsopano ife mwamsanga titenga izi. Tsopano kumbukirani.

...diso lirilonse lidzamuwona iye,...

297 Tsopano, umenewo sunali Mkwatulo pamenepo, ndi choncho? [Osonkhana akuti, “Ayi.”—Mkonzi]. Mukuona? Sunali Mkwatulo. Iwo sunali Mkwatulo. Kodi Iye anali kuyankhula chiyani? Kubwera kwachiwiri.

...ndipo iwo nawonso amene anampyoza iye: ndi achibale onse a pa dziko lapansi adzabuma chifukwa cha iye.

298 Tsopano ife tibwerera ndi kukatenga mbiriyakale ina. Tiyeni tibwerere mmbuyo ku Zakariya, ndipo tikatenge mutu wa 12 wa Zakariya. Zakariya. Chabwino.

299 “Ndipo Ambuye amawonjezera ku mpingo tsiku ndi tsiku monga amene akanati apulumutsidwe.” Mmene ife tiriri

othokoza chifukwa cha vumbulutso labwino la Yesu Khristu! Kodi inu simuli okondwa chifukwa cha Iye? Tsopano, ife tiziika izi kukhala bukhu mofulumira basi mmene ife tingathere, kwa anthu, ndiyeno inu mukhoza kudzakhala nalo ilo, kuti muzikawerenga ilo mu kachetechete wa chipinda chanu ndi zinthu, ndi kukaliwerenga ilo, nokha. Chabwino.

³⁰⁰ Zakariya, Zakariya, mutu wa 12 tsopano wa Zakariya. Ndipo ife tikufuna, muzitenge izi mwapemphero kwenikweni tsopano. Ndipo ine ndikufuna kuti nditenge izi kwa ulemelero wa Mulungu. Tsopano, Zakariya 12, tiyeni tiyambire pa ndime ya 9. Mveterani mwatcheru tsopano. Iye akuyankhula za Kubwera. Zakariya 12, ndipo ife tiyambira pa 9, mu ndime ya 9.

Ndipo izo zidzafika pochitika . . .

Zakariya, akunenera, zaka foro handiredi ndi eyite-seveni kusanati kudza kwa Khristu.

Ndipo izo zidzafika pochitika mu tsiku limenero, kuti ine ndidzafuna kuwononga onse . . . mafuko amene adzabwere motsutsana ndi Yerusalemu. (Taganizani za zimenezo.)

Ndipo ine ndidzatsanulira pa nyumba ya Davide, ndipo pa okhala mu Yerusalemu, mzimu wa chisomo ndi wa kupembedza: ndipo iwo adzayang'ana pa ine yemwe iwo anampyoza, . . .

³⁰¹ Tsopano, ndi liti limene Uthenga udzabwerere kwa Ayuda? Pamene tsiku la Amitundu lidzatha, Uthenga wakonzeka, kupita kwa Ayuda. Oh, ine ndikhoza, ngati ine ndingathe kuneneratu kwa inu chinachake chaching'ono chimene chikukonzekera kuchitika pompano, mwaona, mu tsiku lomwe lino. Inu mukuona? Icho chikukonzekera kuti chichitike. Ife tidzazipeza izo mu M'badwo wa Mpingo. Ndipo chinthu chachikulu ichi chikukonzekera kuti chichitike, tipitirira kupita ku Chivumbulutso 11 ndi kukatenga aneneri awiri amenewo, Eliya ndi Mose kubwerera kenanso kwa Ayuda. Ife takonzekera zimenezo. Chirichonse chikukhala mu dongosolo, basi chakonzeka. Uthenga wa Amitundu uwu, monga Ayuda anawubweretsera iwo kwa Amitundu, Amitundu adzawubwezera iwo kwa Ayuda kenanso. Ndipo Mkwatulo udzabwera.

³⁰² Tsopano kumbukirani, ichi apa chikubwerachi, chikadzatha Chisautso . . . Mpingo sudzadutsa mu Chisautso. Ife tikudziwa zimenezo. Baibulo limanena chomwecho. Mukuona? Chabwino.

³⁰³ Tsopano, Iye adzatsanulira pa nyumba ya Israeli, (chiyani?) Mzimu Woyera womwewo, mwaona, ukadzatha Mpingo wa Amitundu.

. . . ndipo iwo anayang'ana pa ine yemwe iwo anampyoza, ndipo iwo adzambulira iye, monga mmodzi

amene alirira mwana wake yekhayo, ndipo adzakhala ali mu zowawa chifukwa cha iye, monga wina yemwe ali mu kumva kuwawa chifukwa cha woyamba kubadwa wake.

Ndipo mu tsiku limenero kudzakhala...kulira kwakukulu mu Yerusalemu...ndi kulira...mu—mchigwa cha Megiddon.

Ndipo—ndipo dziko lidzalira, banja lirilonse kugawanika; banja la nyumba ya Davide kugawanika, ndipo...banja la nyumba ya Nataniele kugawanika, ndipo mmodzi aliyense wa nyumbazo kugawanika; (pamene iwo awona, chimene chiti chidzachitike, chimene chiti chidzachitike pamene Iye adzabwera mmitambo ya ulemelero, pa kuwonekera Kwake kwachiwiri.)

³⁰⁴ Ndipo pamene Ayuda amenewo amene anampyoza Iye... Inu mukudziwa, Lemba lina limanena kuti iwo adzamufunsa Iye, kumene Iye anakatenga mabala amenewa.

Iye anati, “Mu nyumba ya Mzanga.”

³⁰⁵ Ndipo siidzakhala nthawi yolira yokha kwa Ayuda omwe anamukana Iye, ngati Mesiya, koma iyo idzakhala nthawi yolira kwa Amitundu osiyidwa awo kumbuyo uko, omwe avomereza...omwe amukana Iye ngati Mesiya wawo wa tsiku lino. Iwo adzakhala akubuma ndi kulira. Namwali wogona adzakhala akubuma. Umenewo ndi mpingo uwo umene unakana kutenga Mafuta mu nyali yake. Panali anamwali khumi anatuluka kunjja, onse anthu abwino, koma asanu a iwo anali ndi Mafuta mu nyali zawo. Asanu enawo anali anthu abwino, anthu abwino, koma analephera kuti apeze Mafuta mu nyali zawo. “Ndipo iwo anaponyeredwa mu mdima wa kunjja kumene kudzakhale kulira, kubuma, ndi kukukuta kwa mano.”

³⁰⁶ Ndi izi apa, “Iwo adzakhala akubuma.” Baibulo linanena apa, “Iwo adzakhala akubuma, ndipo adzakhala wosweka mtima kwambiri, kufikira mpakana...”

³⁰⁷ Apa, ine ndikupatsani inu lina, Genesis 45, ngati inu mukufuna kufika ku zimenezo. Tiyeni tifike kwa izo mphindi chabe ndipo tiwerenge izonso mu Genesis, a...ine ndikukhulupirira, mutu wa 45 wa Genesis. Ine ndikanafuna nditatenga ichi apa, Yosefe akuzizindikiritsa yekha kwa ake—kwa anthu ake. Ndipo ife titenga ichi, basi kungowonetsera zo—zoimira za chimene chiti chidzachitike mu tsiku limenero, kenako ife tidzazimangiriza izo pamodzi.

Kenako Yosefe sakanatha kudziletsa yekha pamaso...iwo amene anaïma ndi iye; ndipo iye analira, Anapangitsa munthu aliyense apite...achoke kwa ine.

308 Tsopano kumbukirani, Yosefe, akudzidziwitsa yekha, iye analira, “Munthu aliyense achoke pamaso panga.”

Ndipo pamenepo sipanaime munthu wina aliyense ndi iye, pamene Yosefe anali kudzidziwitsa iyeyekha kwa abale ake.

Ndipo iye analira mokweza: ndipo a Igupto ndi nyumba ya Farao anamumva iye. (Iye ayenera kuti anakuwa mokweza.)

Ndipo Yosefe anati kwa abale ake, Ndine Yosefe; kodi bambo anga adakalibe ndi moyo? Ndipo abale ake sakanatha kumuyankha iye; pakuti iwo anali wosautsika ndi kupezekapo kwake.

Ndipo Yosefe anati kwa abale ake, Bwerani pafupi. . . ine, ine ndikukupemphani inu. Ndipo iwo anabwera pafupi. Ndipo iye anati, ndine Yosefe m'bale wanu, yemwe. . . yemwe inu—yemwe inu munamugulitsa kwa Igupto.

Tsopano kotero musati mukhumudwe ayi, kapena kudzikwiyira inueni, kuti inu munandigulitsa ine kuno: pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndidzasunge moyo. (Oh, ndi zokongola motani!)

Kwa zaka ziwiri izi kwakhala. . . njala yakhala ili mdziko: ndipo. . . mmene mudzakhale, kudzakhala kuti sikudzakhala ngakhale khutu kapena zokolola.

Ndipo Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndidzakusungireni inu mtundu pa dziko lapansi, ndi kudzapulumutsa miyoyo yanu ndi chiwombolo chachikulu.

309 Ndiloleni ine ndingotenga tsopano ndi kufanizitsa zimenezo ndi Zakariya, wa 12, basi kwa mphindi chabe. Tsopano, ife tikudziwa zimenezo, moimira. Ngati inu mumaphunzitsa zoimira, ndiye inu nthawizonse mudzazimvetsa izo molondola, ine ndikuganiza, mu—mu choimira.

310 Tsopano, Yosefe, pamene iye anabadwa, iye ankadedwa ndi abale ake. Nkulondola uko? Tsopano ine ndikufuna ndikuwonetseni inu, Yosefe amaimira Mpingo wodzazidwa ndi Mzimu. Yosefe ankadedwa ndi abale ake. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anali wauzimu. Yosefe sakanachitira mwina chifukwa iye amatha kuwona masomphenya. Iye sakanachitira mwina chifukwa iye ankalota maloto, mwaona, ndipo amatha kutanthauzira maloto. Iye, icho chinali chimene chinali mwa iye. Iye samatha kuwonetsera china chirichonse koma chimene chinali mwa iye. Chabwino, kenako, abale ake ankamuda iye, popanda chifukwa. Koma abambo ake ankamukonda iye, chifukwa abambo ake anali mneneri.

311 Mukuona momwe izo zinaliri ndi Yesu? Mulungu ankamukonda Mwana Wake. Koma abale, Afarisi ndi Asaduki, ankamuda Iye, chifukwa Iye amatha kuchiritisa odwala, ndi kuneneratu zinthu, ndi kuwona masomphenya, kumasulira. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? “Iwo ankamuda Iye, popanda chifukwa.”

312 Ndipo kodi iwo anachita chiyani kwa Yosefe? Iwo ananamizira kuti iye wafa, ndipo iwo anamuponyera iye mu dzenje. Anatenga chikhotho chamagazi, cha mitundu isanu ndi iwiri, chimene abambo ake . . .

313 Pali mitundu isanu ndi iwiri yokha mu utawaleza. Ndipo utawaleza, ife tikudziwa zimenezo, ife tifika kwa izo mtsogolo pang’ono, ine ndikuganiza, usikuuno. Utawaleza uli pa Iye apa, Yesu, kumene, “Iye ali woti aziwoneka ngati mwala wa jasipa ndi sarde, ndi utawaleza.” Utawaleza ndi pangano.

314 Ndipo limenelo linali pangano la Mulungu pa Yosefe. Ndipo kenako iwo anapaka magazi pa chikhotho chake, ndipo anachitengera icho kwa abambo. Ndipo iye anaganiziridwa kuti wafa. Ndipo . . .

315 Koma iye anatulutsidwa mdzenjemo ndipo anaikidwa mu—mu . . . anagulitsidwa kwa Farao, winawake mu Igupto, ndipo wa—wamkulu anamusunga iye. Ndipo pamene iwo anatero, iye, chinthu choipa chinabwera motsutsana ndi iye, ndipo anaponyeredwa mu ndende. Ndipo kumeneko iye analosera, ndipo anawauza amuna awiriwo kumene mmodzi akanati adzapite ndi kumene mmodzi winayo akanadzapitako; wopereka chikho ndi wo—ndi wophika mkate, pa kutengera za maloto awo.

316 Ndipo kenako iye anakwezedwa kuchoka pamenepo, kupita ku dzanja lamanja la Farao. Ndipo panalibe munthu amakhoza kukafika kwa Farao, kokha kudzera mwa Yosefe. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

317 Chiyani ichi. Tsopano, a . . . pamene Yosefe kenako anadzagulitsidwa kwa Aigupto. Ndipo, penyani, chirichonse chimene iye amachita chimaimira Khristu. Tayang’anani pa wopereka chikho uyu ndi wophika mkate uyu pamenepo, ndipo awiri onsewo onse anali ndi maloto. Ndipo Yesu, pamene Iye anali mu nyumba Yake ya ndende. Kumbukirani, Yosefe anali mu ndende. Ndipo Pamene Yesu anali mu ndende Yake, (motani?) atakhomeredwa pa mtanda, panali mmodzi anapulumsidwa ndipo mmodzi anataika. Yosefe, pamene iye anali mu ndende yake, mmodzi anapulumsidwa, mmodzi anataika.

318 Ndipo zindikirani. Kenako Yesu atachotsedwa pa mtanda, Iye anakwezedwa kupita Kumwamba, ndipo akukhala pa dzanja lamanja la Mzimu waukulu, Yehova. “Palibe munthu angadze kwa Mulungu pokhapokha kudzera mwa Ine.” Palibepo *Tikuoneni Maria*, palibepo wodala *uyu* kapena wodala *uyo*.

Koma, kudzera mwa Yesu Khristu, “Mkhalapakati yekhayo amene alipo pakati pa Mulungu ndi anthu,” thupi lofunikira limenero limene Mulungu ankakhalamo, pakati pathu, amene anatenga Dzina la Mulungu. Ndipo Mulungu anatenga dzina la munthu. Mulungu anatenga . . .

319 Taonani apa. Pachiyambi, pamene Adamu. . . Ine basi ndikulephera kuchokako kwa izo. Zikuwoneka ngati winawake sakuzimvetsa Izo, penapake. Taonani. Pachiyambi. . . Ndiloleni ine ndikuwonetseni inu chinachake kenanso. Mzimu Woyera ukundichenjeza ine kuti ndichite ichi. Ine ndikusiya phunziro langa kwa miniti. Pamene nkhani yoyamba inabwera ku Ulemelero, kuti mwana anali atatayika, Adamu, kodi Mulungu anatumiza Mngelo? Kodi Iye anatumiza mwana? Kodi Iye anatumiza aliyense? Iye anabwera, Iyemwini, kuti adzamuwombole mwana Wake wotaika. Aleluya! Mulungu sanadalire izo kwa mmodzi aliyense koma Iyemwini. Mulungu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu, ndipo anamuwombola munthu, Iyemwini. Ndizo. . . “Ife tinapulumutsidwa,” Baibulo linati, “mwa Magazi a Mulungu.” Wachivundi, Mulungu anali. . . Mulungu wachisavundi anapangidwa kukhala wachivundi, ndi cholinga chofuna kuchotsa tchimo, kuti adzakhale Mwanawankhosa, Iyemwini; kuti akalowe mu Ulemelero, ophimbidwa, ndipo ndi Magazi Ake Omwe pamaso Pake, kuseri kwa chophimba.

320 Tsopano, Yosefe, uko mu Igupto iye akupita. Ndipo kumeneko iye anakwezedwa kuchoka mndende yake, kupita ku dzanja lamanja la Farao, ndipo anapangidwa kukhala woyang’anira. Ndipo chirichonse chinkapambana mu masiku a Yosefe.

321 Tsopano, pamene Yesu adzabwerera, ngakhale chipululu chidzaphukira ngati duwa. Iye ndi Mwana wa kuchitabwino, choimira cha Yosefe.

322 Iwo anamuika Yosefe mu. . . Woyang’anira anamutengera iye mnyumba yake; chirichonse chimene iye amachita, iye amachita bwino. Iwo anakamuika iye mu ndende, ndipo ndende yonse inachita bwino. Chirichonse iwo amachita, iye amachita bwino. Ndipo pamene iye anakwezedwa, pamwamba kwambiri, pa Farao, wachiwiri kwa Farao, chirichonse mu Igupto chinachita bwino pamwamba pa chirichonse pa dziko lapansi.

323 Pamene Iye adzabwerera, ilo lidzakhala dziko lochita bwino. Zipululu zakale zidzaphukira, ndipo padzakhala chakudya paliponse. Ndipo ife tikhoza, mmodzi aliyense, atakhala pansu pa mtengo wathu wathu wa mkuyu, ndi kumaseka ndi kumasagalala, ndikukhala moyo kwa nthawizonse mu Kukhalapo Kwake, kumene Iye adzabweranso ngati Mfumu.

324 Iye anali Mwana wa munthu, Mneneri. Amen. Iye anali Mwana wa munthu, Nsembe, Wansembe. Iye ndi Mwana

wa munthu, ngati Mfumu, Mwana wa Davide atakhala pa mpando wachifumu wa ulamuliro Wake. Mwana wa munthu, Iye ali mu-... Mulungu anawonetseredwa ngati Mwana wa munthu. Iye anatsika pansi ndipo anadzakhala munthu, kuti adzachotsere machimo kutali ndi dziko lapansi. Iye anadzakhala munthu, ngati Mneneri. Iye anadzakhala munthu, ngati Wansembe. Iye anadzakhala munthu, ngati Mfumu; Mfumu ya Kumwamba, Mfumu ya oyera, Mfumu ya Muyaya; nthawizonse anali Mfumu, nthawizonse adzakhala Mfumu, Mfumu ya Muyaya.

³²⁵ Tsopano zindikirani, ndiye, Yosefe. Yosefe asanatulukire, iwo ankayenera kuimba lipenga, poyamba. Ndipo anthu amafuula, “Amamupindira bondo Yosefe.” Zinalibe kanthu chimene munthuyo amachita, iye amagulitsa malonda pa msewu, pamene lipenga limenero liwomba, iye amapinda bondo lake. Munthu anali atakonzeka kuti afikire ndikutenga ndalama yake, koma iye amapinda bondo lake, Yosefe akubwera. Oh! A m- . . . wo—wo—wotsanzira anali atakonzeka kuti apange sewero lake, ndipo iye amachita chiyani? Iye amaima kaye. “Yosefe akubwera.” Lipenga lawomba.

³²⁶ Limodzi la masiku awa, chirichonse, ngakhale nthawi, idzaima njii. “Pamene lipenga la Mulungu lidzawomba, ndipo akufa mwa Khristu adzauka, ndipo mmawa udzaswekera ku Muyaya, udzacha mwabwino.” Chirichonse chidzapinda bondo. “Bondo lililonse lidzagwada, ndipo lirime lililonse lidzavomereza kwa Izo.”

Yambani tsopano. “Machimo a anthu ena amapita patsogolo, ena amatsatira.”

³²⁷ Koma tsopano zindikirani chimene chinachitika. Nchaulemelo bwanji! Pamene Yosefe kenako . . . atakwatira wa Amitundu ndipo analandira banja, Efreimu ndi Manasse, ana ake aamuna. Kodi inu munazindikira pamapeto? Pamene Yosefe . . . Yakobo anayamba kumudalitsa Efreimu ndi Manasse. Pamene iye anayamba kuti ayike manja ake, iye anamuika Efreimu kumanja, Manasse kumanzere, kuti atenge madalitso a dzanja lakumanja pa wamkuluyo. Koma pamene iye anayamba kupemphera, manja ake anapingatsidwa, ndipo anampatsa wamng'onoyo madalitso a dzanja la kumanja mmalo mwa mmodzi amene anali pa dzanja lamanja.

³²⁸ Ndipo Yosefe anati, “Osati chomwecho, Atate.” Anati, “Inu mwaika madalitso pa Manasse mmalo mwa Efreimu.”

Ndipo iye anati, “Mulungu wapingatsitsa manja anga.”

³²⁹ Chiyani? Kuchokera kwa Ayuda, wamkulu, woyambakusankhidwa wa Mulungu, kudzera pa Mtanda panabwera madalitso kubwerera kwa Amitundu, kukamutenga Mkwatibwi. Madalitso anabwera kudzera pa Mtanda, kuchoka kwa Ayuda

kupita kwa Amitundu. Wokanidwa, iwo anakana Mtanda, chotero Iye anakatenga Mkwatibwi wa Amitundu.

330 Tsopano pamene Yosefe, chisanachitike ichi, pamene iye anali . . . anamvedwa ndi abale ake, omwe . . . Iwo anali atachoka mu chiyanjano kwa zaka zambiri, Myuda.

331 Tsopano penyani. Ife tikubwerera ku Zakariya tsopano, kumene iwo anabuma, ndi kulira ndi kubuma. Ndipo ngakhale mabanja adzadzilekanitsa okha kuchoka ku mabanja ena, kupita kunja, kukati, “Ife tinachita bwanji izo? Zinatheka bwanji kuti ife tinachita zimenezo?” Pamene iwo adzati, “Nkuti kumene Inu munatenga mabala awo, zipsyera zimenezo mmanja Mwanu?” ngakhale iwo amene anamupyozza Iye. “Iye adzabwera mmitambo. Ndipo iwo adzamuwona Iye, ngakhale iwo amene anamupyozza Iye. Ndipo nyumba iliyonse idzalira, ndipo iwo adzabuma.” Iwo sazadziwa choti achite.

332 Ndipo pamene Yosefe . . . Inu mukuidziwa nkhaniyo. Pamene iye anawona abale ake, ndipo iye anadzipangitsa ngati kuti iye samatha kuyankhula Chihebri, ndipo anatenga wotanthauzira kuti azimutanthauzira iye. Ndipo iye samatha kuyankhula Chihebri, iye akuchita chomwecho; koma iye ankafuna kuti afufuze. Ndipo chotero pamene potsiriza, tsiku lina, pamene iwo anamubweretsa mchimwene wake wamng’ono, kodi inu munazindikira? Iye anali Benjamin amene anawuyatsa moyo wa Yosefe?

333 Nchiyani icho, lero, chimene chiti chidzayatse moyo Wake, Yosefe wathu, Yesu? Mpingo waung’ono uja umene wakhala uli uko ku Iran kutali, yemwe wasunga malamulo a Mulungu. Ndipo ndi anthu obadwa mwatsopano amene asonkhana ku Palestina, ndipo abwezeretsedwanso kenanso. Nyenyezi ya nsonga sikisi ija ya Davide, mbendera yakale kwambiri mdziko, fuko labadwa mu zaka pang’ono zapitazi. Ndi ameneyo Israeli.

Mafuko akusweka, Israeli akuwuka,
Zizindikiro zimene Baibulo linaneneratu;
Masiku a Amitundu atha, ndi zowopsya
zachuluka;
“Bwererani, O omwazika, kwanu komwe.”

Tsiku la Chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera mwa mantha;
(Tangoyang’anani izo, iwo onse akhala a
misala.)
Dzadzidwani ndi Mzimu, nyali zanu ziwale,
Yang’anani mmwamba! Chiwombolo chanu
chayandikira.

Aneneri abodza akunama, Choonadi cha
Mulungu akuchikana,
Kuti Yesu Khristu ndi Mulungu wathu;

(Ulemelero!) Koma Vumbulutso labwera.
Chotero ife tidzayenda momwe atumwi
anaponda. (Mmalo awo kumene.)

Pakuti Tsiku la Chiwombolo layandikira,
Mitima ya anthu ikulephera mwa mantha;
Dzadzidwani ndi Mzimu wa Mulungu nyali
zanu ziwale,
Yang'anani mmwamba! Chiwombolo chanu
chayandikira.

334 Oh! Oh, Yosefe, pamene iye anamuwona Benjamin
wamng'ono ataima pamenepo! Ameneyo ndi mchimwene
wake wamng'ono. Inu mukumuwona Benjamin wamng'ono
tsopano uko...? ...kutali uko, atakhala pamenepo? Mafuko a—
a dziko lapansi, a Ayuda, atabwerera kumbuyo uko kumene
kudzakakhale handiredi ndi forte-foro sauzande a iwo ataima
pamenepo, kuti akamulandire Khristu pamene iwo adzamuwona
Iye Akubwera. Iwo adzati, “Taonani, uyu ndi Mulungu wathu
Yemwe ife tamudikirira.” Kenako iwo adzawona opyozedwa...
“Kodi izi zinachokera kuti?”

Iye anati, “Mnyumba ya Mzanga.”

335 Ndipo iwo adzabuma ndipo iwo adzalira. Ndipo banja
lirilonse, mitundu yawo ya Davide ndi Neftali ndi onse,
adzadzilekanitsa okha, banja lirilonse, ndipo adzazilirira iwoeni
pamene iwo adzamuwona Iye ataima mu mlengalenga, Mmodzi
amene iwo anamupyozza.

336 Kodi uthenga Wake udzakhala chiyani? Penyani chimene
Yosefe ananena. Pamene iye anati... .

337 Penyani chinthu china. Pamene Yosefe anapeza ana ali
pamaso pake, iye anawayang'ana iwo, iye anamuwona Benjamin
wamng'ono. Iye anamuwona Efreimu, iye anawona ena onsewo
pamenepo, Gadi ndi onse a iwo. Ndi mafuko thwelofu, mafuko
teni pamenepo, ataima pamaso pake. Iye anawawona iwo onse
ataima pamenepo. Iye anadziwa kuti iwo anali abale ake. Ndipo
iye anamuyang'ana Benjamin wamng'ono, molunjika, ku mmelo
kwake kunayamba kudzadza. Anadziwa iwo anali ake. Kodi
iye ananena chiyani? “Lolani munthu aliyense andichokere
ine.” Chinachitika ndi chiyani kwa mkazi wake ndi ana? Iwo
anakalowa ku nyumba yachifumu.

338 Kodi Mpingo wa Amitundu udzapita kuti pa Mkwatulo?
Udzakalowa ku Nyumba yachifumu. Mkwatibwi, Aleluya,
Mkwatibwi adzachotsedwa kuchoka pa dziko lapansi, mu
Mkwatulo. Kenako pamene Iye azidzabwerera, Mkwatibwi
Wake sali kumeneko pamene Iye akudzidziwitsa Iyemwini kwa
abale Ake, Ayuda, iwo amene anamupyozza Iye, iwo amene
anamukana Iye.

339 Koma mkazi wake ndi okonedwa ake, azimzake apafupi
pamenepo, ake—abwenzi ake otumizidwa ndi Mulungu anali

nawo mu kachisi. Ndipo pamene iye anayang'ana, iye anati iwo anali. . . Iwo sanadziwe. Iwo anati, "Oh, kalonga wamkulu uyu!" Iwo anayamba kunena, kwa wina ndi mzake, oh, zokhudza zinthu izi za zimene iwo anachita.

³⁴⁰ Ine ndikukhulupirira anali Efreimu, kapena osati Efreimu, koma ine ndaiwala amene iye anali tsopano, amene—amene ananena, "Chabwino, ife sitimayenera kumupha m'bale wathu, Yosefe." Anati, "Inu mwaona, ife tikulipidwa." Rubeni, Rubeni anati, "Ife sitimayenera kumupha m'bale wathu," anati, "chifukwa, inu mwaona, ife tikulipidwa chifukwa cha zimene ife tinachita."

³⁴¹ Ndipo Yosefe ataima pamenepo; iwo samaganiza kuti iye akanatha kumamva Chihebri. Koma iye amachidziwa icho.

³⁴² Ena amaganiza, sangathe kuyankhula. . . kumvetsa kuyankhula ndi malirime, koma Iye amadziwa zonse za izo. Eya, Iye amadziwa. Ufumu wa Amitundu unabwera ndi kuyankhula ndi malirime ndi kutanthauzira, mu mutu wa golide (mutu woyamba) iwo usanagwe. Kodi chinathetsa nyengo yoyamba ya Amitundu ndi chiyani? Zolemba za malirime osadziwika pa khoma, ndipo munthu pamenepo anatha kutanthauzira izo ndi kunena chimene izo zinali. Iwo udzachoka mwanjira yomweyo. Amen. Kulowa mkati ndi kudzatuluka mwanjira yomweyo.

³⁴³ Iwo ankaganiza iye samatha kumva malirime amenewo amene iwo anali kuyankhula, koma iye amadziwa izo. Iwo anati, "Inu mukuona chimene ife tapeza?"

Ndipo Yosefe ndiye anawona kuti iwo akumva chisoni ndi chimene iwo anachita.

³⁴⁴ Tsopano Iye akuwona chisoni chawo ndipo akukhumudwa chifukwa chomukana Iye, chotero Iye akutsamwa ku mmelo Kwake tsopano. Iye wakonzeka kuti abalalitse Mpingo Wake kuchoka pa dziko lapansi, kumutengera Iye kupita ku Ulemelero. Kenako nkudzabwerera, ndipo kenako mafuko onse a padziko adzalira.

³⁴⁵ Kodi iwo anachita chiyani? Rubeni, onse a iwo, anayamba kulira, iwo anati, "Oh! Oh!" Iwo anachita mantha ndipo anati, "Uyu ndi iyeyo. Tsopano ife tikudziwa tapezeka chifukwa cha zijazi. Tsopano iye atipha ife. Tsopano iye. . . Ife tikudziwa kuti ife tiwonogedwa pakali pano, chifukwa ameneyo ndi Yosefe amene wakhala kutali ndi ife kwa nthawi yaitali. Ameneyo ndi Yosefe, m'bale wathu, tsopano ndithudi ife tapezeka chifukwa cha zijazi."

³⁴⁶ Iye anati, "Musati mudzikwiwire inueni. Mulungu anachita izi kuti asunge moyo."

³⁴⁷ Kodi Mulungu anachita chiyani? Nchifukwa chiyani Ayuda anamukana Yesu? Kuti ife Amitundu, chotero, kuti, anthu amene

Iye anawaitana chifukwa cha Dzina Lake, Mulungu anachita izo kuti akasunge moyo wa Mpingo wa Amitundu, Mkwatibwi.

³⁴⁸ Mafuko onse omwe anamukana Iye adzalira. Iwo adzadzibisa okha mmauna, ndi mmiyala, ndi zinthu, adzati, “Atabisala, mugwere pa ife, mapiri.” Iwo anakana Izo, Iye. Achibale onse apa dziko lapansi adzabuma chifukwa cha Iye. Ndipo banja lirilonse mu Israeli mmenemo adzadzilekanitsa okha. Mabanja adzadzilekanitsa, mmodzi kuchoka kwa mzake, ndi kuti, “Nchifukwa chiyani ife tinachita zimenezo? Zinatani kuti ife timukane Iye? Motani? Apo Iye wayima. Ndi ameneyo Mulungu Yemwe ife tamudikirira. Ndipo ndi Uyo apo, ndi zipsyera za misomali mmanja Ake, ndipo ife tinachita izo.”

³⁴⁹ Ndizo ndendende zimene abale amenewo ananena kumusi uko, pamene iwo anadzabwerera ndi kuti, “Ndi ameneyo Yosefe, yemwe ife tinamugulitsa.”

Iye anati, “Ndine Yosefe, m’bale wanu, yemwe inu munamugulitsa ku Igupto.”

³⁵⁰ “Oh!” Iwo anachita mantha. Ndipo iwo anali kulira ndi kubuma, ndipo amathamangira kwa wina ndi mzake, “Kodi ife tichite chiyani?”

³⁵¹ Iye anati, “Musadzikwiyire inueni, chifukwa Mulungu anachita zonse izi. Mulungu ananditumiza ine patsogolo.”

³⁵² Mulungu analenga anthu onse; anthu oyera, anthu akuda, anthu abrawuni, anthu achikasu, munthu aliyense. Mulungu anamulenga munthu aliyense. Iye analenga Amitundu, analenga Myuda. Iye analenga onse. Zonsezo ndi za kwa ulemelero Wake. Ndipo Ayuda ankayenera kuti akanidwe ndi cholinga chakuti adzamtenge Mkwatibwi wa Amitundu.

³⁵³ Ndicho chifukwa cha zoimira zonsezi. Chotero Mkwatibwi wa Amitundu ndi mphukira Zake ndi Iye, Mpingo wa Ulemelero wa Pentekoste uja wotsukidwa mu Magazi a Mwanawankhosa, ndi mphamvu zonse za chiukitsiro zikukhala mwa iwo, adzauka tsikulina mu Mkwatulo (mu kamphindi, mu kuthwanima kwa diso) kupita kukakhala mu Kukhalapo kwa Yesu, pamene Iye azidzabwerera (ndipo adzabalalitsa chirichonse) kuti adzadzidziwitse Yekha kwa abale Ake.

³⁵⁴ Penyani chimene Lemba likunena apa, potseka. Oh!

Taonani, iye akubwera ndi mitambo; ndipo diso lirilonse lidzamuwona iye, (tsopano iye akuyankhula za Kudza kwachiwiri, osati Mkwatulo), ndi iwonso amene anamupyozza iye: . . .

³⁵⁵ mutu wa 7, ndime ya 1 . . . Kapena, ndime ya 7 ya mutu wa 1.

. . . diso lirilonse lidzamuwona iye, ndi iwonso amene anamupyozza iye: ndi abale ake onse a dziko lapansi adzabuma chifukwa cha iye. Ngakhale chomwecho, Amenii.

356 Kenako Iye akupereka chobwereza chachikulu chija. Uyu ndi Ndani? Uyu ndi Ndani amene iwo akupita kuti akamufufuze?

Ndine Alfa ndi Omega, Ndine A mpaka Z, (Chigriki A ndi Z, chilembo cha Chigriki) . . .

357 Machitidwe 2:36, a . . . Petro anati, “Palibe dzina lina laperekedwa pansu pa Kumwamba limene anthu akuyenera kupulumutsidwa nalo.” Kapena, ayi, ine ndikupempha kukhulukidwa kwanu; ndabwereza molakwika zimenezo. Iye anati, “Mulole nyumba yonse ya Israeli idziwe ndithudi, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, yemwe inu munamupachika, ziwiri zonse Ambuye ndi Khristu.”

358 Yohane 14:7 ndi 12, Thomasi anati, “Ambuye, tiwonetsereni ife Atate, ndipo izo zitikwanira.”

359 Anati, “Ine ndakhala ndi iwe nthawi yonseyi, ndipo iwe sukundidziwa ine?” Anati, “Iye amene wandiwona Ine wawawona Atate. Bwanji iwe ukuti, ‘Mundiwonetsere ine Atate?’ Ine ndi Atate Anga ndife Mmodzi.”

360 Ine ndinanena zimenezo nthawi ina kwa munthu. Dona anati, “Miniti yokha, Bambo Branham.” Anati, “Inu ndi akazi anu ndinu mmodzi, aponso.”

Ine ndinati, “Koma osati mwa mtundu umenewo.”

Iye anati, “Ine ndikupempha chikhulukiro chanu.”

Ine ndinati, “Kodi inu mukundiwona ine?”

Iye anati, “Ine ndikutero.”

Ine ndinati, “Inu mukuwawona akazi anga?”

Iye anati, “Ayi.”

361 Ine ndinati, “Ndiye, Izo ndi za mtundu wosiyana. Iye anati, ‘Pamene iwe wandiwona Ine, iwe wawawona Atate.’” Chotero zimenezo zinali zokwanira kwa izo.

362 Chotero mu Yohane Woyera, kapena Yohane Woyamba 5:7 mpaka 8, inu nonse amene mukulemba izo. Yohane Woyamba 5:7 mpaka 8, Baibulo linati. Woyankhula, munthu yemweyo amene analemba Vumbulutsu ili limene Yesu anamupatsa iye, iye anati, “Alipo atatu amene akuchitira umboni Kumwamba: Atate, Mawu (Mawu ndi Mwana) . . . Atate, Mawu, ndi Mzimu Woyera, ndipo atatu awa ndi mmodzi. Ziripo zitatu zimene zimaikira umboni pa dziko lapansi: madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndipo izo zimagwirizana; osati ziri chimodzi, koma izo zimagwirizana mwa chimodzi.”

363 Inu simungathe kukhala ndi Atate popanda kukhala ndi Mwana. Inu simungakhale ndi Atate kapena Mwana popanda kukhala ndi Mzimu Woyera. Kulondola. Koma inu . . . Ndi madzi, Magazi, ndi Mzimu, ndizo zinthu zimene zimatengera kuti mukalowe mu Thupi Lake.

364 Pamene kubadwa kwa thupi kuchitika, chinthu choyamba ndi chiti chimene chimachitika pamene mzimayi akubereka mwana? Chinthu choyamba, ndi madzi. Chinthu chachiwiri, ndi magazi. Kulondola uko? Chinthu chotsatira, ndi mzimu. Mwana amagwira kupuma kwake, amayamba kupuma. Madzi, magazi, ndi mzimu, zimenezo zimapanga kubadwa kwachiregedwe.

365 Ngakhalenso, Kubadwa kwauzimu. Ubatizo wa mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu; kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu. Madzi! Chotsatira nchiyani? Magazi; kuyeretsedwa, kutsuka, kumutulutsa iye panja.

366 Pamenepo ndi pamene inu anthu a Nazarene munalepherera; inu munangopita patali chomwecho ndipo simunapite patali paliponse. Chida chimene chayeretsedwa pa guwa, kukonzekera utumiki, koma osati mu utumiki. “Odala ali iwo,” chiphunzitsa cha pa phiri, “amene akuchita njala ndi ludzu la chirungamo, pakuti iwo adzakhutitsidwa.” Chidacho chayeretsedwa. Ndizo zoon.

367 Ameneyo ali ngati namwali. Mawu akuti *namwali* amatanthauza “wangwiro, woyera, wosadetsedwa, woyeretsedwa.” Asanu anali ndi mafuta, ndipo asanu analibe; asanu anadzadzidwa, ndipo enawo anangokhala mu kuyeretsedwa. “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera *kuyambira* pamene munakhulupirira,” inu Abaptisti, Presbateria?

“Ife sitikudziwa ngati pali Mzimu Woyera uliwonse.”

“Ndiye, inu munabatizidwa chotani?” Uh-huh.

368 Iye atatha kuika manja pa iwo, pamenepo ndiye iwo, atatha kupulumutsidwa ndi kuyeretsedwa, iwo anadzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Kulondola.

369 Madzi, Magazi, Mzimu! Yesu anabwera kudzatsuka ndi kudzayeretsa, ndi kudzawuyeretsa Mpingo, kuti Iye akathe kubwera ndi kudzakhalamo. Ndi Magazi Ake Omwe; Iye anapereka Magazi Ake Omwe wobadwa mwa Mulungu, kuti Iye akakhoze kutiyeretsa ife ku kubadwa kwathu kwa kugonana, ndi kupereka kwa ife chida choyeretsedwa, choyera kuti Iye Mwiniwake akathe kubwera.

370 “Kanthawi pang’ono, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine chifukwa Ine,” mlowammalc waumwini, “ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a chimaliziro.” Ameni. “Njira yonse kumapitirira, Ine ndidzakhala ndi inu ndipo mwa inu. Ntchito zimene Ine ndikuchita inunso mudzazichita. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Mulungu mu Mpingo! Oh, mai! Umulungu! “Alipo atatu amene amachitira umboni Kumwamba: Atate, Mawu (Mwana), Mzimu Woyera. Iwo ali Mmodzi.”

³⁷¹ Tsopano, inu mukhoza kupulumutsidwa popanda kuyeretsedwa. Inu mukhoza kuyeretsedwa ndipo osakhala ndi Mzimu Woyera; kulondola, mzimu woyeretsedwa, popanda kudzadzidwa. Kuyeretsa mtima wako, kuyeretsa mtima wako, popanda kuwudzadza iwo ndi chinachake. Ndizo zimene Iye ananena, “Pamene mzimu woipa watuluka kuchoka mwa munthu, iye amayenda mu malo wowuma. Umabwereranso, umadzapeza nyumba yake yonse itakonzedwa, ndipo amalowamo. Chikhalidwe chomalizira cha munthu ameneyo nthawi zambiri, kasanu ndi kawiri, chimakhala choipa kuposa mmene analiri poyambirira.”

³⁷² Ndi zimene zinachitika ndi inu a Pilgrim Holiness, Nazarene, ndi ena otero. Inu munavomera. Ndipo pamene Mzimu Woyera ubwera, kuyamba kuyankhula ndi malirime, ndi kupereka zizindikiro ndi zodabwitsa, inu munadzitcha izo “mdierekezi” ndipo munachitira mwano ntchito za Mulungu, munadzitcha izo “chinthu chosayera.” Ndipo inu munawona kumene mpingo wanu unapita? Tulukani mwa iye! Ora liri pano, Vumbulutso la Yesu Khristu likuphunzitsidwa, Mulungu kuwululidwa mu mphamvu ya kuwonetsera Kwake kwa Mzimu Woyera. Amen. Tsiku la chiwombolo layandikira.

³⁷³ Tsopano, Umulungu mwa Iye, Timoteo Woyamba 3:16.

. . . Popanda kutsutsana chachikulu ndi chinsinsi cha umulungu: pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi . . . anawonedwa ndi angelo, . . . anakhulupiridwa pa dziko lapansi, analandiridwa mu ulemelero.

³⁷⁴ Oh, basi kumangopitirira ndi kumangopitirira ndi kumangopitirira. Koma ife tiri pati tsopano? Pamapeto a ndime ya 8.

³⁷⁵ Usikuuno ife tiyambira pa—pa ndime ya 9, *Masomphenya Apa Patmo*. Oh, muli zinthu zazikulu zasungidwira kwa ife. Kodi inu mukumkonda Iye?

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

³⁷⁶ Inu mumachitadi zimenezo? Kodi Mulungu wazidziwitsa Yekha kwa inu, wawululidwa kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, Mulungu kuwonetseredwa mu thupi, kukachotsa tchimo? Iye akudziwulula Iyemwini mmasiku otsiriza ano mu mipingo Yake, kudzipangitsa Yekha kudziwika.

³⁷⁷ Tsopano, zinthu zomwezi zimene zikuchitika mu Mpingo, penyani ndipo muwone, pamapeto a Uthenga uwu, kuti ngati Baibulo silinena kuti zinthu izi zidzachitika, ndendende basi. Muwone ngati iwo sanachite ndendende, mu M’badwo wa Efeso, ndi wa Pergamo, Tiyatira, mpaka mmunsi kumapitirira, m’badwo uliwonse.

378 Ananena momwe Lutera akanadzachitira, ndi momwe Wesile akanadzachitira. Ndipo momwe chipembedzo ichi cha Pentenkoste chidzapitire mu Laodikaya, chikhalidwe chofunda, koma, pakati pa zimenezo, Iye akanadzawakoka anthu. Uko nkulondola. Ndizo ndendende. Ife tiri pamapeto. Oh, ndine wokondwa! Ndipo, oh, monga ine ndadziwonera ndekha ndikuswekera, ndi kuwawona azimzanga ndi zinthu, ndi kuliwona dziko ndi chi—ndi chisokonezo chimene ilo lirimo, ndiyeno nkuganiza kuti Kubwera kwa Ambuye kukuyandikira kwambiri. Ife tiri pamapeto a m'badwo.

379 Mitima ya anthu ikulephera ndi mantha. Konsekonse, aliyense, zikumakhala zowopsya pa wailesi, nthawi zonse, “Muzikhala okonzekera nkondo ya mmwamba. Mutengere *ichi* mkati, mutengere *icho* mkati, ndipo mupite pansi kupansi.” Inu mukabisala bwanji kwa izo? Simungakhoze kubisala kwa izo. Chabwino, chinthu chimenecho chidzapita mapazi handiredi ndi fifite mu nthaka, kwa mamailo handiredi ndi fifite, bwalo lake. Bwanji, kusokonezeka kwa icho kudzakhoza... Ngati izo zidzamenye kuno, izo zidzagwedeza Indianapolis mpaka mnthaka. Bwanji, izo zikhoza kudzawombera Indianapolis mzidutswa, kumenya komwe kuno mu Louisville, mwaona, chimodzi cha izo. Nzovuta kunena chimene iwo ali nacho pambali pa icho.

380 Ndipo, taonani, inu simukusowa kuti... Inu mukudziwa, Russia sakusowa kuchita zimenezo. Cuba akhoza kuchita zimenezo. Malo aang'ono aliwonse, a—malo aang'ono kwambiri kukula kwa Alcatraz kutali uko, akhoza kuchita zimenezo, kuphimba dziko lonse. Chinthu chokha chimene inu mukuyenera kuchita ndi kumuika iye pamzere ndi kukoka chingwe chimodzi. Inu simukusowa ankhondo ayi. Inu mukungosowekeka wotentheka mmodzi kuti achite zimenezo, mmanja a mdierekezi. Ndizo ndendende kulondola. Iye akhoza kuchita zimenezo, zikatero ndiye kuti chinthu chonsecho chatha. Izo zonse zatha zikatero.

381 Koma, oh, ndiloreni ine ndikupatseni inu chinthu chodala ichi. Pamene ife tiwona izo zayandikira kwambiri, pamene ife tiwona kuti izo zikhoza kuchitika mmawa usanafike. Kumbukirani, Mpingo udzapita kwawo zimenezo zisanachitike. Mkwatulo udzachitika zisanati.

382 Tsopano, kuti musasokonezedwe, kumbukirani, Yesu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, monga izo zinali mmasiku a Loti.” Kumbukirani, mvula iliyonse isanagwe, Nowa anali mu chombo. Mukuona? Nowa anali mu chombo. Iye ananyamulidwira pamwamba, anadutsa izi. Ndipo tsopano, Nowa anali choimira cha Myuda. Koma Enoki anapita kwawo wopanda kufa. Ndipo pamene Nowa anamuwona Enoki akupita, iye anadziwa inali nthawi, yoyambapo chombo. Uko nkulondola. Icho chinali chizindikiro cha Nowa, pamene Enoki

anapita kwawo. Ndipo mwamsanga Mpingo wa Amitundu ukadzangochotsedwapo, kenako Iye adzadzzipangitsa Iyemwini kudziwika kwa Israeli. Mukuona? Uko nkulondola.

³⁸³ Kumbukirani, mmasiku a Loti, monga Yesu ananenera, kachidutswa kamodzi ka moto kasanakhudze dziko lapansi, Mngelo ameneyo anati, “Changu. Fulumirani. Tulukani kuno, pakuti ine sinditha kalikonse kufikira inu mutachoka kuno.” Moto uliwonse usanakanthe, Loti ndi banja lake anali kunja ndipo atapita. Chotero, Mkwatulo udzabwera Chisautso chisanachitike.

³⁸⁴ Chisautso, anthu ambiri amasokoneza zimenezo. Iye tiziwongola izo, sabata ino, Ambuye akalola, mwa kuthandizidwa ndi Ambuye. Kumbukirani, inu mukuyang’anizana ndi Nthawi ya Chisautso chachikulu, imene inali, ngati inu mungadzifanizitse izo mu Baibulo, amenewo anali masiku a vuto la Yakobo, inu mwaona, pamene iye anavutitsidwa. Zimenezo zinalibe kalikonse kochita ndi Amitundu. Wamitundu alibe kalikonse kochita ndi zimenezo. Mulibemo choimira mu Baibulo kwa icho. Mpingo wa Amitundu Wakwatulidwa.

³⁸⁵ Ndipo inu mukuyembekezera kuti “madzi asanduke magazi,” ndi zinthu ngati zimenezo. Zimenezo zikubwereranso kwa Israeli kenanso, zidzabwereranso ndi Mose ndi Eliya, pamene iwo akubwerera. Eliya, kwa nthawi ya chinayi, akubwereranso mu mzimu. Palibe wa iwo anali atafa, kapena, Mose anafa, iwo sanadziwe kumene iwo anakamuika iye. Iye ankayenera kuti adzaukitsidwe kwinakwake pakati pa nthawiyo ndi apo, chifukwa, pa Phiri la Chiwalitsiro, anali ali pamenepo, akuyankhulana ndi Yesu, sanatero iye? Mukuona?

³⁸⁶ Chotero iwo adzabwereranso ndipo adzaphedwa, ndipo adzagona mu msewu wauzimu wotchedwa “Sodomu,” kumene Ambuye wathu anapachikidwa, Yerusalemu. Iwo adzakhala akulalikira kwa Ayuda, ndipo adzakantha dziko lapansi, ndipo adzatseka mmiyamba, ndi zina zotero monga chomwecho. Ndipo kutha kwa utumiki wa Amitundu kudzapitirira ndi kudzalumikizana ndi zimenezo, ndipo Amitundu adzapita kwawo, ndipo utumiki umenewo udzakhala ukupitirira. Padzakhala chiwonongeko cha zinthu zonse. Magawo awiri a atatu a dziko lapansi adzagwa, ndi china chirichonse. Pamene matupi akufa amenewo anagonekedwa mmisewu, masiku atatu, onani mtundu wanji iwo unali.

³⁸⁷ Tayang’anani pa zithunzi izi zimene ine ndinatenga kuchokera uko ku South America, pamene iwo anamupha wa mishonare wa Pentekoste kumeneko, mkazi wake, atagona mu msewu, ndi iye ndi ana ake awiri aang’ono. Mtsikana wamng’ono, ndi mimba yake yaing’ono itafufuma monga *choncho*. Iwo osakawaika mmanda nkomwe iwo.

Amangodutsapo, nkumawalavulira iwo monga chomwecho, kwa masiku atatu kapena anayi. M'bale Kopp anatenga chithunzi. Ine ndiri nazo izo kunyumba, mwaona, momwe iwo amachitira.

³⁸⁸ Kenako iwo amatumizirana mphatso, kwa wina ndi mzake. Muwone momwe izo zikuimiridwa mu Baibulo, inu muwona mpingo umene udzachite zimenezo. Uko nkulondola, ziri pafupi kuchitika, ndipo zikuyenda kulowa mkati ngati njoka pakali pano, zothyathyalika basi monga izo zingakhali, chizindikiro cha zinthu padakali pano.

³⁸⁹ Tayang'anani pa ulosi Ambuye anandipatsa ine mu '33, momwe izo zikanadzachitikira, "Iwo akanadzaloleza akazi kuti aziponya voti. Mu kuvota, iwo akanadzasankha munthu wolakwika." Zinthu seveni zinaperekedwa, ndipo faivi za izo zachitika kale. Chinthu chotsatira chinali mzimayi wamkulu, mpingo, mphamvu kapena chinachake, chikanadzatenga United States uyu, kuti alamulire. Kenako ine ndinaliwona ilo liri ngati phulusa, litakhala, pamene ilo linafika pamapeto. Iyo inali nthawi ya kumapeto.

³⁹⁰ Iwo anati, "Iwo akanadzakhala ndi makina amene amatha kuyendetsa. Iwo samasowa kukhala wopanda woyendetsa mmenemo." Iwo angoikonzanso kumene iyo. Iwo anati, zaka leveni. . .

³⁹¹ Mzimu Woyera unanena kwa ine. Ndizimenezo izo pa pepala. Inu simungathe. . . Izo sizingakhoze kukanidwa. Ndizimenezo pa pepala, monga Mzimu Woyera unanenera.

³⁹² Zaka eleveni Maginot Line asanamangidwe, Ine ndinati, "Achi German. . . America adzangoti. . . President Roosevelt adzakhala mthakati wa onse a iwo." Ndipo ndiko kulondola. Iye anali.

³⁹³ Osati kukupwetekani kumverera kwanu inu a Democrat, koma ine—ine ndikukuuzani inu. Si wa Democrat kapena wa Republican tsopano. Ndi Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, amene ife tikumukamba. Ine sindiri wa Democrat kapena Republican. Ine ndine Mkhristu. Chotero ndiye, iwo chirichonse chimene icho chinali, koma inu muzindikire pamenezo.

³⁹⁴ Ndipo taonani apa, tsiku lina, ngati inu mukufuna kuwona gulu la chigawanga limene ilo liri. Kutenga makina amenewo ndi kuwakonza iwo, pamene, nthawi iliyonse inu mukavotera Bambo Nixon, inu mumavotera munthu winayu, nthawi yomweyo. Ed- . . . J. Edgar Hoover anakokera makina panja. Ndi angati akhala akuwerenga izo? Bwanji, ndithudi, izo ziriponseponse mmapepala, nyuzi, ndi china chirichonse. Inu mukuona pamene ife tiri?

³⁹⁵ Palibe chirichonse choona mtima panonso koma Khristu. Ameni. Oh, Bukhu lodala lakale limenelo! Ndi zimenezotu. Ndi Limodzi lokhalo limene limakuuzani inu yemwe inu muli, kumene inu munachokera, ndi kumene inu mukupita (Inde,

bwana.), ili ndi Bukhu lakale lodala, oh, ilo limandipangitsa ine kumukonda Iye. Silitero ilo kwa inu?

Chikhulupiriro mwa Atate, chikhulupiriro
mwa Mwana,
Chikhulupiriro mwa Mzimu Woyera, atatuwa
ali Mmodzi;
Ziwanda zidzanjenjemera, ndipo ochimwa
adzawuka;
Chikhulupiriro mwa Yehova chimapangiritsa
chirichonse kugwadera.

³⁹⁶ Ameni. Ndi tsiku lopambana bwanji liri patsogolo pa ife, abwenzi! “Chivumbulutso cha Yesu Khristu chimene Mulungu anapereka kwa mngelo Wake, ndipo anabwera ndipo anadzaziwonetsera izo kwa Yohane, kuti izo zikakhoze kudziwika kudzera mu Mibadwo ya Mpingo, zinthu zimene zasungidwira ife.”

³⁹⁷ Ambuye atidalitse ife tsopano, pamene ife tikuima pa mapazi athu. Ndipo yense amene akuimba limba, tipatseni ife poyambira pang’ono ngati inu mungathe, *Tengani Dzinalo La Yesu Ndi Inu*.

³⁹⁸ Tsopano mvetserani. Pali, wopanda kukaikira, pali alendo pano pakati pathu mu kachisi mmawa uno. Ine ndikufuna inu mugwire manja awo. Ayitanireni iwo, apite kunyumba ndi inu, ndi zochulukira zake. Ndipo mumupange aliyense akhale wolandiridwa. Ine ndikufuna aliyense akhale wotsimikiza kuti akachita zimenezo.

³⁹⁹ Ndipo kumbukirani msonkhano uyamba pa seveni koloko, usikuuno. Ndipo pa hafu pasiti seveni, ine ndidzakhala ndikuyankhula *Masomphenya Apa Patmo*. Mawa usiku, Ambuye akalola, ine ndidzakhala ndikuyankhula pa m’badwo wa mpingo woyamba, Efeso, wa M’badwo wa Mpingo.

⁴⁰⁰ Tsopano ife tiziimba *Tenga Dzina La Yesu Ndi Iwe*, nyimbo yathu yaing’ono ya pakachisi yotulukira. Ndipo tiyeni wina aliyense ayimbe tsopano. Chabwino.

Tenga Dzinalo la Yesu,
Mwana wosaukawe;
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,
Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;
Dzina lofunika, (Dzina Lofunika!) O kukoma
kwakeko!
Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

⁴⁰¹ Tsopano ife tisanaimbe ndime yotsatira, ine ndikufuna Amethodisti, Abaptisti, Apentekoste, Akatolika, Anazarene, Apilgrim Holiness, kwa onse basi mungofikirako, mugwirane chanza ndi winawake kutsogolo kwanu, pa mbali panu, kumbuyo kwanu, nenani, “Mwendamnjira Wachikhristu, mzanga, ndine wokondwa kukhala ndi iwe muno mmawa uno. Wokondwa kuyanjana ndi iwe, pozungulira zinthu za Mulungu. Ine ndikudziwa ife takhala ndi nthawi yopambana. Ndikuyembekezera kudzakuwonaninso inu pano kenanso usikuuno.” Chinachake ngati chimenecho, pamene inu mukugwirana manja ndi anthu, kutsogolo kwanu, kumbuyo kwanu, pozungulira inu.

Pa Dzina la Yesu kuwerama, (Ndikuwonani inu usikuuno, M'bale Neville. Ndikuwonani inu usikuuno.)

. . . mapazi,

Mfumu ya mafumu, Kumwamba, tidzamuveka
Iye korona,

Pamene ulendo wathu watha.

Oh Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;

Dzina lofunika, O kukoma kwakeko!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!

Mpaka tidzakomane pa mapazi a Yesu; (Mpaka
tidzakomane!)

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!

Mulungu akhale nanu mpaka
tidzakomanenso!

Tsopano pamene ife tikuweramitsa mutu wathu:

Mpaka tidzakomane! mpaka tidzakomane!



CHIVUMBULUTSO CHA YESU KHRISTU CHA60-1204M
(The Revelation Of Jesus Christ)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi la Mlungu mmawa, Disembala 4, 1960, ku Branhama Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2022 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org